

KUYESERA KUTI UMUCHITIRE

MULUNGU NTCHITO

POPANDA ICHO KUKHALA

CHIFUNIRO CHA MULUNGU



Abale atumiki, ndi inu abwenzi kunja uko, ine ndikuti ndi chamwayi kukhala pano mmawa uno. Kudziwitsidwa koteroko monga choncho, bwanji, ine sindikudziwa momwe ine ndingadzakwanitsire kufika pamenepo.

² Koma kungokhala pamenepo nkumayankhula, M'bale Nolan, ine sindikukhulupirira ndinayamba ndakumanapo ndi munthu ndendende basi (Ife tonse tinawumbidwa mosiyanasiyana, koma ndi Mulungu yemweyo.) monga M'bale Jack Moore, um-hum, chabwino, iye wakhala ndithudi ali... M'bale Nolan akungoti, "Popeza ine ndakhala ndiri pano ndi iye..." (uyo ndi mpongozi wake wamwamuna), ndi momwe iye anaphunzirira kumukonda iye ndi kulemekeza nzeru zake ndi zinthu. Ndipo izo, ine ndikhoza kunena "ameni" ku zimenezo. Chinthu chabwino kwambiri...nthawi zimene ife takhala nazo limodzi, iye ndi ine, ndi M'bale Brown, M'bale Boutliere pano. Amuna abwino a Mulungu amene ine ndimawakonda kwenikweni iwo ndi mtima wanga wonse.

³ Ndiyeno ine—ine ndikuwona kuti ife tonse sitilinso achichepere, chabwino, ine ndikungoganiza tsopano za nthawi yomwe ikutiyang'ana ife pamene ife tikusintha kuyambira pafupifupi zaka twente zapitazo tikudutsa zipululu, ndi zina zotero limodzi monga amuna achichepere. Koma kungodziwa kuti kuli Dziko komwe ife sitidzakalambako. Ife tidzakakumananso kumeneko tsiku lina.

⁴ Usiku wathawu pamene ine ndimachoka ku kachisi, panali dona wamng'ono atagona kumbuyo uko pa machira, ndipo iye anati, "M'bale Branham, zaka zapitazo..." Ine ndikuganiza kuti iye anali atapuwala. Iye anati, "Inu munandiuza ine..." Ine ndimayiwala chimene chonena cha mkaziyo chinali tsopano, chinachake chonga ichi, Ine ndikuyembekeza kuti sindikubwereza molakwika izo. Anati, "Kuti kusautsika uku kumene ine ndinali nako kukhoza kukhala pa cholinga," kapena chinachake, kuti iye akanadzakhala ndi mwana. Ndipo iye samamvetsa momwe izo zikanadzachitikira ndi iye mu

chikhalidwe chimenecho.

⁵ Apo panadzayima mnyamata wamng'ono, wowoneka bwino, iye anati, "Ndine mwanayo yemwe iye anali naye." Anati, "Ndine mwana yemwe iye anali naye."

⁶ Ndipo zinthu zambiri zachitika mu njira yonse, ife tiribe nkomwe nthawi pano kuti tikambirane za zimenezo. Ife tidzatero ku tsidya linalo.

⁷ Ndipo chaputala ichi cha Amuna Azamalonda, ine sindine wa bungwe lirilonse, ine ndikuganiza monga momwe inu nonse mukudziwira, koma ine... Ili ndi gulu lokhala lomwe ine ndalumikizana nalo, kunyamula khadi lachiyanjano, ndilo... Iwo ndi azipembedzo zosiyanasiyana, ndi anthu amalonda chabe. Iwo akhala chipangizo chopambana kwa ine ndi mtundu wa utumiki umene Ambuye Atate wathu wandipatsa ine. Ndi... sizinali ndendende kuti ine sindimakonda bungwe; ndi utumiki basi umene waperekedwa kwa ine, ndipo ngati ine sindiri womvera ku kuitana kumeneko, ndiye ine ndidzakhala munthu wosakhulupirika kwa Mulungu.

⁸ Ndipo, ine ndikuganiza, ine basi ndisanachoke ku Tucson, mwinamwake ambiri a inu munali kumeneko, tsiku lina ine ndinali, Los Angeles ndikuyankhula kwa chaputalacho. Ndipo uko kunali... Ine ndinangolisalaza bungwelo mwinamwake pang'ono—molimba pang'ono. Ine—ine sindinkatanthawuza kuti ndikhale choncho. Ngati inu mukutanthauza izo kukhala zankhanza, ndiye ine ndikanakhala wachinyengo. Inu simuyenera kuchita zimenezo, ayi, uko ndikungomuphwasula winawake. Koma ine ndinayankhula za mtengo umene ine ndinawuwona mu bwalo la M'bale Sharrit. Iwo unali nazo zipatso za mitundu isanu yosiyana pa iwo. Ndipo ine ndinati, "Ine sindinayambe ndawuwonapo mtengo ngati umenewo mmoyo wanga." Iwo unali a... iwo unali ndi manyumwa, iwo unali ndi mandimu, iwo unali nanchesu, tangelo, malalanje, chirichonse chikumera pa mtengo womwewo. "Chabwino," Ine ndinati, "Ine—Ine ndithudi sindikumvetsa zimenezo. Ndi mtengo wa mtundu wanji umenewo?"

"Ndi mtengo walalanje."

Ndipo ine ndinati, "Chabwino, manyumwa awo?"

Anati, "Eya."

Ine—ine ndinati, "Zikutheka bwanji zimenezo?"

Anati, "Izo zamezanitsidwa."

Ndipo ine ndinati, "Oh, ine ndikuwona."

⁹ Iye anati, "Iwo onse ndi a banja la citrus, ndipo mtengo uliwonse womwe uli wa banja la citrus ukhale... ukhoza kumezanitsidwa."

10 Ine ndinati, “Ine ndamvetsano.” Ndiye ine ndinayamba kufuula pang’ono pokha, inu mukudziwa, chifukwa ndine wamanjenje ndi wotengeka.

11 Kotero, iye anati, “Chavuta ndi chiyani?”

12 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine ndimangoganiza za chinachake.” Ndipo ine ndinati, “Tsopano ine ndikufuna ndikufunsi inu funso.” Ine ndinati, “Tsopano, chaka chamawa maluwa akamadzabwera, sipadzakhala malalanje, tangelo, manyumwa, mandimu; zonsezo zidzakhala malalanje chifukwa izo ziri mu mtengo wa lalanje, sichoncho?”

13 Iye anati, “Ayi, ayi. Ayi, nthambi iliyonse imabala zake zomwe.”

14 Ndinati, “Ine ndawona.”

15 Kotero izo zinkamveka bwino kwenikweni, chifukwa ine...inu mukudziwa ndiri...ndithudi ine ndinalandira digirii kuchokera ku Hartford ndi mayunivesite ena onse awa, inu mukudziwa. Kotero—kotero ndine...ndimayang’ana *chirengedwe*, ndiyo yunivesite yabwino kwambiri yomwe ine ndinapezapo, yunivesite ya Mlengi. Kotero ngati ine ndiyang’ana icho, ine ndimapeza ulaliki wanga kuchokera momwe ine ndimawonera *chirengedwe* chikuchitira.

16 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, izo zikungondipangitsa ine kumverera bwino kwenikweni.”

17 Iye anati, “Chavuta ndi chiyani?”

18 Ine ndinati, “Ine ndinangoganiza za chinachake.”

19 Kotero, tsiku limenero, ine ndinali kulalikira pa zimenezo. Ndipo ine ndinati, “Tsopano, inu mukuwona, pamene mpingo unayamba koyamba, iwo unali...Yesu anati...” Ine ndinali kulalikira Yohane 15. “Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi zake. Ndipo nthambi iliyonse imene simabala zipatso idzadulidwa, nkutenthedwa.”

20 Ndipo wina anangong’amba khosi langa molimba kwenikweni pa chimenecho, anati, “Inu mukuwona, ine ndimaganiza ngati inu munadzazidwa kwenikweni ndi Mzimu Woyera ndi kupulumutsidwa, inu munati, ‘iwo sangathe kuchoka ku zimenezo.’”

21 “Uko nkulondola.”

22 Iye anati, “Nanga bwanji zimenezo?”

23 Ine ndinati, “Tsopano inu mukuyankhula pa phunziro losiyana. Iye akuyankhula za kubala zipatso pamenepo, osati Mpesa; Iye akuyankhula za kubala zipatso, ndipo osati Moyo. Iye anati, ‘Chabwino, ingodulani mtengowo kuti ukule, ubale zipatso.’”

24 Iye anati...

²⁵ Ndipo ine ndinati, “Tsopano, tawonani, mtengo uwu, pamene iwo unayamba, wonse unali weniweni, Akhristu a Baibulo. Ndiye motsatira panadzabwera nthambi yotchedwa Lutera, Methodisti, Baptisti, Presbateria: mandimu ndi zina zotero.” Ndipo ine ndinati, “Inu mukuwona, izo zimachita bwino pa dzina la Chikhristu, koma izo... Izo zikukhala moyo kuchokera ku Mtengo umenewo, koma izo zikubala mtundu wake womwe wachipembedzo. Mukuwona? Koma,” ine ndinati, “ngati mtengo wa lalanje umenewo utulutsa nthambi ina wokha, iwo udzabala malalanje monga iwo unachitira pachiyambi.”

²⁶ Apo zinachitika kuti panali, atakhala pamenepo, mkulu wa opambana... limodzi la mabungwe athu aakulu Achipentekoste. Ine sindikudziwa momwe ndingazipangire zimenezo kotero kuti aliyense amvetse kuti si maganizo anga kuti—kuti ndine—ndine wotsutsana nawo abale amenewo, alongo; zimenezo ndi zolakwika. Ine sindimamvetsetsedwa kwambiri, ndipo ine sindikudziwa chifukwa chiyani. Mukuwona? Anthu amaganiza kuti ine sindimakhulupirira ngakhale kuti anthu azipita kutchalitchi. Ndizo mailosi milioni kutalikirana ndi Choonadi. “Ife tiyenera kudzisonkhanitsa tokha pamodzi, ndipo makamaka pamene ife tikuwona tsikulo likuyandikira.” Mukuwona? Ife tikuyenera kubwera pamodzi mu umodzi. Ife mwina sitingathe...

²⁷ Ngati ine ndikanakhala mu mzinda ndipo iwo analibe kalikonse kumeneko koma a... chabwino, mpingo wina (ine sindikufuna kutchula dzina lirilonse), koma basi mpingo uliwonse, ngati iwo akanangokhulupirira chinthu chimodzi, kuti Yesu anali Waumulungu, zina zonse za izo zinali zolakwika, Ine ndikanapita ku mpingo umenewo. Ngati ine sindingathe kupeza buledi wathunthu, ine—ine ndidzatenga kachidutswa. Mukuwona? Ine ndidzapitako kukamvetsera, kukampembedza Ambuye, ndi kukamusonyeza Iye kuti ine ndikuchita gawo langa. Ine ndikufuna kuti Iye adziwe kuti ndine wamoyo. ndiri—ndiri... ndikufuna aliyense kuti adziwe mbali yomwe ine ndiri. Ine ndimasonkhana ndi Akhristu, ndipo kumeneko kukampembedza ndi—ndi kukamutumikira Ambuye.

²⁸ Koma ndizovuta kwambiri, ine... zinkandivutitsa ine moyipa kwambiri, ndipo kenako ine ndinapeza kuti ngakhale Ambuye wathu sankamvetsetsedwa mu zinthu zambiri. Iye ankatha kunena chirichonse, ndipo iwo ankatero... sankamvetsetsedwa. Ine ndikuganiza izo zikungoyenera kukhala mwanjira imeneyo. Koma iwo amene ali anzeru adzamvetsa. Mwawona? Baibulo linanena chomwecho. Iwo adzachigwira Ichu.

²⁹ Kotero mmawa uno pamene ndimanena izi... Ndipo ine ndinati, “Tsopano, iwo—iwo amakhala moyo kuchokera ku dzina la Chikhristu, koma iwo amabala mtundu wolakwika wa zipatso. Iwo uli ndi chipatso cha chipembedzo. Iwo

anakhazikitsa chinthu, ndipo iwo akukhala moyo kuchokera ku iwo, ndi kumakhala Moyo womwewo.”

³⁰ Ndi zimene ine ndimayesera kuti ndinene usiku wathawu, mzimu umenewo ukhoza kubatizidwira mu Mzimu umenewo ndipo nkusakhalabe Mkhristu. Mwawona? Inu mukukhala moyo kuchokera ku Moyo womwewo, koma zipatso zimene inu mumabala zimanena chimene inu muli. Mwawona? Uko nkulondola. Mukuwona? Iwo akhoza kuchita zizindikiro zonse, ndi kupempherera odwala, ndi kuchiritsa odwala, ndi kutsegula maso, ndi kutulutsa ziwanda, ndi—ndi kuchita zinthu zonse izi, kukhala moyo kuchokera ku Moyo womwewo umene uli mmenemo, koma komabe awo ndi mandimu. Mukuwona? Uko nkulondola. “Zipatso, inu mumadziwika,” Yesu anatero. Ndipo kotero ndiye ife tikupeza . . .

³¹ Ndipo pamene ine ndinatsika pa nsanja, mtsogoleri wamkulu uyu anayimirira, iye anati, “Iye samatanthauza zimenezo.” Iye anati, “Ife tikudziwa kuti ife tonse tamezanitsidwamo.” Chabwino, izo nzoona kuti ife tinamezetsanidwa, chitsa chomezetsanidwa, ndiko kulondola; koma osati mu Mpesa, kumezanitsidwa. Kotero ndiye iye anati . . . anayamba kumakhala ngati—kumakhala ngati kundinyogodola ine mmbuyo pang’ono.

³² Ndipo panali mnyamata wamng’ono pamenepo, ine ndikuganiza ndi anthu ena a katswiri wa pakanema. Dzina lake ndi Danny Henry, ndipo iye anali mnyamata wa Chibaptisti. Chabwino, iye anabwera pa nsanja kuti adzandikumbatire ine, ndipo iye anati, “M’bale Branham, ine ndikuyembekeza kuti izi sizimveka zonyoza, koma,” anati, “Ine ndikukhulupirira uwo ukhoza kukhala pafupifupi mutu wa 23 wa Chivumbulutso.”

³³ Ndipo ine ndinati, “Zikomo inu.”

³⁴ Ndipo iye anayamba kunena chinachakenso ndipo iye anayamba kuyankhula m’malirime, mnyamata wa Chibaptisti. Ndipo pamene iye anatero, panali mka—mkazi wochokera kuno mu Louisiana, iye anali Mfaransa, wokhala ngati mkazi wamkulu wojintcha, iye analemba kumasulirako.

³⁵ Chabwino, ndiye apo panali mnyamata wina atakhala cha kuno anali Mfaransa, iye analemba zomwe iye ananena. Iwo anafanizitsa zolembazo, ndipo izo zonse zinali zofanana.

³⁶ Ndipo kenako mnyamata wamkulu, wamutu woyera atayima kumbuyo uko mmbuyo, ku Clifton’s Cafeteria, anabwera akuyenda. Iye anati, “Ndiloleni ine ndiwoneko zolembazo. Ine ndikufuna kuti ndiwone chomwe izo zinali.”

³⁷ Ndipo onse atatu a iwo anali ofanana mu kumasulira. Iye anali womasulira wa U.N., womasulira wa Chifaransa. Ndipo izo zinanena izi:

Chifukwa iwe wasankha njira yowongoka ndi yopapatiza iyi, njira yovuta, iwe wachita izo mwa kusankha kwako komwe...

Koma ndi chisankho chaulemerero bwanji chimene wachipanga, chifukwa ndi NJIRA YANGA.

Mukuwona? Ndipo anati...ndipo anapitiriza ndipo anati ndiye:

Ichi, mwa ichochokha ndi chomwe chiti chidzachititse, ndi kupangitsa ndi kubweretsa, chidzachititsa, chigonjetso chopambana mu Chikondi Chaumulungu.

³⁸ Inu mukuwona, nthawizonse, ngakhale mu Chifaransa, mnene patsogolo pa muonjezi apo mu—mu—mu kumasulira. Kotero mu zimenezo ine sindikanakhoza kunena...Mose, iye anapanga kusankha kwake, iye anayenera kupanga kusankha kwake. Iye tonse timayenera kupanga kusankha kwathu ndi kuchita zonse zimene ife tingathe. Ndipo Mulungu... Ine ndimalemekeza uthenga wa munthu aliyense umene iye wapatsidwa wokhudza Mulungu. Ine...chirichonse chimene icho chiri, ine ndimachilemekeza icho ndi mtima wanga wonse.

³⁹ Tsopano, ine ndikuwona m'bale wina wamng'ono akubwera kanthawi kapitako, M'bale Stringer, ine ndikuganiza wochokera uko mu Louisiana...kapena Mississippi, anatibweretsera ife zithunzi zina pano zomwe inu mwatiwona ife tikuziwonerera izo. Izo zinali za Mngelo wa Ambuye, pamene Icho chinawonekera. Ndi angati anayimva nkhanayo? Ine ndikuganiza aliyense wa inu pano anayimva iyo. Inu mwakhala nazo izo pa tepi, ndi zina zotero.

⁴⁰ Tsopano, izo zinanenedwa kwa ine mmawa wina pa teni koloko, nditayima mu chipinda changa mu Indiana. Anandiuza ine ndikanati ndidzakhale ku Tucson, kudzakhala molawirira mmawa, Ndikanakakhala ndikutola chisoso (chimene ife timachitcha kumeneko, chamutu wambuzi) pa mwendo wanga wa thalauza. Ndipo Angelo seveni anabwera ndipo anaphulitsa ichi, ndipo nthaka inaphulika ndi china chirichonse, ku... miyala inagudubuzika kuchoka mmapiri, ndipo Angelo seveni anayima pamenepe.

⁴¹ Ndipo ine ndinati, "Chabwino..." Ine ndinamuza mkazi wanga, ndipo iye alipo penapake mmawa uno, "Iwe ukonzekeretse chirichonse chifukwa palibe njira yomwe munthu angapululumukire pa zimenezo," ine ndinati, "ndikutuluka mu zimenezo. Ine ndikupita ku Tucson, ntchito yanga yatha pano pa dziko lapansi. Ine ndikupita Kwathu kuti ndikakhale ndi Ambuye Yesu."

⁴² "Chabwino," iye anati, "iwe ukutsimikiza?"

⁴³ Ine ndinati, "Inde. Eya, palibe amene akanakhoza—akanakhoza kupirira zimenezo. Palibe njira yochitira izo."

44 Ine ndangolalikira kumene *Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo*. Ndiko kumene ine ndinamuyitana wolimba, M'bale wathu Jack Moore wamng'ono kuti ndimufunse iye za izi, Yesu, mu Chivumbulutso 1, atayima pamenepo ndi tsitsi loyera ndi chirichonse.

45 Ine ndinati, "Iye anali Mwamuna wachichepere." Ndipo ndi kumene vumbulutsolo linabwera la munthu ameneyo pokhala atavala wigi, ndipo osati Iye; Iye wavala wigi (ndipo ine sindimakhoza kuzimvetisa izo), monga kukhala Waumulungu Wapamwamba. Ndipo oweruza akale anakakonda kutero mu Israeli, ankayenera kukhala amutu-woyera. Ndipo choyera chimayimira chiyero. Ndipo oweruza a Chingerezi mpaka lero, mmakhoti apamwamba a ku England, amavala wigi yoyera pamene iwo atuluka, chifukwa palibe lamulo lina pamwamba pa lawo pa dziko lapansi. Mukuwona? Ndipo iwo ndi oweruza apamwamba.

46 Ndipo ine ndikukumbukira ine ndinapita uko mu Arizona ndi chirichonse, ine ndimayesera mwakuthekera kwanga kuti . . .Ndinachita mantha mpaka ku imfa. Ine ndinapita ku msonkhano wa ku Phoenix. Ndipo kumbukirani, ine ndinalalikira ulaliki, *Mabwana, Ndi Nthawi Yanji Ino?* Mukukumbukira zimenezo? Ine ndinanena kuti ine ndinaziwona zimenezo, ine ndinati, "Izo zisanafike pochitika, kumbukirani, PAKUTI ATERO AMBUYE, 'Chinachake chichitika.'" Inu mwinamwake muli nawo matepi mu laibulale yanu ya matepi tsopano. Ndipo pamenepo ine ndinati, "Inu mukukumbukira tsopano masomphenya amene samalephera. 'Chinachake chichitika.' Kumbukirani!"

47 Ndipo masiku angapo zitachitika zimenezo, ine ndinayamba kuchita manjenje, ndipo ine ndinaganiza, "Nchiyani ichi? Kodi ine ndifa? Ngati. . .Ine ndikuyembekezera kuti ndizofulumira mwakuti ine ndikhoza kuzivomereza izo. Ine sindikufuna kuchedwachedwa."

48 Ndipo mmawa wina Ambuye anati, "Pita pamwamba pa Sabino Canyon."

49 Ndipo ine ndinali pamwamba apo nditakweza manja anga mmwamba, ndikupemphera. Ine ndinamverera chinachake chinakhudza dzanja langa. Ilo linali lupanga. Tsopano, inu mukhoza kungolingalira momwe inu mungamverere, mutayima pamenepo mwa inunokha ndipo apa pali mpeni mdzanja lanu pafupifupi kutalika *choncho*. Ine ndinawutsitsa ndipo ndinayang'ana pa iwo. Iwo unali mpeni chabe, umodzi wa iyo. . . ndipo ine ndimachita mantha ndi mpeni, mulimonse. Ndipo iwo unali ndi chi—unali ndi chi—chitsulo, chinachake monga umodzi wa mipeni iyi, monga chitsulo cha poto kapena chinachake, chakuthwa kwenikweni ndi chopypayala. Unali ndi chigoba mozungulira iwo *apa*, kumene womenyayo ankagwiritsa ntchito,

kuti asachekane mmanja a wina ndi mzake, ndipo—ndipo ilo linali ndi ngale mu chogwirira apa. Linangokwanira mdzanja langa ndendende. Chabwino, ine ndinasisita nkhope yanga ndi kuyang’ana mmbuyo.

Pompo pa malo omwewo, tsiku lina, ine ndinawona nkunda yaing’ono, yoyera ikutsika. Ndikuuzani za zimenezo nthawi ina.

⁵⁰ Ndipo ine ndinali nditaligwira ilo mu dzanja langa, ine ndinaganiza, “Izo nzachilendo. Tsopano, Ambuye, ine. . .kodi ine ndikutaya malingaliro anga? Kulibe aliyense kuno. Ndiri mamailosi kutali ndi aliyense ndipo apa pali lupanga. Ine ndinali nditakweza dzanja langa mmwamba, ndipo kodi ilo linachokera kuti?” Ndipo ine ndinaganiza, “Ndicho chinthu chachilendo kwambiri. Tsopano penyani apa, ndi lupanga.” Mwawona, ndinaligunda ilo, ndipo ilo linali lupanga. Ndipo ine ndinati, “Palibe aliyense pano amene wayima pano. Ine ndiri pamwamba pa miyala iyi, pomwe pamwamba pa phiri.” Ndipo inu simukanakhoza ngakhale kuwona Tucson kuchokera kumeneko, kunali kutali kwambiri mmusi.

⁵¹ Ine ndinaganiza, “Tsopano, icho ndi chinthu chachilendo. Tsopano, muyenera kukhala mu dera lino penapake, Winawake amene angakhoze kulenga ndi kupanga lupanga ndi kuliyika ilo mu dzanja langa.” Ine ndinati, “Uyo akanakhoza kokha kukhala Mulungu yemweyo amene anamulengera Abrahamu mwanawankhosa, akanakhoza kulenga agologolo amenewo,” zomwe inu mwazimva. Ndipo ine ndinati, “Apa pali chipangizo, mitundu itatu yosiyana ya zipangizo mmenemo, ndipo ine ndikuchigwira icho mu dzanja langa chenicheni basi monga china chirichonse chimene ine ndingakhoze kuchigwira mu dzanja langa.”

⁵² Ndipo ine ndinamva Liwu, linati, “Ndilo Lupanga la Mfumu!”

⁵³ Ndipo ine ndinaganiza, “Tsopano, kodi Ilo linachokera kuti? Panali cha pomwepo mmiyala imeneyo kwinakwake.” Ndipo ine ndinaligwira ilo mu dzanja langa monga *choncho*, ndipo ine ndinati, “Lupanga la mfumu.” Ndipo ine ndinayang’ana pozungulira, ndipo lupanga linali litapita. Ndipo ine ndinati, “Lupanga la mfumu.” Ndiko kuti. . .amamenya ndi—ndi lupanga, ine ndikuganiza ndiko kulondola, ankhondo kapena mwanjira ina, iwo amamenya ndi ilo, inu mukudziwa. Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ndicho chifukwa chimene ilo linali mwina. Izo zikutanthauza kuti mwinamwake ine ndikuyenera kumayika manja pa atumiki, kapena chinachake chonga, icho, kuti ndiwapange iwo atumiki.” Ndiyeno ine. . .

⁵⁴ Liwu linayankhulanso kachiwiri, linati, “Lupanga la Mfumu!” Osati mfumu; Lupanga la Mfumu! Mukuwona?

55 Ine ndinaganiza, “Tsopano, ine mwina ndasokonezeka, malingaliro anga achoka, kapena pali chinachake chikuchitika, pali winawake wayima mozungulira pano ndi ine.”

56 Ndipo abale, zinthu izi ndi zowona. Ine sindi—ine sindikudziwa momwe ndingakuwuzireni inu, inu nthawizonse mwakhala mukuziwona izo zikuchitika mwanjira imeneyo nthawizonse. Ndipo ndi . . . Ine sindinkakhoza kuzimvetisa izo. Kotero . . . Ndiko kumverera kwachilendo kwambiri.

57 Ndipo ine ndinayima pamenepo. Ine ndinaganiza, “Tsopano, aliyenseyo Yemwe ali amene wayankhula kwa ine moyo wanga wonse, kuyambira ndiri wamng’ono, mnyamata wamng’ono, wayima pomwe pano, ndipo ine sindikukhoza kumuwona Iye nkomwe.” Ine ndinati, “Lupanga la Mfumu?” Izo zikanakhala . . . Mulungu *ndiye* Mfumu. “Ndipo lupanga ili ndi chiyani?”

58 “Mawu, Iwo ayikidwa mu dzanja lako.” Anati, “Usati uwope imfa, ndiwo utumiki wako.”

59 Oh, mai! Kutsika kuchokera pa phiri limenero ine ndinapita, ndikulira, ndikufuula, pamwamba pa liwu langa, ndikudumphapamwamba pa miyala. Ine ndinapita uko, ndinamuza mkazi wanga, ine ndinati, “Ine sindifa, wawona, ndi—ndi—ndi utumiki wanga.” (Ine ndinamuza iye kuti akamubweretse Billy Paul kuno, ndi kukawatenga ana. Ine ndinati, “Tsopano, ine ndiribe chirichonse, koma mpingo udzawonetsetsa kuti inu nonse musakhale ndi njala ndi zinthu, ndipo ndidza—ndidzakumana nanu kutsidya linalo.”) Ndipo—ndipo iye . . . Ine ndinati, “Ayi, ine sindifa, ndi chinachake chokhudza utumiki wanga.”

60 Masiku pang’ono zitatha izo ine ndinali kutuluka kuchokera mu msonkhano; ndinali ndi telegalamu ya masamba atatu, inali yochokera kuno ku Houston, Texas. Ndipo munthu ameneyo amene ananditsutsa ine moyipa kwambiri usiku womwe Mngelo wa Ambuye anajambulidwa, chithunzi cha Izo chinajambulidwa uko ku Houston, iye anandiyimbira ine, iye anati . . . anatumiza telegalamu, mkazanga anati, “Ine ndikudziwa, M’bale Branham, ndinu wotanganidwa. Mwana wanga wamwamuna (mnyamata wa mlongo wake wa Ted Kipperman) wakhala mu mzere wa imfa kuti afe mu mpando.” Anati . . . (Nanga bwanji iye akanakhala Billy Paul?) Iye anati, “Iye ndi msungwana wamng’ono akuyenera kuti afe.” Ndipo inu nonse munaziwerenga izo mu pepala, ndithudi. Ndipo anati, “Chiyembekezo chokha chimene ife tiri nacho ndi chakuti inu mubwere ndi kudzachititsa msonkhano ndi kuwasonkhanitsa anthu pamodzi.”

61 Ndipo Raymond Hoekstra anali atandilemba kale ine kangapo, koma inu mukudziwa, ine ndinali nditakonza kuti ukatha msonkhano umenewo ndipite kukasaka ndi Bambo Mc Anally ndi iwo. Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, ngati ine

ndingawasiye ana awo kuti afe ndipo nkusayika kuyesetsa kwanga, ine sindidzathanso kupita kokasaka kenanso.”

⁶² Kotero ine ndinati, “Chabwino, ine ndibwera.” Ine ndinabwera ku Houston, ndinali ndi msonkhano, ndipo ndithudi i . . . iwo sanawaphe konse iwo, iwo basi . . . iwo anawapatsa iwo moyo. Ndipo ndicho chimene iwo ankafuna kuti iwo achite, basi kungowapatsa iwo moyo. Kotero izo ziri pafupifupi zaka twente wani, ine ndikuganiza, mu—mu Texas.

⁶³ Kotero ndiye, ndipo kubwerera mmbuyo, ine ndinapita pamwamba pa phiri ndipo ine ndinapita ndi M’bale Fred Sothmann. Iye ali pano penapake. M’bale Fred, inu muli kuti? Pomwe pano. M’bale Fred Sothmann, M’bale Gene Norman; tsiku lina, tsiku lachiwiri nditakhala pamenepo, Mngelo wa Ambuye anabwera mpaka mu msasa momwe ife tinali, ndi kuyamba kunena za ana awo ndi zinthu zomwe iwo ankachita.

⁶⁴ Ine ndinanyamuka ndipo ndinabwerera paphiri. Ndipo ine ndinali nditapeza kale javelina yanga, ndipo ine ndinkayesera kuyikusira ina mozungulira kwa M’bale Fred. Kotero ine ndinadzapeza pamene izo zinkadyera m’mbali mwa phiri, ndipo ine ndinati, “Chabwino, tsopano, ine ndikuuzani inu chimene ndichite, M’bale Fred.” Ine ndinati, “Tsopano, inu mudzapite uko pa nsonga imeneyo m’bandakucha.” Ife tidzapita kumeneko mmawa, kukakwera pamwamba pa phirilo. “Ndipo tidzapita kumeneko mmawa, ine ndikafika uko kumbali inayo. Tsopano, ine sindidzawombera iliyonse, koma ngati izo zidzathawire mbali iyi, ine ndidzawombera patsogolo pa izo ndi kudzazibwezera izo mmbuyo. Iwe udzasankhepo yayikulu.”

⁶⁵ “Chabwino,” iye anatero.

⁶⁶ Kotero M’bale Fred anapita kumeneko. Ndipo M’bale Gene Norman (ine sindikuganiza kuti M’bale Gene anabwera, iye anatero?), iye anali—iye anali mbali inayo. Ambiri a inu mukumudziwa Gene Norman, bwenzi lapamtima kwa ambiri, m’bale wabwino. Ndipo iye anatsikira pansi pang’ono. Kumene, nkhumba zimenezo, izo basi kunalibeko kumeneko mmawa umenewo. Ndipo ine ndimakhoza kumuwona M’bale Fred, kubaibitsa kwa iye, iye anali pafupifupi mailosi kuchoka kwa ine. Chabwino, ine ndinaganiza, “Kodi izo zingakhale kuti zapita kuti?” Ine ndinatsikira mu chigwa chachikulu, ndipo ndinatsika pansi, ine ndinaganiza, “Ine ndiwona ngati ine ndingapeze komwe izo ziri.” Ndinayamba kubwerera. Iko kunali kutangotsa kumene mmawa, dzuwa linali litangoyamba kutuluka.

⁶⁷ Ine ndinapita mozungulira phompho lalikulu, oh, mai, mapazi mazana ndi mazana, basi miyala yayikulu mu chigwa chachikulu chimenecho uko, makoma aakulu amenewo. Ndipo iko kumangokhala ngati kukufika . . . dzuwa linali likukwera, pafupifupi seveni koloko, ine ndikuganiza, kapena chinachake

chonga icho. Ndipo ine ndinakhala pansi ndipo ine ndinali kuyang'ana pozungulira, ndinapezeka kuti ndinayang'ana pansi pa mwendo wa thalauza langa ndipo apo panali chisoso, cha mutu wa ng'ombe. Ndipo ine ndinati, "Inu mukudziwa, izo zikuwoneka zachilendo. Inu mukudziwa, Mngelo wa Ambuye anandiiza ine kuti ine ndidzakhala pafupifupi mailosi forte kumpoto chakummawa kwa Tucson, Ine ndikanakhala ndikuchotsa chisoso pamiyendo yanga." Inu mukukumbukira izo? Inu mukutero? Inde, bwana. Mwawona? Ine ndinati, "Izo nzachilendo." Ine ndinkachigwira icho.

⁶⁸ Ndipo basi pamene ine ndinayang'ana mmwamba, ine ndinawona pafupifupi nkhumba twente pafupifupi mayadi faivi handiredi kuchokera kwa ine, zinatuluka zikudya mpsyipsya zazing'ono izi ndipo zinagona pansi. Ine ndinati, "Tsopano, ngati ine ndingakhoze kungomutenga M'bale Fred ndi kumufikitsa iye ku malo amenewo uko, iye adzapeza nguluwe yake pomwe apo. Koma ine ndikudziwa iye ali pafupifupi mailosi imodzi kapena awiri kuchokera kwa ine tsopano. Kotero," ine ndinati, "ngati ine ndikanakhoza kuwoloka pa mtumbira wawung'ono uwu popanda izo kundiwona ine, apo pafupi ndi mtengo wawung'ono wa mkungudza uko," ine ndinati, "ngati ine ndingazungulire mbali iyi, pali kanjira ka agwape kakutsetserekerera mbali iyi, ine ndikhoza kuthamangira kumeneko ndi kuchokapo pa njirayo. Ndi kukapachika kachidutswa kakang'ono ka pepala apa kumene ine ndikudziwa kuti ndi chiti cha zala choti nditulukirepo, pa chigwa, ine ndikhoza kumutengera M'bale Fred kumeneko basi mu nthawi."

⁶⁹ Ine ndinaponyera chisoso chaching'ono ichi pansi, kuyiwala za Izo. Ndipo ndinayamba kuwoloka phirilo mophweka kwenikweni ndi kuyang'ana mmbuyo, izo sizinandiwone ine, ndipo ndinathamangira kumusi ndi kukatulukira mnjira ya agwape ija. Ine ndinali nditavala chipewa chachikulu chakuda. Ine ndinayamba kuthamanga kudutsa mu chigwa ichi mofulumira kwenikweni, ndipo izo zinachitika.

⁷⁰ Dziko lonse lapansi linagwedezeka, kulikonse. Miyala yayikulu *chotero* inagubuduzikira pansi, fumbi likuwuluka monga *choncho*. Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo anayima patsogolo panga anayima Angelo seveni; ndendende basi momwe izo zinaliri. Ine ndinamverera ngati ine ndinali kuyimirira mmwamba kuchoka pa nthaka. Poyamba, ine ndimaganza kuti winawake anali atandiwombera ine, inu mukudziwa, nditavala chipewa chakuda chimenecho; ndinkawoneka ngati nguluwe ya javelina, mulimonse, inu mukudziwa izo ndi zakuda. Ine ndinkaganiza kuti winawake anali atandiwombera ine, monga...pafupi pomwe. Ndipo ine—ine ndinawona ndiye chimene icho chinali. Chabwino, mwamsanga pamene...Ine ndinalandira kutumidwa kwanga, mu Lemba, "Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zomwe ziri zinsinsi

zisano ndi ziwiri.” Mukuwona?

⁷¹ Winawake ananena kwa ine, anati, “Tsopano . . .” Oh, iye anati, “Chabwino, tsopano, tsiku lina Ambuye mwinamwake (inu mukuwona masomphenya, M’bale Branham) adzaulula kwa inu chimene zinthu izi ziri, ife tonse tikhoza kuyandikira kwa Mulungu ndi kukhala ndi mphamvu zambiri kuposa zomwe ife timazipeza mu kuyankhula mmalirime ndi zinthu.”

⁷² Ine ndinati, “Izo sizingakhale mwanjira imeneyo.”

⁷³ Chifukwa, onani, ine ndimakhulupirira Mawu kukhala Choonadi. Ndipo Baibulo linati, “Aliyense amene adzawonjezere mawu amodzi kapena kuchotsera Mawu amodzi kwa Iwo.” Izo ziyenera kukhala mu Mawu awa. Mukuwona? Ndi zinsinsi zomwe anthu anazinyalanyaza, pakuti pomwepo ndi pamene panachokera Uthenga wanga wa *Mbewu ya Serpenti* ndi Chikhulupiriro choona cha chitetezero cha wokhulupirira.

⁷⁴ Ine sindikunyozeza abale anga Achipresbateria pamene, ndi ena a inu abale Achibaptisti pa momwe inu mumakhala ndi chitetezero. Ine sindikunena izi kuti ndikhale wosiyana, koma inu simunachite izo molondola. Mukuwona? Ndiko kulondola. Mukuwona? Koma, ine ndinali nditalakwitsa, nanenso. Koma pamene Mngelo ayima kuchokera Kumwamba ndi kukuwuzani inu, ndipo apa izo ziri mu Lemba lomwe, Izo nzoona. Mukuwona? Ndiko kulondola. Mwawona, Iye nthawizonse amayankhula chimodzimodzi ndi Lemba.

⁷⁵ Mmenemo ine ndinayang’ana mpaka mkomberowo unakwera mmwamba, ndikuyamba kusesa mmwamba, ndipo iwo anasanduka ngati kuwala kwachinsinsi, ngati chifunga. Ndendende basi momwe . . . Ndi angati anawona chithunzi cha Icho chimene chinajambulidwa mu Houston? Pafupifupi nonse. Mukuwona? Chabwino, ndi momwe izi zinaliri basi. Icho chinasanduka chinthu chomwecho, Icho chinapitirira kukwera ndi kukwera.

⁷⁶ Ine ndinkathamanga ndi kuthamanga, kuyesera kuti ndimupeze M’bale Fred ndi iwo. Patapita kanthawi, pafupifupi theka la ora kenako, ine ndimakhoza kumuwona iye pansu kutali, akubaibitsa manja ake; ndipo M’bale Gene akubwera, akubaibitsa. Iwo ankadziwa kuti chinachake chinali chitachitika. Ndipo kotero ndiye ine ndinakhala nawo iwo. Ameneyo ndi M’bale Fred wakhala pomwe apo.

⁷⁷ Pamene izo zinkapita mmwamba, ine sindimadziwa kuti zowunikira ndi zinthu, komwe ku Mexico, zinali zikujambula chithunzi chimenecho. *Life* magazine inazitenga izo pamene Izo zinkapita mmwamba. Ndipo ambiri a inu . . . Apa pali *Life* magazine itatenga chithunzi cha Izo. Chinthu chachinsinsi apa, ndipo iwo anati iwo sakudziwa kumene icho chinachokera; ndi mmwamba kwambiri. Ndi pamwamba pa miyamba yonse ndi china chirichonse kuti chikhale . . . Ndi m’mwamba kwambiri

kwa chifunga, chifukwa ndi mailosi sate mmwamba ndi mailosi twente-seveni mulitali izo zitakwera mmwamba chomwecho. Kulibe ngakhale chinyezi kapena kalikonse kumwamba uko, inu mukuwona.

⁷⁸ Ndipo iwo ankaganiza za ndege; kotero iwo anafufuza malo onse, panalibe ndege mmwamba tsiku limenero. Mwawona, iwo ayenera kutero, chifukwa cha kugwedeza mazenera ndi zinthu. “Panalibe ndege mmwamba.” Izi ziri pomwe apa mu magazini, adzakuuzani inu chinthu chomwecho. Ndipo—ndipo icho chinapitirirabe ndi kumapitirira. Ndipo lero mu. . .

⁷⁹ Izi ziri mu magazini ya *Science*, kumene, iwo sangathe kumvetsa. Iwo sakudziwa chomwe Icho chiri.

⁸⁰ Tucson, ku yunivesite, mzanga wa ine anapita uko tsiku lina ndipo anali kuyankhula kwa iwo za izo. Anati, “Ife sitikutha kumvetsa chimene. . .”

⁸¹ Ine ndinati, “Musati munene kanthu, sizingachite ubwino ayi. ‘Musati muponyere ngale zanu patsogolo pa nkumba.’” Mukuwona? Ndi zakwa Mpingo, kwa Osankhidwa, oyitanidwira kunjawo. Mukuwona?

⁸² Ndipo aliyense ankabwera, akuti, “M’bale Branham, ine ndikuwona chithunzi chanu apa. Ine ndikuwona *izi*. Ine. . .” Inu mukudziwa momwe izo ziliri. Koma uko—kusesa kwakutali uko monga m’bale uyu ali nako pano pamene iko. . . Mundikhululukire ine. Umu ndi momwe Izo chinayambira, kusesa. Kwenikweni *izi* zinali kudzanja lamanja. Ndipo inu nonse mukukumbukira ine ndinati, “Mngelo wodziwikayo ndi amene anayankhula kwa ine, anali kudzanja lamanja,” ngakhale izo zisanachitike. Inu mukukumbukira? Mapiko ake analoza mmbuyo monga *choncho*. Ndizo ndendende mapiko a Mngelo uja pamene iye ankapita mmwamba. Mwawona, monga izo. . . Kotero iwo anayamba kujambula zithunzizo chifukwa izo zinali zosamvetsetseka. Koma pamene chithunzi chotsiriza, pamene Icho chinadzipanga Chokha m’mlengalenga ndi zina zotero, ichi ndi icho monga *Look* apa inachitengera icho. Inu mukuwona momwe izo zikukwerera mmwamba basi pamene iwo akuyamba kuziwona izo, inu mukuwona. Ndipo apo pakubwera cha—chachikulu chenicheni ndi chithunzi chotsiriza, pamene icho chinapangidwa.

⁸³ Iwo sakudziwa kumene icho chinachokera kapena kumene icho chinapita, iwo sakudziwa panobe. Sayansi yadodometsedwa nazo kwathunthu, siyikudziwa zomwe zinachitika. Koma ife tikudziwa: “Padzakhala zizindikiro kumwamba kuthambo.” Ife tikuzidziwa izo. Mukuwona? Ndipo Iye analonjeza zinthu *izi*. Mukuwona? Ndipo chinthu chokhacho chimene ichi chinaloledwa kuti chitengedwe. . .

⁸⁴ Tsopano, ine ndikudziwa ndife anthu a kwathu kuno mmawa uno. Ngati ine ndingakusangalatseni abale inu kapena

alongo monga m'dziwa-zonse, chonde ndikhululukireni ine. Ine sindikutanthauza kuti ndikhale choncho. Ine ndiima... ndakhala pano mmawa uno ndikuyankhula pamaso pa amuna omwe ali masikolala, amuna omwe ali anzeru; Ine—ndine wosaphunzira, sindimatha ngakhale kutchula Malemba anga molondola. Ine ndiri ndi mutu woti ndiwerenge mmawa uno, ndine... ndinali woti ndifunse mmodzi wa abale pano kuti andiwerengere ine iwo, chifukwa ine sindingathe ngakhale kutchula mayina omwe ali mmenemo, Mbiri Yoyamba 13, (ngati inu mungathe, M'bale Jack, inu mukhoza kumayisaka iyo), kwa phunziro langa. Ine—ine sindingathe ngakhale kutchula mayina amenewo, ine ndikumusiya iye kuti achite izo, chifukwa iye akhoza kuwatchula iwo.

⁸⁵ Ndipo ine ndikudziwa kuti ndikuyankhula ndi amuna anzeru. Koma, abale, zinthu izi zachitidwa kuti inu musayang'ane pa umbuli wanga, koma khulupirirani kuti ine ndikukuuzani inu Choonadi. Ndi Mulungu akukuuzani inu Choonadi. Ndicho Choonadi. Mukuwona?

⁸⁶ Tsopano, ndipo pamene ine ndiyankhula za zipembedzo, Ine sindikutanthauza kwa kuti inu mukhale wankhanza kwambiri ndipo... Ayi, ine sindikutanthauza kuti inu musamapite ku tchalitchi chanu. Pitani ku mpingo kwanu, nzomwe mukuyenera kuchita. Koma musati mujowine nawo mabungwe amenewo, chifukwa tsiku lina ine ndidzakhala ndikukuuzani inu ndi kutsimikizira izo mwa Lemba, icho ndi chilemba cha chirombo. Ndipo inu mungokumbukira, ndicho chilemba.

⁸⁷ Ine ndikulalikira... Ine sindikanati ndilalikire izo mu mpingo wa M'bale Jack, iye akanakhoza kundiuza ine, "Pitirizani ndi kuchita izo"; koma ine ndikupita ku kachisi, iwo udzakhala wotalika maora foro. Ndipo mutu wanga ndi, "Chirombo pa chiyambi ndi chirombo pa mapeto, kudutsa mu njira ya serpenti." Mukuwona? Zitenga pafupifupi maora foro. Ine ndiri nawo Malemba anga onse atayalidwa. Chirombo kuyambira pachiyambi, iye anali chirombo mmunda wa Edeni, iye ndi chirombo pa mapeto, ndi kusonyeza kuti iye ndi munthu wachipembedzo ndipo chipembedzo (chimene chinapanga chipembedzo); ndi kubwera kudutsa mu njira ya izo, ndi kutsimikizira izo kwa inu mwa Malemba kuti izo ziri. Ine sindinkadziwa izo mpaka Mzimu Woyera utapereka izo kwa ine tsiku lina kumtunda uko.

⁸⁸ Tsopano, mu izi, ine ndinali kuyang'ana izi tsiku lina, nditayima, ndipo Chinachake chinanena kwa ine... ndikuyang'ana pa icho, ndipo ine ndinaganiza... M'bale Hickerson, mmodzi wa matrastii anga... kapena madikoni ku tchalitchi ku Jeffersonville... Ngati ine sindikhulupirira mu kupita kutchalitchi, nchifukwa chiyani ine ndiri ndi tchalitchi? Ife tinali nawo iwo onse kudutsa m'dzikoli, titalumikizitsana

usiku wina, mailosi thuu handiredi aliwonse a mabwalo anali ndi imodzi ya matchalitchi anga.

⁸⁹ Tsopano, ichi—chithunzi ichi, ine ndinali nditaima, ndikuyang’ana pa icho, ndi Chinachake...Ine ndinali kuyimirira mchipinda changa. Chinachake chinati, “Tembenezira icho kumanja.” Ine ndinamvetsera.

⁹⁰ Ine ndikudziwa izo zikumveka ngati winawake yemwe wasokonezeka pang’ono malingaliro, koma, inu mukuwona, monga ine ndinanena usiku wina, zinthu zazikulu zonsezi ndi zasukulu kwambiri...Tsopano, ine sindikutsutsana nazo izo. Kumbukirani, ife tiyenera kutumiza ana anu ku sukulu ndi kukapeza maphunziro ndi zina zotero, koma ine ndikuuuzani inu tsopano, izo sizidzawachitira ubwino mu dziko limene liri mkudza, chifukwa icho chidzakhala chitukuko china, chopambana kwambiri kuposa ichi. Chitukuko chimenecho sichidzakhala nayo nkomwe iliyonse...Sichidzakhala ndi masukulu aliwonse mmenemo, sichidzakhala ndi imfa iliyonse mwa icho, simudzakhala tchimo lirilonse mmenemo. Ichi chiri ndi zonse izo; ziribe kanthu kuti ife tikhala otukuka chotani, imfa yochuluka imawonjezeredwa nthawi zonse. Mukuwona? Chimenecho chidzakhala chopanda imfa. Koma tsopano ife timayenera kukhala nayo sukulu, ife timayenera kuvala zovala, ife...

⁹¹ Ine ndimati ndiyankhule mmawa uno pa *Edeni wa Satana* (ambiri a inu muli nayo tepi yake), *Edeni wa Satana*. Iye wapanga munda wina wa Edeni, ndipo zaka sikisi sauzande zinamutengera iye kuti amupange iye, monga momwe Mulungu anachitira ndi Wake pachiyambi. Mulungu anapanga Edeni Wake, ndipo Satana anamuyipitsa iye. Tsopano Satana wapanga Edeni wakewake, ndipo Mulungu adzamuwononga iye (uko nkulondola) ndi kuyikapo WakeWake.

Chinachake chinati kwa ine, “Tembenezira icho kumanja.”

Ine ndinaganiza, “Ine ndikuganiza ine ndikuyang’ana pa icho molondola.”

Chinati, “Tembenezira icho *kumanja*.” Mukuwona?

⁹² Ine ndinaganiza, “Mwinamwake Liwu limenero limatanthauza kutembenezira icho *kupita* kumanja.” Ndipo pamene ine ndinatero, inu mukuwona chimene icho chiri: *Mutu wa Khristu* wa Hofmann, pa sate-firii. Apa, yang’anani mkati umu, onani ndevu Zake zakuda, nkhope Yake, maso Ake, mphuno Yake, ndi china chirichonse. Mukuwona gawo mu tsitsi Lake apa likutulukirapo. Ndipo Iye wavekedwa ndi wigi ya Mngelo yoyera imeneyo kuti asonyeze kuti Uthenga wa Iye kukhala Mulungu ndi Choonadi. Iye ndiye Woweruza Wamkulu wa chilengedwe chonse, Woweruza Wamkulu wa Kumwamba ndi dziko lapansi. Iye ndi Mulungu, ndipo sichina chakenso koma Mulungu. Iye ndi Mulungu

wofotokozedwa mmawonekedwe a munthu wotchedwa Mwana wa Mulungu, yemwe Mwana anali Munthu. Ndipo ngati izo sizikupanga Uthenga wathu kukhala wolondola ndendende: kuzindikiritsidwa ndi Lemba, kuzindikiritsidwa mu utumiki, kuzindikiritsidwa ndi Kukhalapo Kwake, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Chotero Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izo ziri Choonadi, abale. Mutha kusagwirizana nazo izo, koma ingokhalani pansu ndi kuziwerenga izo ndi mtima wanu wotseguka nthawi ina, ingololani Mzimu Woyera ukutsogolereni inu kuchokera . . .

⁹³ Apa, pamene M'bale Jack . . . Ine ndinamuyimbira iye ndisanalalikire izi ndipo ndinayankhula naye nthawi ina za “Kodi wigi yoyera imeneyi inali chiyani?”

⁹⁴ Iye anati, “Chabwino, M'bale Branham, Ine ndikulengeza iyo kuti zinali mu Chake . . . pambuyo pa chiukitsiro Chake mu thupi Lake laulemerero.” Ine ndinkayankhula kwa M'bale Jack. Ndipo pali . . . Ine sindikudziwa aliyense padziko lapansi yemwe ndingadalire za ziphunzitso zawo zafiyoloje ndi zinthu monga ine ndikanafunira M'bale Jack Moore ndi M'bale Vayle, ndi amuna oterowo—monga choncho, afiyoloje enieni amene awerenga mitundu yonse ya mabuku ndi ngodya zosiyanasiyana kuchokera ku chirichonse. Chabwino, koma, inu mukuwona, ngakhale ndi zimenezo, ndi mzanga wa pamtima, Ine—ine—ine sindinathe basi kuchilandira icho, panali chinachake pamenepo chomwe sichikanachilandira icho.

⁹⁵ Ndiyeno pamene izo zibwera, izi, ndiye ine ndikuwona chomwe izo ziri. Apa pali ndevu Zake zakuda. Inu mukuziwona Izo, ine ndikuganiza. Mukuwona? Ndevu zake zakuda ndi tsitsi lakuda, maso Ake, mphuno, chirichonse, mwangwirowo basi, ndipo ngakhale gawo mu tsitsi Lake likubwera cha mbali iyi. Iye ndi Mulungu! Mwawona? Ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo iyi ndi magazini ya *Look* . . . kapena magazini ya *Life*. Ine ndikuganiza kuti izi ndiye . . . Ine ndayiwala kuti ndi nkhani yanji tsopano; oh, Meyi pa seventini, 1963. Ndi pamene icho chinatulukira, ngati aliyense akufuna magaziniyo. Ndi chithunzi chomwecho chomwe chiri ndi Rockefeller ndi wake—mkazi wake kumbuyo kwake kwa icho. Ndipo iyi ndi magazini yatsopano ya *Science* kuti “chikadali chinsinsibe.”

⁹⁶ Kodi ine ndinanena zinthu izi chifukwa chiyani? Kutu izo zikhoze kukupatsani inu mawonedwe pang'ono a zinthu zomwe ife tikuyesera kunena, kutu Mulungu akuzindikiritsaponse pawiri kumwamba ndi padziko lapansi kukhala zolondola. Kuzindikira zamumtima uku, masomphenya, ife tiri nazo zotsanzira zambiri, ife nthawizonse. Koma kumbukirani, pasanati pakhale dola yabodza, payenera kukhala dola yeniyeni poyamba; choyamba chiyenera kukhala dola yeniyeni, ndiyeno iwo amapangidwa kuchokera ku imeneyo. Basi monga ife

tinali naye Mose weniweni ndi Aroni weniweni, ndiye ife tinali nawo a Yambre ndi a Yane pambuyo pawo. Mukuwona momwe izo zonse zimabwerera? Iwo amachiwona icho ndipo kenako amayesera kuchitsanzira icho, pamene zoonza zake pali *chimodzi* chapachiyambi. Ndiko kulondola. Osati kunena zimenezo kuti ndipweteke kapena kunyozetsa, kapena kuika chinachake molakwika, koma kwa Choonadi chokha; kuti ndidziwe kuti ine . . .

⁹⁷ Ine ndikuyamba kukhala munthu wokalamba, ndipo ine ndikudziwa kuti nthawi yanga si yotalika kwambiri. Ngati Yesu, achedwa, ine ndikhoza. . . ndikhoza kukhala kwa kanthawi pang'ono; koma ine ndikudziwa kuti tsiku lina mtima uwu udzapanga kugunda kwake komaliza, ndipo ine ndikulowa mu chipinda chachikulu, chamdima kumeneko chotchedwa imfa. Koma pamene iyo ibwera, ine sindikufuna chirichonse choti ndidzayang'ane mmbuyo, kuti ndiyesere kuchilapa. Ine ndikufuna, pamene ine ndidzafika ku nthawi imeneyo, kuti ndidzakhale woyera ndi wangwiro mwa chisomo cha Mulungu. Ine ndikufuna kudzikulunga ndekha mu miinjiro ya chilungamo Chake, pamene ine ndidzalowa mmenemo, ndi chinthu chimodzi ichi mmalingaliro anga: Ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake; ndipo pamene Iye adzayitana, Ine ndidzatuluka pakati pa akufa ndi kukakhala ndi Iye kwanthawizonse. Ndipo ndicho cholinga changa pano tsopano kuti ndiyesere kumutenga munthu aliyense. . . osati kuti ndisinthe ma fiyoloje anu kapena kalikonse, koma kuti ndikulitse chikhulupiriro chanu mu lonjezo la Mulungu la tsiku lino.

Tsopano tiyeni ife tipemphere:

⁹⁸ Wokonedwa Mulungu, ndife anthu othokoza mmawa uno, koma komabe, Ambuye, ife tikukhala mu dziko lamdima limene. . . Palibe mmodzi wa ife pano mmawa uno, Atate, koma amene tikumverera kuti ife—ife tikufuna kuyenda pafupi ndi Inu, ife tikufuna iko—kukhudza kwa Inu mmiyoyo yathu komwe kungathe kutifewetsa ife ndi kutipanga ife ofewa kotero kuti Inu mukhoze kutisintha ife pa nthawi iliyonse, kutiwumba ife kuti tikhale ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Icho—ndicho cholinga chathu pano, Atate, ndicho—ndicho cholinga changa chokhacho chomwe ine ndiri nacho ndi kuyesera kuti—kuti ndikhale moyo pamaso Panu ndi kuwatenga Mawu Anu ndi kuwayankhula Iwo mobwezera kwa amuna ndi akazi amene. . . osati kuti ndikhale munthu wosiyana koma kuyesera kulemekeza Iye amene wandipatsa ine Moyo. Perekani izo, Ambuye.

⁹⁹ Mulole pasakhale munthu pano lero. . . Kapena—kapena ngati. . . Ife talumikizitsidwa mmawa uno, kudutsa fukoli kenanso. Mulole pasakhale munthu yemwe ali mu liwu la mawu athu kupita konse mu chipinda chachikulu icho asakukudziwani

Inu mu mphamvu ya chiwukitsiro Chanu. Ngati pangakhale ochimwa ena kwinakwake kudutsa mdzikoli, amene. . . kapena mu chimango chino, nyumba yoyankhuliramo yayikulu iyi, atakhala pano mmawa uno. Ngati alipo amene sakukudziwani Inu, mulole lero likhale tsiku limene chikumbuntima chawo chiti chigwedezedwe, chidzutsidwe, ndipo iwo azindikira kuti iwo sakudziwa miniti yomwe ife tingayitanidwe kapena kulamulidwa kuti tidzayankhe chifukwa cha miyoyo yathu, uko Kumwamba. Ndipo ngati dzina lathu likadali pa bukhu la kawundula ilo, ife tidzakhala owonongedwa; koma ngati liri mu Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa, Moyo weniweniwo, ndiye ife tapulumutsidwa.

¹⁰⁰ Ndipo mulole, Ambuye, pamene Moyo umenewo ukuyenda kuchokera ku tsamba kupita mu mungu, kupita mu mankhusu, kenako ku njere, pamene ife tikudutsa mmawa uno ngati pangakhale Moyo wina umene ukupita mu njere yomwe yagona mu phesi limenero, utulutseni iwo lero, Ambuye, mulole iwo utsatire kusuntha kwa njereyo, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁰¹ Pepani kuti ndatenga nthawi yochuluka. Ine ndinayiwala za izi ngakhale kukhala nthawi ya wailesi kunja uko, nthawi ya pafoni.

¹⁰² Tsopano tiyeni ife titembenukire ku kuwerenga kwathu. Ndipo M'bale Jack, kodi inu muli nalo Baibulo lanu pamenepo? Pamene ine ndikupeza Lemba langa, ine ndimufunsa M'bale Jack kuti awerenge Lemba ili chifukwa ine sindingathe kutchula mayina awa. Chabwino. Ziri mu Mbiri Yoyamba 13. [M'bale Jack Moore akuti, "Mutu wonse?"—Mkonzi.] Uh-huh.

[Ndipo Davide anafunsira kwa akapitawo a zikwi ndi mazana, ndipo ndi mtsogoleri aliyense.]

[Ndipo Davide anati kwa khamu lonse la Israeli, Ngati icho chikukomerani inu, ndi kuti chiri cha AMBUYE Mulungu wathu, tiyeni titumize kwa abale athu kulikonse, amene atsala m'dziko lonse la Israeli, ndipo ndi iwo nawonso kwa ansembe ndi Alevi okhala mmizinda yawo ndi mmidzi, kuti iwo adzisonkhanitse okha kwa ife:]

[Ndipo tiyeni tibweretse Likasa la Mulungu wathu kwa ife: pakuti ife—ife sitinafunsire kwa ilo m'masiku a Sauli.]

[Ndipo khamu lonse linati iwo adzachita chomwecho: pakuti chinthucho chinali choyenera pamaso pa anthu onse.]

[Kotero Davide anasonkhanitsa a Israeli onse pamodzi, kuyambira ku Sihori wa ku Igupto kufikira polowera ku Hamati, kuti akatenge likasa la Mulungu kuchokera ku Kiriyati-yearimu.]

[Ndipo Davide anakwera, ndi a Israeli onse, ku Baala, kumene kuli, ku Kiriyati-yearimu yemwe anali wa Yuda, kuti abwere nalo likasa la Mulungu AMBUYE, amene amakhala pakati pa akerubi, amene dzina lake limatchulidwa pa ilo.]

[Ndipo iwo ananyamula likasa la Mulungu mu ngolo yatsopano kuchokera mnyumba ya Abinadabu: ndipo Uza ndi Ahiyo anayendetsa— anayendetsa ngoloyo.]

[Ndipo Davide ndi a Israeli onse anasewera pamaso pa Mulungu ndi mphamvu zawo zonse, ndipo ndi kuyimba, ndipo ndi azeze, ndi zisakasa, ndi malingaka, ndi zinganga, ndi malipenga.]

[Ndipo pamene iwo anafika pa bwalo lopunthira la Kidoni, Uza anatambasula dzanja lake kuti agwire likasa; pakuti ng'ombe zinapunthwa.]

[Ndipo mkwiyo wa AMBUYE unayakira momutsutsa Uza, ndipo iye anamkantha iye, ndipo chifukwa chakuti iye anaika dzanja lake pa likasa: ndipo pomwepo iye anafa pamaso pa Ambuye.]

[Ndipo Davide anaipidwa, chifukwa AMBUYE anali atapanga cholakwa pa Uza: chifukwa chake malowo anatchedwa Perezi-uzi mpaka lero.]

[Ndipo Davide anawopa Mulungu tsiku limenero, nati, Ndidzatengera bwanji likasa la Mulungu kunyumba kwa ine?]

[Kotero Davide sanabweretse likasa kunyumba kwake ku mzinda wa Davide, koma analinyamula ilo mmbali mnyumba ya Obedi-edomu Mgiti.]

[Ndipo likasa la Mulungu linakhalabe ndi banja la Obedi—Obedi-edomu mnyumba miyezi itatu. Ndipo AMBUYE anadalitsa nyumba ya Obedi-edomu, ndi zonse zimene iye anali nazo.]

¹⁰³ Zikomo inu, M'bale Moore, chifukwa chondiwerengera ine Lemba. Tsopano, pepani ine sindikanakhoza kuwerenga zimenezo inemwini, koma ine—ine sindikanakhoza kuchita izo.

¹⁰⁴ Tsopano ine ndikufuna kuti inu mutembenezire ndi ine ku Marko 7:7, ndipo ife tiwerenga ndime zoyamba zisanu ndi ziwiri za Marko Woyera mutu wa 7.

Pamenepo anasonkhana kwa iye Afarisi, ndi ena mwa alembi, amene anabwera kuchokera ku Yerusalemu.

Ndipo pamene iye anawona ena a ophunzira ake akudya mkate ali odetsedwa, ndiko kunena kuti, osasamba mmanja, iwo anawapezera cholakwika.

Koma Afarisi, ndi Ayuda onse, pokhapokha iwo atasamba mmanja mwawo... kawirikawiri samadya, akugwira—akugwira miyambo ya akulu.

Ndipo pamene iwo anabwera kuchokera ku msika, pokhapokha iwo atasamba, iwo samadya. Ndipo zinthu zina zambiri zinali—anali iwo... zimene iwo analandira kuchokera kwa a... analandira kuti azizigwiritsitsa... kutsuka kwa zikho, ndi kwa miphika, ndi zotengera zamkuwa, ndi za magome.

Pamenepo Afarisi ndi alembi anamfunsa iye, Chifukwa chiyani ophunzira anu samayenda monga mwa mwambo wa akulu, koma amadya mkate ndi mmanja mosasamba?

Iye anayankha ndipo anati kwa iwo, Chabwino kodi Yesaya analosera za inu onyenga, monga kwalembedwa, Anthu awa andilemekeza ine ndi milomo yawo, koma mtima wawo uli kutali ndi ine.

Komabe pachabe iwo amandipembedza ine, kuphunzitsa ngati chiphunzitso malamulo a anthu.

Tiyeni ife tipemphere.

¹⁰⁵ Wokonedwa Mulungu, lemekezani Mawu Anu tsopano, ndipo mulole Iwo akwaniritse chimene Iwo alingaliridwira. Tigwiritseni ife ntchito ngati zida zoyankhulira Iwo, ndi makutu athu kuti amve kuchokera kwa Inu, ndi mitima yathu kuti iwalandire Iwo. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu, kwa ulemerero wa Mulungu. Amen.

¹⁰⁶ Tsopano, phunziro langa kwa mphindi pang'ono ndi ili... Ine...

¹⁰⁷ Ife tiri pa kulumikiza pa telefoni kwa fuko lonse mmawa uno. Ndipo ine ndamva kuti mzanga wabwino, Roy Borders, akumvetsera kuno, ndinatopa kwambiri usiku wathawu. Ine ndimayiwala kuti ife tinali pa wailesi... kapena kulumikizana uku usiku wathawu. Roy, kulikonse kumene iwe uli, ngati iwe uli uko ku San Jose mu tchalitchi kumeneko, kapena mwina uko ku tchalitchi cha M'bale McHughes, kapena kulikonse komwe iwe uli, usati uwope, m'bale wanga, chirichonse chikhala bwino. Ukhazikike, iwe basi... Iye achipanga icho kudziwika kwa ine, Roy; usati udandaule, mwana, khala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

¹⁰⁸ Mutu wanga mmawa uno ndi: *Kuyesera Kutu Umuchitire Mulungu Ntchito Popanda Icho Kukhala Chifuniro Cha Mulungu*. Tsopano, ilo ndi phunziro lachilendo, ndipo ine ndikudalira kuti Ambuye awulula izi kwa ife tsopano. Kumbukirani, "Kuyesera kutu umuchitire Mulungu ntchito popanda icho kukhala chifuniro cha Mulungu." Tsopano,

izo zikuwoneka zachilendo kwambiri. Koma, mu zimenezi, mwinamwake Mulungu akhoza kutithandiza ife.

¹⁰⁹ Chinthu china chimene ine ndikufuna kuti ndinene mmawa uno, kuti ndife okondwa kukhala naye pakati pathu bwenzi langa, mzanga wokondedwa kwambiri, mnyamata wachichepere. Ambiri a inu anthu pa wailesi tsopano mukhoza, kapena, pa kulumikizana kwa patelefoni, mukumudziwa yemwe uyu ali. Lero ndi tsiku lake lobadwa, usinkhu wa zaka naintefirii, M'bale Bill Dauch wakhala kuno patsogolo panga, usinkhu wa zaka naintefirii.

¹¹⁰ Zaka zingapo zapitazo adokotala anati, "Iye sangakhoze kukhala moyo." Ine ndangozindikira iye atakhala pano tsopano. Pansi pa hema wa okosijeni, ndipo mkazi wake wokondedwa anandiyimbira ine ndipo anati, "M'bale Branham, ngati inu mukuyembekezera kumuwona bwenzi lanu lakale, Bill, ali moyo, inu kulibwino mubwere pompano."

¹¹¹ Ndipo ine...Limodzi la matayala anga linadulidwa m'mbali, gudumu langa linali litaphwasuka, ndipo ndinang'amba tayala la galimoto yanga ndikuyesera kuti ndikafike kwa iye. Ine ndinali ndikungochokera ku a—a—malo, malo omwetsera mafuta, ndipo ndikubwera kuchokera ku malo opumulira kumene ine ndinali nditayima mu Ohio ndikuyesera kuti ndikafike kwa iye, ndipo ndikuyenda kunja ine ndinawona masomphenya. Ndipo apo panayima M'bale Dauch, atayima mu tchalitchi atatambasula dzanja lake panja; izo zinasintha, ndipo ine ndikukuwonani inu mukubwera chotsika mu msewu ndi kudzandigwira dzanja langa. Anati, "Pita ukamuwuze iye, 'PAKUTI ATERO AMBUYE.'"

¹¹² Iye anali pafupifupi zaka nainte panthawiyo. Iye anali ndi vuto la mtima ndi kutsekeka kwa mtima, ndi kulephera kwathunthu kwa mtima. Dokotala wochenjera kwambiri. Mwamunayo siali...iye samafuna...Ayi, ine sindinena zimenezo. Iye ndi munthu basi amene angakhoze kukwanitsa kupeza dokotala aliyense amene iye angamufune. Iye anali ndi dokotala wabwino Wachiyuda amene anakumana nane mu holo ndipo anati, "Palibe mwayi kwa iye kuti angakhale moyo."

¹¹³ Ndipo ine ndinalowa mkati ndipo ndinalowetsa dzanja langa pansu pa hema wa okosijeni, ine ndinati, "Bill, iwe ukukhoza kundimva ine?" Iye anagwedeza mutu wake. Ine ndinati, "PAKUTI ATERO AMBUYE, 'Iwe siufa tsopano.'"

¹¹⁴ Sabata kuchokera pamenepo, pamene ine ndinakafika pa guwa kuti ndilalikire Uthenga wanga, apa panabwera M'bale Dauch akuyenda kudutsa mchchipindamo. Ndipo pamene ine ndinapita ku Furr's Restaurant, kuwoloka... Ine ndikutanthauza Blue Boar, kuwoloka mu Louisville, apa iye anali akutuluka mu galimoto, akubwera chotsika mu msewu, atatulutsa dzanja lake panja; ndendende basi molingana ndi

Mawu a Ambuye. Ndipo ndizo zaka zitatu kapena zinayi zapitazo; ndipo apa iye wakhala njira yonse kumusi kuno, mu Shreveport (amadutsa fukoli, osati pa ndege tsopano, pa galimoto), uh-huh, wakhala pano mmawa uno. “Tsiku lobadwa labwino, M’bale Dauch.” Ndiko kuchokera ku fuko lonseli, kuchokera kulikonse. “Mulungu akudalitseni inu!”

¹¹⁵ Ine ndinamubatiza iye, pambuyo pokhala wa Utatu, ine ndinamubatiza iye pamene iye. . . unali umodzi wa misonkhano yanga yoyambirira, pamene M’bale Banks Wood anachita kumulola iye kuvala zovala zake (iye ndi mwamuna wamulingo wabwino, monga inu mukuwonera), ndipo iye analowa mu dziwe ndipo ine ndinamubatiza iye ali pafupifupi usinkhu wa zaka eyite-faivi kapena nainte, mu Dzina la Ambuye Yesu. Iye anati sankakhoza konse kumverera bwino mpaka iye atapeza chitetezero chimenecho cha chinachake. Kenako iye anadzalandira tsiku lobadwa kumene iye sadzakalamba konse. Ndiko kulondola, Dziko lalikululu limenero. Iye mpaka akuyembekezera kuti akhala moyo kuti adzawone Kudza kwa Ambuye; izo zikhoza kuchitika. Koma ngati iye ati agone, iye. . . ndipo ife nkudzakhala kuti tiri maso pa nthawi imeneyo, iye adzabwera poyamba. Kulondola. Koteru, M’bale Dauch, palibe njira tsopano yoti muziphonyere izo. Muli pamzere ndendende. Khalani pamenepo, m’bale wanga, ndipo Mulungu akudalitseni inu. Ndipo ine ndikumuthokoza Ambuye chifukwa cha mwamuna wabwino monga ameneyo, ndi chifukwa chomupatsa iye zaka zonsezi.

¹¹⁶ Mu Buku la Mbiri, “Kuyesera kuti umuchitire Mulungu ntchito popanda icho kukhala chifuniro Chake.” Mulungu ndi wochita mwayekha, choyamba, ife tikufuna kuti tizimvetsetse zimenezo. Anthu lero akudabwa chifukwa chimene ife sitikukhala ndi chitsitsimutso. Kodi inu mumakhulupirira kuti Mulungu ndi wochita mwayekha? Mwawona, Baibulo limayankhula mwanjira iyi.

¹¹⁷ Ndipo ife timayesera. . . Pamene ine ndinali kukambirana ndi gulu la abale anga abwino, abale Achibaptisti, osati kale kwambiri, ndipo iwo anati, “M’bale Branham, ife tikhoza kokha kukhala ndi chitsitsimutso pamene ife titenga Mawu, mawu ndi mawu, tsamba ndi tsamba, chilembo ndi chilembo.”

¹¹⁸ Ndipo ine ndinati, “Ine ndikukhulupirira inenso, tsamba ndi tsamba.” Iye anatero. . . Ine ndinati, “Iwo akhala akuyesetsa kuchita zimenezo nthawi zonsezi.”

¹¹⁹ Iye anati, “Koma ife tikuyenera kupeza kutanthauzira kwa Chigriki kwa Mawu, chimene Chigriki chimanena.”

¹²⁰ Ine ndinati, “Ine sindinawerenge mochulukwa kwambiri, koma kuwerenga mbiriyakale ya mpingo, ndi *Bungwe la Nicaea*, ndi *Pre-Nicaea Council*, ndi *Nicaea Fathers*, ndi ena otero, iwo anali kutsutsana kumbuyo uko za Chigriki. Ndizo zaka

thuu sauzande zapitazo. Mmodzi anati, ‘Izo zikutanthauza *ichi*,’ ndipo wina akuti, ‘Izo zikutanthauza *ichi*. Mawu achigiriki amatanthauza *ichi*.’”

¹²¹ Basi monga chinenero chathu; mawu oti *see*. Gwiritsani ntchito mawu oti *see*, inu mukhoza kutanthauza “madzi ambiri,” “Ine ndikumvetsetsa,” kapena zinthu zambiri. *Bored*, akhoza kukhala, “anabowola bowo, kupanga kuyenda,” kapena—kapena “iwe wanditopetsa ine,” kapena “iwe unandilipirira borodi langa,” kapena iwo akhoza kutanthauza chirichonse . . . zinthu zambiri. Ndipo mavawelo aang’ono amenewo, ndi zina zotero, zimangosintha tanthauzo lonselo. Kotero inu simudzachita izo monga choncho. Mulungu anzilemba Izo monga choncho, chifukwa . . .

¹²² Ndipo Mawu onse ndi odzozedwa, ndipo Iye ananena kuti, “Ine ndikukuthokozani Inu, Atate, Inu mwazibisa zinthu izi pamaso pa anzeru ndi aluntha, ndipo mudzaziwulula” (ameni) “kwa makanda omwe angaphunzire.” Ndi vumbulutso la Iye, monga ine ndinanena usiku watha, “Adzawulula Izo kwa makanda.”

¹²³ Ine ndinati, “Izo sizigwira ntchito, bwana.” Ine ndinati “Chitsitsimutso sichidzabwera mpaka Mulungu, Mulungu wochita mwayekha, atachitumiza icho; ndiyeno Iye akhoza kutenga mbuli yaying’ono yomwe siingakhoze ngakhale kulemba dzina lake, ndi kuchita zimenezo ndi ilo, amene sadziwa ngakhale Chingerezi chabwino ngakhale Chigiriki.”

¹²⁴ Ndicho chimene Iye anachita mu nthawi imene Petro analalikira pa Pentekoste, inu mukudziwa, iye sankatha ngakhale kulemba dzina lake, mbuli ndi wosaphunzira. Koma Mulungu amachita zinthu mwanjira yachilendo chotero ku kuganiza kwathu kwaluntha. Izo zimamupanga kukhala Mulungu. Ngati Iye akanakhala ndi gulu la azamulungu ndi olemekeseka, ndi ena otero, iwo akanati, “Kayafa wanzero uja, inu mukuwona, iye ananena izo molondola basi.” Koma Mulungu anapita kumeneko ndipo anakatenga asodzi amene sankakhoza ngakhale kulemba dzina lawo, ndipo ndicho chimene Iye anatenga. Ameneyo ndi Mulungu, Iye amatenga chinachake chimene sikanthu ndi kupanga chinachake kuchokera mwa icho kwa ulemu Wake Womwe. Iye anatenga chisokonezo ndipo anapanga Edeni. Uh-huh, ndi Mulungu.

¹²⁵ Tsopano, ngati pali aliyense amene ali ndi zimango za chitsitsimutso, ndi m’bale wathu wolemekeseka, Billy Graham. Koma zimangozo ziri bwino, koma zimangozo sizingasunthe icho, izo zimatengera mphamvu kuti zisunthe icho. Inu mutha kupanga galimoto, kuyikamo mipando yabwino mmenemo, kupanga mapistoni abwino ndi—ndi kutsimikizira mwa sayansi zimene iyo ingakhoze kuchita; koma pokhapokha mphamvu

zikhale pamenepo, iyo yangokhala chidutswa chakufa cha katundu.

¹²⁶ Koteru, mu chitsitsimutso cha Welsh, chimodzi mwa zitsitsimutso zathu zomaliza Chipentekoste chisanafike, palibe amene ankadziwa chomwe chinayambitsa chitsitsimutsocho, gulu la anthu chabe.

¹²⁷ Tsopano, pamene ife tiwatenga onse . . . bwenzi lathu, Billy Graham, tikawatenga onse a Presbateria, ndi Achilutera, ndi Achipentekoste, ndi chirichonse pamodzi, kulowa mu mzindawo ndipo kumeneko nkukakhala ndi msonkhano waukulu wa masauzande, ndipo sarte sauzande nkubwera (mmasabata awiri) ndi kudzapereka mitima yawo kwa Khristu; kudzabwerera masabata ena awiri ndipo inu simudzapezako aliyense. Mwawona, zimenezo ndizo zimangozo. Koma mumulole Mulungu mu chisomo Chake choyima pachokha angoyankhula kwa mbuli ina yaying'ono, monga kunena kuti, wamng'ono wopandapake; mulole Mzimu Wake ugwere mu mzinda ndipo amuna sangakhoze kupita ku ntchito, akazi sangakhoze kutsuka mbale, mdzakazi sangakhoze kuyala pabedi, akufuula ndi kulira manja awo ali mmwamba mu mlengalenga. Chimenecho ndicho chitsitsimutso, ndicho mu chifuniro cha Mulungu.

¹²⁸ Izo zinanenedwapo kuti anthu ena olemkezeka ochokera ku mpingo anapita ku Wales kuti akamvetsetse, kapena kulingalira zomwe zimango zonse zinali mu chitsitsimutsocho, mu nthawi ya chitsitsimutso cha Welsh. Ndipo pamene iwo anatsika mu chombo atavala zipewa zawo zazitali, ndi kolala yawo yozungulira, powona, akubwera chotsika mu msewu, wapolisi wamng'ono, akugwedeza chibonga chake mozungulira ndi kuzungulira monga *choncho*, akuyimba muluzu, iwo anati, “Munthu wanga wabwino, kodi inu mungandiuzeko komwe kuli chitsitsimutso cha Welsh?”

¹²⁹ Iye anati, “Inde, abale anga, inu mwayima pakati pa icho!” Uh-huh, uh-huh, uh-huh. Iye anati, “Inu mukumvetsa, *ine* ndine chitsitsimutso cha Welsh,” anati, “chifukwa chitsitsimutso cha Welsh chiri mwa ine.”

¹³⁰ Ndiko kuchita mwayekha! Ndicho chimene Mulungu amachita, ndipo Iye yekha amakhala ndi ufulu wotumiza chitsitsimutso. Osati kusunghanitsa zimango palimodzi, ndi kupemphera kuti Mulungu atumize mphamvu—mphamvu.

¹³¹ Iye amangowululira Mawu Ake mwa okonzedweratu. Tsopano, pamene ine ndigwiritsa ntchito mawu oti *kukonzedweratu* . . . Tsopano, iwo ndi mawu oyipa kuti mugwiritse ntchito pagulu, makamaka pamene ife tiri ndi magulu osakanizikana pakati pa Achiarminia ndi Achicalvin. Ndipo osati a . . . Ine ndakufunsani inu kuti musaganize kuti ine ndikudziwa izo zonse, koma iwo onse akulakwitsa molingana

ndi Lemba. Chisomo ndi chimene Mulungu anandichitira ine, ntchito ndi zimene ine ndimamuchitira Iye. Mukuona? Zikatero inu mwachipeza Icho. Ngati inu mukwera pa imodzi ya nthambizo, inu ndithudi mudzazipeza nokha kumapeto kwa nthambiyo ndipo simudzatha kubwereranso. Bukhu la Aefeso limazikokera izo pamodzi, ine ndikuganiza.

¹³² Tsopano, koma mawuwo, pamene ine ndiwagwiritsa ntchito iwo, *okonzedweratu*, musaganize kuti ndine...ndiwo mawu okhawo amene ine ndikuwadziwa ku—kupanga...Ndi kudziwiratu kwa Mulungu, mwawona, kuti Iye anadziwa. Iye—Iye sanganene...Iye—Iye anafa kuti onse apulumutsidwe, Iye anatero, koma mwa kudziwiratu Kwake Iye anamudziwa amene akanadzatero ndi amene sakanadzatero. Mukuona? Ndi zimene Iye amadziwa, ine sindikusidziwa izo ndipo inu simukuzidziwa izo, kotero ife timachigwirira ntchito chipulumutso chathu chomwe ndi mantha ndi monjenjemera.

¹³³ Tsopano, koma Mulungu amawakonzeratu Mawu Ake, ndipo wakhala akutero mmibadwo yonse. Kudziwiratu Kwake kwamupangitsa Iye kuti akhale mu mpingo, ngakhale mwa anthu, zinthu zina zimene Iye anazichita kuchokera pachiyambi. Ndiyeno Uthenga umene ukulalikidwa kwa m'badwo *umenuw* umangowululidwa kwa anthu enaake, ena onse a iwo samawuwona Iwo. Mukuwona? “Zikomo Inu, Atate, Inu munazibisira zinthu izi ku maso a anzeru ndi aluntha, ndi kuziwulula Izo kwa makanda omwe angakhoze kuphunzira.” Mwaona, ndiko kukonzedweratu. Osati kuti Iye anachita zimenezo mwa, inu mukuti, “Ine ndikusankha *iwe*, ndipo sindikusankha *iwe*.” Mwa kudziwiratu Kwake, Iye anadziwa chimene inu mukanati mudzachite.

¹³⁴ Mwa Iye pokhala wopandamalire...Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ndi wopandamalire? Ngati Iye siali, Iye sangathe kukhala Mulungu. Ndiye, inu mukuganiza, pokhala wopandamalire: Iye ankadziwa utitiri uliwonse umene ukanati udzakhale pa dziko lapansi, ndi kangati kamene utitiri umenewo udzaphethire maso ake, ndi phula lochuluka bwanji lomwe linali mu utitiri uliwonse, tsamba lililonse la udzu lomwe iwo ukanati udzakhalepo; ndiko kupandamalireko. Ndipo ife tiri ndi malire, ife timapunthwa mu mdima. Mulungu anatifanizitsa ife ndi nkhusa, ndipo ife tiyenera kukhala ndi Mtsogoleri. Ndipo Mtsogoleri ameneyo si munthu, Mtsogoleri ameneyo ndi Mzimu Woyera, Mzimu wa Khristu pakati pathu. “Kanthawi pang’ono ndipo dziko lapansi silindiwonanso Ine.” Umunthu Wake wathupi unakwezedwa kupita pa Mpandowachifumu wa Mulungu, kumene Mzimu *unali* pa Mpandowachifumu; tsopano Khristu ali pa Mpandowachifumu, Yesu. “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silindiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu kufikira chimaliziro cha dziko lapansi, ngakhale mwa inu.” Mpandowachifumu wa Mulungu,

wa Khristu, wayikidwa mu mtima mwanu; ndipo Iye akukhala pa Mpandowachifumu wa Mulungu, koma mu Zakachikwi Iye akukhala pa Mpandowachifumu Wake Womwe; chimene, Iye analumbirira kuti Iye adzamudzutsa Munthu uyu, Mwana Wake, Mwana wa Davide, kuti adzakhale pa Mpandowachifumu Wake.

¹³⁵ Tsopano, Iye amawulula zinthu izi mwa kudziwiratu Kwake kwa iwo amene Iye anawadzoderatu ku zinthu izi, apo ayi iwo samaziwona Izo. Kuyima pomwepo, nkumayang'ana kumene pa Izo, ndipo osakhoza kuziwona Izo.

¹³⁶ Ndi angati anayamba achiwonapo chithunzi chija cha ng'ombe mthengo, kuti iwe umangoyenera kuyang'ana ndi kuyang'ana? Kodi inu munayamba mwachiwonapo icho? Kapena munachiwonapo chithunzi cha Khristu mu chitsamba, kapena mu mlengalenga, kapena mmitambo? Mwaona, wojambula uja anachikonza icho chomwecho mwabwino mpaka iwe umayenera kuyang'ana pa icho mwanjira inayake basi. Chabwino, ndiye, iwe ukangochiwona icho kamodzi, iwe sungakhoze kuwona chinanso koma chimenecho. Nthawi iliyonse iwe ukayang'ana, pamene icho chiri. Ndi angati anaziwona zithunzi zimenezo? Chabwino, zedi inu munatero.

¹³⁷ Chabwino, umo ndi momwe Khristu amakhalira, Iyemwini, Uthengawo, Uthenga umakhalira. Iwe ukangowuwona kamodzi Uthenga wa ora, palibe china chirichonse chimene iwe ungachiwone koma Iwo. Ndizo zonse. China chirichonse chapita, zina zonse zimangokhala zolowetsapo, mwawona, mwawona, pamene iwe ungowuwona Uthenga kamodzi!

¹³⁸ Ndizo—zinalipo mu nthawi ya Nowa. Pamene Nowa ndi gulu lake . . . onani momwe . . . Pamene iwo anawuwona Uthenga, panalibe chimene chinali ndi ntchito. Pamene gulu la Mose linawuwona Iwo, panalibe chimene chinali ndi ntchito. Pamene gulu la Yohane linawuwona Iwo, panalibe chimene chinali ndi ntchito. Pamene gulu la Yesu linawuwona Iwo, panalibe chimene chinali ndi ntchito. Pamene gulu la Luther linawuwona Iwo, gulu la Wesley linawuwona Iwo, gulu la Chipentekoste linawuwona Iwo, panalibe chimene chinali ndi ntchito, iwo anachokako kwa chirichonsecho. Bwanji? Mwa kudziwiratu Kwake Iye anakonzeratu zinthu izi kuti zidzachitika.

¹³⁹ Iye amamusankha munthu Wake Yemwe mwa kudziwiratu Kwake. Monga Iye ananena mu Aroma 8 apa, kuti Esau . . . kuti kuti—kuti kusankha kwa Mulungu kukhale kotsimikizika. Kutu Esau ndi Yakobo onse obadwa mwa makolo oyera, mapasa, kuti kusankha Kwake kukhale kotsimikizika ndi koono, Iye anati, “Ine ndamuda Esau, ndipo ndamukonda Yakobo,” aliyense wa anyamatawo asanabadwe. Mukuona? Iye amadziwa

zomwe ziri mwa munthu, Iye anazidziwa izo kuchokera pachiyambi chomwe izo zinali, chotero Iye akhoza kupangitsa chirichonse kugwira ntchito ndendende basi pa nthawi ya koloko. Ife timakhala tonse amanjenje ndi okhumudwa; inu simunamuwonepo konse Iye atakhumudwa. Iwo samatero... Mwaona? Chirichonse chikugwira ntchito bwino, ndendende basi, kolokoyo ikugunda.

¹⁴⁰ Zinthu izi zimene zikuyenera kuti zidzachitike, akazi onse awa okhala ndi tsitsi lalifupi, ndi amuna awa ovala zawo... monga okhala ndi tsitsi ngati akazi awo. Ine ndikuwawona iwo, mwamtheradi, ali ndi zopiringizira izi mu tsitsi lawo, zipiringiza ilo apa mtsogolo. Ndi kupotoza bwanji! Ndizo zotsatira za Edeni wa Satana. Ndipo chimodzimodzi monga mkaziyo: iye akuyesetsa kuti azidula tsitsi lake monga mwamuna wake; mwamuna wake akumalola tsitsi lake kumakula monga mkazi wake. Ndipo iye akumavala zovala za mwamunayo, ndipo iye akumuvalira mkaziyo zovala zake zamkati. Mwaona, ndi zimenezotu. Iye akukhala wachimuna, ndipo iye akukhala wachikazi. Mwaona, ndi Edeni wa Satana, wosiyana ndi yemwe Mulungu anamupanga iye pachiyambi. Ndicho Choonadi.

¹⁴¹ Ngati ine sindiyamba, ife sitilowa mu zimenezi. Koma zinthu izi, ndi njira yoti Iye achitire izo, ndi yemwe ati adzachite izo, ndizo njira Yake Yomwe yosankhidwa, Iye amasankha. Umo ndi momwe Iye amafunira kuti izo zizichitidwira.

¹⁴² Monga ndinamumvera M'bale Pearry Green, m'busa wathu ku Tucson, akulalikira usiku wina za momwe Mulungu anapangira zinthu mwanjira ina (ndayiwala kuti mutu wake unali chiyani.), koma iye anati, "Umo ndi momwe Mulungu amazikondera izo, umo ndi momwe Mulungu amachitira izo." Chabwino, izo nzoona.

¹⁴³ Tsopano, ndi ndani pakati pathu amene angamuwuze Iye kuti Iye akulakwitsa? Ndani angayerekeze kuyimirira pamaso pa Mulungu, ndi kunena, "Inu mukulakwitsa, Ambuye, Inu muzichite izo momwe ine ndikufunira kuti zichitidwire, momwe Dr. *Wakuti-ndi-wakuti* ananenera kuti izo zidzichitidwira"? Ndi ndani uyo yemwe wapita patali chomwecho mu kaganizidwe kawo, kuti anganene chinthu chonga chimenecho? Ayi, inu simungatulukire poyera ndi kudzanena zimenezo, koma mumaganizira zimenezo!

¹⁴⁴ Monga pa Uthenga wanga wa *Wotsutsakhristu*, "Padzawuka akhristu abodza." Tsopano, Iye sanati *a Yesu* abodza. Mwawona, palibe akanati ayime nji kuti azitchedwa "Yesu," mmatchulidwe a Ambuye. Koma *a khristu* abodza amatanthauza "odzozedwa."

¹⁴⁵ Oh, iwo, mmodzi aliyense amaganiza kuti ali ndi kudzoza, "Ulemerero kwa Mulungu, iye akhoza kuchita *ichi* ndi kuchita

icho!” Koma muyikeni iye pa mayeso a Mawu ndipo mupeze kuti atulukira pati, mwaona, Uthenga wa ora.

¹⁴⁶ Iwo anali nako kudzoza mu nthawi ya Yesu, koma osati pa Iye.

¹⁴⁷ Iwo anali nako kudzoza mu nthawi. . . Ngakhale Datani anali nako kudzoza mu nthawi ya Mose. Iye anati, “Tsopano, iwe usaganize kuti ndiwe woyera yekhayo pakati pathu, Mulungu ali nawo ochuluka. Ife tingoyambitsa bungwe pano, gulu la amuna.”

¹⁴⁸ Mulungu anati kwa Mose, “Dzipatule wekha kwa iye,” ndipo Iye anatsegula nthaka ndi kuwameza iwo. Iye anali atapereka Mawu Ake apachiyambi kwa Mose, mneneri Wake; ndiyo njira yokhayo yomwe Iye anayamba wachitirapo konse izo, ndipo njira yokhayo yomwe Iye ati adzachitire konse izo. Iye samasintha dongosolo Lake, mwawona.

¹⁴⁹ Kotero malingaliro athu ndi olakwika, malingaliro Ake ndi olondola, nthawizonse. Ndipo musati muyesere kumuuzza Iye kuti Iye ndi “wolakwa.” Ziribe kanthu yemwe ife tikuganiza kuti ali woyenera bwino, izo siziri kwa ife kuti tizinena yemwe ali woyenera bwino. Tsopano, apo ndi pamene inu mumafika mu bungwe.

¹⁵⁰ M’bale wina wamng’ono wodzazidwa ndi Mzimu amalowa mu mzinda ndipo amapanga bu- . . . kupanga a—gulu labwino la anthu. Ndipo pa msonkhanowo iwo amakumana, ndipo abale onse oyera amagwirizana, inu mukudziwa, ndi kuti, “Inu mukudziwa chiyani? Ine ndikukhulupirira *Jones* wamng’ono kuno,” (iye wangokhala wamng’ono kwambiri pakati pawo) “Ine ndikuganiza iye amayenera kukhala ndi kachisi wamkulu wabwino uyo, ine ndikuganiza. Kodi inu simukuganiza kuti ndi zolondola?” Ayi, mai. Apo iye akupita. Ndipo kenako gululo limamwazikana. Mukuwona? Amawalekanitsa awa! Mulungu amachita kulekanitsako, Iye ndi Yemwe amachichita iko. Koma iwo onse, mmodzi aliyense, amafuna kuti amutenge wamng’ono *uyu*, nkukamuyika iye cha *apa*, ndi *uyu* pansu *apa*. Kumeneko ndi kuganiza kwa munthu.

¹⁵¹ Munthu amakhala nawo mafungulo, koma Mulungu ndi yemwe amawasunga kwenikweni mafungulowo. Iwo anawapatsa ophunzira, mpingo woyera, mafungulo; ndipo penyani nthawi yoyamba yomwe iwo anawagwiritsa ntchito iwo, pamene Yudasi anagwa chifukwa cha kulakwitsa. Iwo anabwera pamodzi ndipo anachita mayere; ndi abale oyera. Ndani anganene kuti iwo sanali abale oyera? Ndani angati iwo sanali oyera? Koma iwo anachita mayere, ndipo iwo anagwera pa Matiyasi. Ndipo pamene iye. . . Kodi iye anayamba wachitapo chiyani? Palibe. Koma Paulo anali mmodzi wosankhidwayo! Ameni. Uko kunali kusankha kwa Mulungu: Myuda wamng’ono, wamphuno yangowe, wamwano, waukali. Osati a Matiyasi, ma D.D., inu mukudziwa, iye—iye anali. . . Ndi Paulo. Mulungu

anamusankha Paulo; mpingo unasankha, unasankha Matiyasi. Mwawona? Inu mulibe ufulu womuza Mulungu kuti Iye ndi “wolakwa.” Iye amadziwa choti achite, Iye amadziwa chimene munthuyo anapangidwa nacho.

¹⁵² Ndani angatero konse . . . Mpingo umenewo unamusankhapo Paulo? O, ayi, ayi. Anati, “Munthu ameneyo ndi amene akutiyika ife tonse mu ndende.”

¹⁵³ Koma Mulungu anati, “Ine ndidzamuwonetsa iye momwe adzavutikire chifukwa cha Ine.” Iye akudziwa chiyani.

¹⁵⁴ Chabwino, ziribe kanthu yemwe ife timaganiza kuti ali wolondola, Mulungu amadziwa yemwe ali woyenera bwino chifukwa Iye amadziwa mtima wa munthu, Iye amadziwa.

¹⁵⁵ Ngakhalenso chitsitsimutso, kapena zinthu izi, sizichitika pa nthawi yomwe ife tikuganiza kuti izo ziyenera kuchitika. Ife timaganiza, “Ndi nthawi ino pakali pano, ulemerero kwa Mulungu!” Ine ndikuzindikira mmachaputala athu ndi zina zotero za Amuna Amalonda, “Kukubwera nthawi yomweyo, aleluya, chitsitsimutso chachikulu!”

¹⁵⁶ Musati munyengedwe, “Iye wabwera kale, ndipo iwo anamchitira iye zomwe iwo anafuna.” Mwawona? Koma iwo amaganiza kuti pali chitsitsimutso. Kodi icho chikuchitika? Ayi! Ichu chachitika, ndipo chafa, chatha. U-nhu. Zindikirani, ino ndi nthawi yokonza nyali, kutuluka ndi kulowa mkati. “Iwo amene ayembekezera pa Ambuye adzatsitsimutsanso mphamvu zawo.”

¹⁵⁷ Zindikirani apa mu nkhani yathu, zindikirani Davide, mfumu ya Israeli, anali iye amene anali nalo vumbulutso la kubweretsa likasa la Mulungu kubwerera ku malo ake; kuti, iwo sanafunsire konse izo mmasiku a Sauli chifukwa Sauli anali atabwerera mmbuyo. Kotero iwo sanafunsire kwa likasa nkomwe, pangano, mmasiku a Sauli, chifukwa iye anali atabwerera mmbuyo ndipo anachoka kwa Mulungu. Kotero Davide, mwamsanga, ali ndi kudzoza . . . Tsopano zindikirani izi, ndi nkhani yosokoneza kwambiri ngati inu simuyimvetisa bwino. Ndipo ine ndikumverera kuti ora likubwera pamene ife tikuyenera kukhala amuna mmalo mwa makanda. U-nhu. Ife tikuyenera kukhala ndi nyama yolimba m'malo mwa mkaka.

¹⁵⁸ Zindikirani Davide, mfumu ya Israeli, mfumu inali itangodzozedwa kumene kukhala mfumu; kapena kusankhidwa kukhala mfumu, Sauli . . . Samueli anamudzoza iye mwa chifuniro cha Mulungu; ndipo iye anali mwamtheradi mfumu yosankhidwa ndi Mulungu, palibe kukaikira pa zimenezo. Ndipo ndi uyu apa, ndipo kudzoza kunamukhudza iye. Izo zinawululidwa kwa Davide. Iye analandira vumbulutso, palibe aliyense amene anali atanena kanthu za izo. “Tiyeni ife tipite ndi kukatenga likasa, chifukwa ndicho chifuniro cha Mulungu kuti ife tikhale nalo likasa kuno ndi ife, kuti ife tizifunsira kwa

Mulungu ndi likasa limeneri.” Kwambiri, chinthu chopambana kwambiri. Kodi inu simukuganiza choncho? Chabwino.

¹⁵⁹ Kumbukirani, koma, iye pokhala mfumu, ndi kukhala nalo vumbulutso, iye anawoloka malire ake. Munali mneneri mu dzikolo dzina lake Natani, iye anali mmodzi amene anadzozedwa kuti apezze vumbulutso. Pali chirichonse choti chiyankhulidwe, Iye anati, “Yehova sachita kanthu mpaka Iye atachiwulula icho kwa atumiki Ake mneneri.” Koma, inu mukuwona, Davide pokhala mfumu, ndi kudzoza kuli pa iye... Tsopano, kodi ilo ndilo Lembalo? Kudzoza kuli pa iye, ndipo anapeza vumbulutso loona; koma izo zinali zolakwika: Chifukwa Natani anali mneneri wa m’badwo umenewo; ndipo vumbulutso silinabwere kwa Natani; ndipo pamene vumbulutso linabwera kwa Davide, iye sanafunsire nkomwe kwa Natani za izo. Iye basi amangopita patsogolo ndi kuchita zomwe iye ankafuna kuti achite. U-nhu.

¹⁶⁰ Koma zindikirani yemwe Davide anafunsira apa mu mutu wa 13, “Koma iye anafunsira kwa akapitawo a zikwi ndi a mazana,” kubwerera kwa osonkhana ake. Mukuwona? “Tsopano, kodi inu simukuganiza kuti ife tiyenera kuchita...?” Izo si zimenezo. Tsopano, iye ankayesera kumuchitira Mulungu ntchito, koma iye sanali wodzozedwa kuti achite izo; mwawona, chifukwa Mulungu anali nayo njira.

¹⁶¹ Monga momwe Mulungu akanakhoza kuyankhula kwa mfu—mfumu za chilonda chake ndi kuchira, koma Iye sanatero, Iye anali nayo njira yoyikidwiratu yochitira izo, imeneyo inali mneneri Wake. Kotero Iye anayankhula kwa mneneri, Yesaya, anamuuza iye kuti abwerere mmbuyo ndi kukamuza Hezekiya zimene zikanati zidzachitike.

¹⁶² Tsopano, Hezekiya ankayankhulana maso ndi maso ndi Mulungu, ndipo—ndipo Mulungu amakhoza kuyankhula kwa Hezekiya, ndithudi, koma Iye anapanga mipita ina! Inu mukumvetsa zimenezo? Mulungu ali ndi njira Yake Yomwe yokhazikitsidwa yochitira zinthu: kutumiza zitsitsimutso, kukamba, kuyankhula, chirichonse chomwe icho chiri. Iye ali ndi njira Yake yochitira zimenezo, ndipo ife siife kanthu kuti tizimuza Iye momwe angachitire zimenezo. Iye amachita izo mwanjira yomwe ingamukomere Iye kuchita zimenezo.

¹⁶³ Kotero, inu mukuwona, Davide, pokhala atadzozedwa... Tsopano, inu mukukumbukira ine ndinanena, kudzoza, kudzoza kwabodza? Kumbukirani Mzimu Woyera ukhoza kubwera ndi kudzamudzoza munthu, ndipo komabe izo ziri kunja kwa chifuniro cha Mulungu. Apa, Izo zikutsimikizira izo pomwe apa. Mwawona? Ife tiyenera kudutsa mnjira ya Mulungu yochitira zimenezo, osati njira zathu, njira ya Mulungu yochitira zimenezo. Chifukwa, Davide, pokhala mfumu, atadzozedwa,

atadzozedwa ndi Mzimu wa Mulungu pa iye (choyimira cha Yesu Khristu), koma umenewo sunali mpita wa Mulungu.

¹⁶⁴ Ndipo khamu lonse, “zinawakomera iwo,” Baibulo linatero. Zindikirani, akapitawo a zikwi ndi a mazana, komanso ansembe ndi afiyoloje ankaganiza kuti izo zinali “zopambana.” Apo pali masukulu anu a Baibulo ndi china chirichonse, iwo ankaganiza kuti izo zinali “zopambana.” Ngakhale anthu onse anavomereza, ndi ansembe, ndi—ndi onse a iwo anavomereza kuti kudzoza kwa mfumu kunali kolondola. Zindikirani! Koma Mulungu anali asanalonjeze kuwulula Mawu Ake mu nyengo Yake kwa *iwo*. Mulungu anali nayo njira Yake yowululira Mawu Ake, koma osati kwa *iwo*. Kumbukirani, izo zinali zosemphana ndi Mulungu.

¹⁶⁵ Chinachake chonga m’masiku a Mikaya mwana wa Imla. Kodi inu mukuyikumbukira nkhani imeneyo? Yuda ndi Israeli anali atalekanitsidwa, ndipo iwo anali nawo maufumu awiri osiyana, ndipo Ahabu anali mfumu pa ufumu umodzi. Ndipo Yehosafati anali wolamulira mfumu—ufumu wa Yuda, ine ndikukhulupirira iwo unali; ndipo Ahabu anali wolamulira Israeli, Yerusalemu.

¹⁶⁶ Zindikirani, ndiyeno apa panabwera gulu la alendo ndipo anatenga gawo la dziko loperkedwa ndi Mulungu limene Mulungu analipereka kwa Israeli, ndipo Afilisti awa kumeneko, kapena Asiriya, anali kugwira malo amenewo ndipo anali kudiyetsa ana awo omwe kuchokera ku nthaka yomwe inali ya Israeli. Ndipo kotero iwo ankayifuna nthaka imeneyo kuti azidyetsa ana awo omwe ndi mabanja awo omwe. Mulungu anawapatsa iwo... Amenewo anali maufulu awo operkedwa ndi Mulungu.

¹⁶⁷ Ndipo kotero Ahabu anamuyitanitsa Yehosafati, ndipo anati, “Tsikani kuno.” Iye anati, “Tawonani uko zomwe mdani wathu akuchita. Kodi nkoyenera kuti ife, anthu a Mulungu, ndi ufulu wopatsidwa ndi Mulungu kuti ife tikhale ndi dziko ili, ilo ndi la kwa ife, Mulungu kudzera mwa mneneri Wake, Yoswa, anagawa dziko ili, ilo liyenera kukhala lathu, ilo ndi la kwa ife, kwa ana athu, ndipo apa achikominisi alilanda ilo? Ndipo ife tiri... Ife tiri ndi njala kwambiri, ndipo iwo ali nawo maufulu athu operkedwa ndi Mulungu. Kodi inu simukuganiza kuti ife tiyenera kupita kumeneko ndi kukalitenganso dziko athu? Ngati inu mungaphatikizane mphamvu zanu: ngati inu Amethodisti, ndi Apresbateria, ndi onse, ndi Apresbateria, ndi Achilutera, ndi zina zotero, nonse mutenge bungwe la ecumenical kuno tsopano, ife tonse tikhala pamodzi, ndipo ife tichitenga chinthucho.” (Ndikunena ndi kuyankhula mu fanizo tsopano.) “Ife tipita kukalitenga ilo.”

¹⁶⁸ “Bwanji,” iye anati, “ndithudi, tonse ndife amodzi.” U-nhu.

169 Tsopano, Baibulo linati, “Awiri angayende bwanji limodzi asanagwirizane?” Mukuwona?

170 Kumeneko pamene munthu wamkulu uja, munthu wamkulu wa Chipentekoste uja, Yehosafati, anasakanikirana ndi gulu lolakwika. Ndipo ndi chimene chachitika kwa Achipentekoste lero. Muli amuna ena enieni mmenemo, koma iwo ali osakanizika mu gulu la chipembedzo limenero. Tulukani mu chinthu chimenecho! Ndi chotembereredwa ndi Ambuye!

171 Zindikirani tsopano! Apo iye anali, ndipo iye anati, “Inde, zimenezo zikumveka zanzeru.” Anati, “Magareta athu ndi anu; anthu athu. Kuyamba nkuyamba, tonse ndife Ayuda. Ndithudi, ife tipita ndi inu.” Koma munali mutangotsala chipembedzo chokwanila mwa Yehosafati kuti anene, “Kodi inu simukuganiza ife—ife tiyenera kumufunsa kaye Ambuye poyamba?” Mwawona? “Ine ndikuganiza lingakhale lingaliro labwino.”

172 Bwanji, Ahabu, “Ndithudi.” Anati, “Bwanji, oh, zedi, ine ndimayenera kuganiza za zimenezo.”

173 “Chabwino, kodi pali munthu wa Mulungu kwinakwake? Kodi muli naye mneneri?”

174 “Aa, ine ndiri nawo foro handiredi a iwo. Ine ndiri nalo bungwe lonse kumusi uko, chipembedzo chonse. Iwo ndi aneneri Achihebri.”

175 Tsopano kumbukirani, Baibulo linati iwo anali “*aneneri*, aneneri Achihebri,” osati aneneri achikunja, aneneri Achihebri; sukulu ya iwo, seminare ya fiyoloje.

176 “Chabwino, abweretseni iwo!”

177 Ndipo mafumuwo anadziveka okha ndi kuyima pamaso pake kuti amukondweretse mneneriyo. Ndipo apa pakubwera, ine ndikukhulupirira iye anali Zedekiya akubwerapo, mkulu wopambana wa aphungu a chigawo, kapena chirichonse chimene iye anali, anabwera kumeneko pakati pawo. Iye anadzipangira yekha nyanga ziwiri zazikulu, iye anati, “Ine ndamva kuchokera kwa Mulungu. PAKUTI ATERO AMBUYE, ‘Ndi nyanga zimenezi inu mudzawakankhira Asiriya uko kuchoka mdzikolo.’”

178 “Oh, ulemerero!” aliyense ankaganiza kuti izo zinali zopambana, chabwino.

179 Yang’anani momwe izo zimayandikira pafupi ndi malire a lumo awo tsopano, pakati pa cholondola ndi cholakwika. Ndipo kumbukirani kuti zidzagwera ku mbali imodzi kapena ina, mpaka izo zimatsika nthawiyina ngati lumo lonoledwa pakati pa kusiyana kwa cholondola ndi cholakwika. Izo zikuyenera kukhala Mawu aliwonse a Mulungu; osangoti pafupifupi Mawu aliwonse, koma Mawu aliwonse! Ndipo izo zatsika pansu lero, osati kwa Achilutera, osati kwa Amethodisti, osati kwa

Achipentekoste, koma kwa m'badwo wosongoka umenewo, mu m'badwo uno momwe kudzoza kwa wotsutsakhristu kuli mwangwiro kwambiri, iko kukanati kunyenge Osankhidwa omwe, iwo adzagwera ku mbali yolakwika ngati iwo sayang'ana izo, ngati mphero. Penyani! Khalani osamala! Ife sitikukhala mu m'badwo wa Chipentekoste tsopano. Ife tadutsa m'badwo umenewo, mofanana basi monga ife tinadutsira wa Chilutera, ndipo tinadutsa... Mukuwona?

¹⁸⁰ Zindikirani. Ndipo aneneri onsewo analosera, foro handiredi a iwo, odyetsedwa bwino, okhazikika bwino, Aneneri Achihebri anawachitira iwo umboni ndi mtima umodzi, "PAKUTI ATERO AMBUYE, 'Pitani, Yehova ali nanu inu."

¹⁸¹ Yehosafati anati, "Chabwino, izo—izo zikumveka bwino. Koma," anati, "kodi inu muli naye mmodzi wina?"

¹⁸² "Mmodzi wina? Ife tiri ndi chipembedzo chonse pano, ife tiri nalo bungwe lonse litasonkhana kunja kuno. Ife tikusowekeranso wina chifukwa chiyani?"

¹⁸³ Iye anati, "Ah, koma ine ndimaganza kuti mwina pakhoza kukhala wina."

¹⁸⁴ Iye anati, "Oh, inde, alipo mmodzi wina, koma iye sali ngakhale wa bungwe ili." U-nhu. "Iye ndi wotayidwa. Ndi Mikaya, mwana wa Imla, ndipo ine ndimamuda." Mukuwona? Anati, "Iwo sangamulandire iye mu chiyanjano, ndipo iye basi ndi wotayidwa wawamba kuyamba nkuyamba. Ndipo iye nthawizonse, chirichonse chimene iye amalosera, iye basi samayilimbikitsa seminare yanga pang'ono." U-nhu. "Ndipo iye amachita zinthu zoyipa zonse izi, iye nthawizonse amalosera zoyipa zokhudza ine, basi kungoti akhale wosiyana."

¹⁸⁵ "Oh," Yehosafati anati, "musati muzilola mfumu azinena chinthu chonga chimenecho. Koma ine ndikufuna nditamva chimene mwamuna uyu anganene."

¹⁸⁶ Anati, "Chabwino, ife timupeza iye." Kotero iwo anatomiza kwina kwake m'chipululu, ndipo iwo anatomiza munthu.

¹⁸⁷ Anati, anamuza iye, anati, "Tsopano, panjira yako yobwerera tsopano, ine ndikufuna ndikuuze iwe chinachake. Kodi iwe ukufuna kuti ubwereranso mu chipembedzo kachiwiri?" Mukuwona? "Kodi iwe ukufuna kukhalanso ndi chiyanjano ndi onse a iwo kachiwiri? Ngati iwe ukutero, ukanene chinthu chomwecho chimene mkuluwampingo wa pa boma akunena, ukanene chinthu chomwecho chimene bishopu akunena, ndipo iwo adzakubwezeretsa iwe. Tsopano ndi nthawi yoti uchite zimenezo."

¹⁸⁸ Koma kodi inu mungalingalire wodzozedwa, mneneri woona wa Mulungu akunyengerera pa Mawu amodzi a Mulungu? Ayi ndithudi!

189 Iye anati, “Pali Mulungu wamoyo, ine ndinena chokhacho chimene Mulungu wanena!” Ife tikusowekera mwana wa Imla. “Pali Mulungu wamoyo, ine ndinena chokhacho chimene Iye akunena.” Ndiko kulondola, “Chomwe *Iye* akunena.”

190 Kotero pamene iwo anafika kumeneko pamaso pa anthu, aneneri onse, iwo anati, “Tsopano, iwe unene iwo . . .”

191 Iye anati, “Dikirani, mundipatse ine usikuuno, mundilole ine ndiwone chimene Ambuye ati anene.” Kotero, usiku umenewo, Ambuye anawonekera kwa iye m’masomphenya ndipo anamuuza iye zoti anene.

192 Mmawa wotsatira iye anati, “Iwe ukuti chiyani, Imla?” pamene iwo onse anali atayima kunja . . . Ine ndikutanthauza “Mikaya, mwana wa Imla,” anati, “iwe ukuti chiyani tsopano? Ife tonse tiri pano pamodzi, ansembe onse, ndi aneneri onse, ndi mafumu onse, ndipo chirichonse chiri pano pamodzi. Iwe ukuti chiyani tsopano pa bungwe lalikulu ili?”

193 Anati, “Pitani,” anati, “koma ine ndinawona Israeli akubalalika ngati nkhoa zopanda m’busa.”

194 Ndipo Ahabu anati, “Ine ndinakuuzani chiyani inu! Wopanduka ameneyo amakhoza kokha kungonenera zoyipa monditsutsa ine!”

195 Kodi iye akanakhoza bwanji kunena china chirichonse pamene Mulungu anali kunena chinthu chomwecho? Mneneri akuyenera kukhala kamwa ya Mulungu akuyankhula, osati maganizo ake omwe. Ake . . . Inu mwawona, iye kwa- . . . wodzipereka kwathunthu kwa Mulungu, iye safana kuvulaza chirichonse, koma iye akuyenera kunena chimene Mulungu akunena, chifukwa iye alibe ulamuliro pa Izo iyemwini. Mukuwona?

196 Iye anati, “Tsopano, ine sindinakuuzeni inu?”

197 Ndiyeno apo panabwera mu—munthu wamkulu ndi nyanga, ndipo anamusasantha iye pakamwa, iye anati, “Ndi njira iti imene Mzimu wa Mulungu unapita pamene Iwo unatuluka mwa ine?” Mwa kuyankhula kwina, ndiloleni ine ndiyesere kuziphwanya izo, “Tayang’anani kuno umu . . . Tayang’anani apa, ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu chinachake, Mikaya. Kodi inu mukuzindikira kuti ine ndine katswiri mu Lemba? Kodi inu mukuzindikira kuti ine ndiri nako kudzoza?” Kapena, “Ubatizo,” tinganene izo lero. “Kodi inu mukuzindikira kuti ine ndiri nazo zimenezo?”

198 Imla anati, “Ine sindikukayikira zimenezo.”

199 Iye anati, “Koma tamvetserani! Mzimu wa Mulungu wandiuza ine, ndipo unachitira umboni ndi foro handiredi anga onse pano, kuti ife ‘tikankha Asiriya kutuluka mu dzikolo.’ Ndipo iwe ndi ndani kuti ubwere ndi kudzanena kuti mfumu

yathu yayikulu iphedwa?” Iye anati, “Mzimu wa Mulungu unandiuza ine zimenezo.”

²⁰⁰ Ndiloleni ine ndingoziphwanya izo kuti inu muzimvetsetse zimenezo. Ndipo mwina ife tikumupeza Mikaya akuti, “Usiku watha m’masomphenya, bwana, ine ndinamuwona Mulungu atakhala pa Mpandowachifumu. Ndipo ine ndinawona khamu lonse la Kumwamba litasonkhana momuzungulira Iye, unhu, ndipo iwo anali ndi msonkhano Kumwamba. Iwo anati, ‘Kodi ife tingakhoze kumupeza ndani kuti apite uko ndi kukamunyenga Ahabu? Chifukwa pansu pa Mpandowachifumu pano pali mneneri, mneneri woona, dzina lake ndi Eliya. Ndipo iye wanenera mwa Mawu Anga ndipo ananena kuti “Ahabu woyipa uja, chifukwa iye anapha Naboti, agalu adzanyambita magazi a munthu woyipayo,” ndipo ife tikuyenera kuzipanga Izo kuchitika chifukwa Izo zinayankhulidwa kale, Izo ndi PAKUTI ATERO AMBUYE! Izo ziyenera kuti zifike pochitika, ziyenera kukhala pamenepo. Ndipo kodi ife tizichita izo motani?”

²⁰¹ “Ndiye kutsika kuchokera ku zigawo zokwawa za otayika, kutali mmenemo kunatulukira mzimu ukuyenda, iye anati, ‘Ndine wonyenga. Ngati ine ndingakugwirireni ntchito Inu, ine ndipita uko ndi kukalowa mwa mneneri wake.’” Chifukwa iwo anali atapanga bungwe kwambiri, iwo amangomvetsa chinthu chimodzi chokha, ndipo ndizo zomverera pang’ono. “Ndipo Ine ndidzawachititsa iwo kuti alosere bodza. Ndipo ine ndidzamatenga Ahabu kuti amvetsere kwa olemekezeka amenewo mmalo mwa mneneri Wanu weniweni; chifukwa iye adzafufuza chirichonse chimene iye akunena ndi Mawu Anu, iye adzafufuza masomphenya *ake* mwa Mawu, iye adzafufuza chirichonse chimene iye akuchita ndi Mawu, ndipo ngati izo siziri ndi Mawu iye sakanati azimvetsera kwa izo. Koma ngati izo . . . Ine ndikhoza kunyenga ena awa, ndipo ndidza . . . iwo . . . Ahabu ali ndi chidaliro chochulukira kwambiri mu umodzi wawukuluwo pamodzi wa chitetezo chawo, kotero iwo amapita mozungulira pamodzi ndipo iwo amabwera pamodzi. Ndipo ine ndidzamatenga Ahabu kuti azimvetsera kwa iwo, kupita kumeneko. Ndipo umo ndi momwe ife tidzachitire zimenezo.”

²⁰² “Mulungu anati, ‘Iwe ukhoza kukachita izo, ndiwe wonyenga weniweni; iwe pita kumeneko.’”

²⁰³ Ndipo kenako Zedekiya anamumenya iye kukamwa, anati, “Iwe unali kuti . . .?”

²⁰⁴ Iye anati, “Udzadziwa ukadzakhala mu ndende yamkati.” Uh-huh.

²⁰⁵ Iye anati, “Pitani!” anatero Zedekiya kwa mfumu. Anati, “Pitani ndipo mudzabwerere mu mtendere!”

²⁰⁶ Ahabu anati, “Mutengeni munthu ameneyo ndipo mumuyike iye mu ndende. Mumuyike iye mmaunyolo, mumudyetse iye mkate wachisoni ndi madzi achisoni. Ndipo

ine ndikadzabwerera ndi chigonjetso changa kuchokera kunja kuno, chimene aneneri anga anandiuza ine kuti ‘chitsitsimutso ichi chidzachitika ndithu,’” anati, “Ndidzathana naye munthu ameneyo!”

²⁰⁷ Tamvetserani ku mawu otsiriza a Mikaya kwa mwamuna ameneyo: “Ngati inu mungabwerere konse, ndiye kuti Mulungu sanayankhule kwa ine.” Amen.

²⁰⁸ Mwaona, Mulungu ali nayo njira Yake yochitira zinthu. Amuna awa ankaganiza kuti iwo amamuchitira Mulungu ntchito. Samalani! Osati zomverera, osati kutengeka, osati zongolingalira, koma zikuyenera kukhala “PAKUTI ATERO AMBUYE,” zikuyenera kukhala zolondola. Chabwino, ziribe kanthu. . . Ife tikuzipeza zinthu izi chomwecho.

²⁰⁹ Zindikirani tsopano pamene Davide anali atapanga kulengeza kwakukulu uku, ndipo chinawoneka ngati icho chinali chabwino, chinthu chabwino kuchichita. Ndiye ife tikupeza kuti (Kodi ndikukutopetsani inu? Kodi ndachedwa kwambiri kuti ndibweretsepo wina?) iwo anali atapanga kulengeza kwakukulu uku, iye sanafunsire kwa mneneri.

²¹⁰ Tsopano, aliyense akudziwa kuti Amosi 3:7 ananena kuti Mulungu analonjeza kuti Iye sadzachita kanthu mpaka poyamba Iye atachiwulula icho kwa mneneri Wake. Kudutsa mmibadwo ya mpingo takhala nawo okonzanso; koma zinalonjezedwa ndi Malaki 4 kuti mudzakhala mneneri mu dziko mmasiku otsiriza (chifukwa izo ziyenera kugwirizana ndi dongosolo limenero, mwaona) isanafike nthawi yotsiriza.

²¹¹ Yesu asanabwere poyamba, Eliya akubwera, Eliya wa Malaki 3. Mateyu 11 amanena chomwecho, “Ngati inu mungazimvetse izo, uyu ndi amene anakambidwa, ‘Taonani, Ine ndituma Wanga—mthenga Wanga patsogolo Panga.’” Tsopano, Iye analoseredwa, afiyoloje onse amakhulupirira zimenezo: kuti mu tsiku lotsiriza, Mzimu wa Eliya udzabwera, nawonso. Iwo ukuyenera kubwera nthawi zisanu, Mulungu amagwiritsa ntchito Mzimu umenewo: Elisa, Eliya, Yohane M’batizi, ndi kwa mpingo wa Amitundu, ndipo kenako kwa Ayuda mu Chivumbulutso mutu wa 11. Ndicho, g-r-a-c-e cha Mulungu, f-a-i-t-h, J-e-s-u-s, Yesu, zi—zilembo faivi. Sizingalekezere pa foro, zikuyenera kufika ku faivi. Mukuona? Zindikirani!

²¹² Tsopano, Iye analonjeza zimenezo, kotero izo zimakhazikitsa Baibulo ndendende basi kufikira lero, ndi Sodomu ndi Gomora. Ndipo Eliya sanali. . . Ameneyo sanali Eliya; Umenewo unali Mzimu wa Mulungu pa Eliya; Eliya anangokhala munthu chabe. Tsopano, ife takhala nawo a Eliya, ndi zovala za Eliya, ndi malaya a Eliya, ndi chirichonse cha Eliya. Koma Eliya wa tsiku lino ndi Ambuye Yesu Khristu. Iye akuyenera kuti adzabwere molingana ndi Mateyu seventini- . . . Luka 17:30, ndi, Mwana wa munthu akuyenera kudzadzilulula Yekha pakati pa

anthu Ake. Osati munthu, Mulungu! Koma izo zidzabwera kudzera mwa mneneri. Tsopano, Iye sanakhalepo nawo konse aneneri aakulu awiri pa nthawi imodzi, ayi, mu dziko lapansi. Mukuona? Ziribe kanthu kuti ndizochulukuka bwanji. . . awiri—mitu iwiri siyingathe. . . Uyenera kukhala mutu umodzi. Mulungu amayenera kumutengera munthu mmodzi pansi pa ulamuliro Wake. Mukuona? Pali Mulungu mmodzi; panali Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, koma Mulungu mmodzi pamwamba pa zonsezo, zindikirani, ndipo anangowagwiritsa ntchito maudindo amenewo. Iye wachitanso chimodzimidzi ndi Eliya, Mzimu wa Eliya; Iye ankagwiritsa ntchito Mzimu umenewo, koma Mulungu yemweyo akuwulamulira Iwo nthawi zonse kuti akwaniritse Mawu Ake.

²¹³ Tsopano, zindikirani mu izi tsopano, Davide ankaganiza kuti chirichonse chinali mu dongosolo. Ndipo iye anadzozedwa. Mukuona momwe Mzimu Woyera ungamudzozere munthu? Koma izo ziyenera kukhala mu dongosolo la kudzoza. Mzimu wakunja ukhoza kudzozedwa ndi Mzimu Woyera, ndipo solo nkukhala yakuda ngati phula. Chisoso chimamera pa madzi omwewo amene amawumba. . . amayika moyo mu tirigu, amayika moyo mu chisoso; koma pansi pa chisosocho, pali moyo wa chisoso. Ichu chikusangalala, ndi kuchita maluwa, ndipo chiri nawo moyo, ndipo nkumachita chirichonse chimene tirigu amachita, koma *solo* yake ndi *chisoso*. Mwaona? Aphunzitsi abodza akhoza kuwuka, nkumaphunzitsa mitundu yonse ya utatu ndi china chirichonse, ndi kukhala odzozedwa ndi Mzimu Woyera, ndi kumachita zozizwitsa zochulukuka basi monga momwe Uthenga woona ungatherere. Koma mwa Mawu apa, ndi zomwe zimachita izo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Tsopano, ndi zabwino kuphunzitsa izi, ine ndikuganiza, ndiri—ndiri mu kachisi wa zipembedzo zosiyanasiyana mmawa uno, mu—mu hotelo iyi kuno.

²¹⁴ Zindikirani, penyani chimene ife tikunena. Tsopano, chabwino, mvetserani. Davide anali nako kumverera konse kumene chitsitsimutso chenicheni chinali nako. Zindikirani! Iwo anafuula, iwo anakuwa, iwo anavina, iwo anapezadi chinachake kuchokera mu kudzoza kumeneko. Ndithudi anatero! Zonse monga chitsitsimutso chenicheni, koma, inu mukuzindikira, Mulungu sanali mu zimenezo. Mulungu sanali mu zimenezo. Iye anali naye mneneri akukhala mu dziko momwemo. Iwo ayenera kuti ankadziwa. Mukuona? Davide ankayenera kudziwa zimenezo.

²¹⁵ Chinachake lero, ife tiri nazo zimango zonse, monga zipembedzo zazikulu, misonkhano yokopa anthu ya nthawi yathu, koma zotsatira zake zikupezeka zofanana ndi zomwe zinali munthawiyo; zotsatira za misonkhano yathu yayikulu yokopa anthu, ndi malingaliro athu aakukulu abwino, nyumba zathu zazikulu, ndi zazikulu zathu. . . kumanga masauzande,

ndi kuwonjezera mamembala ndi zinthu, izo zimawoneka mwanjira yomweyo, zonse zolephera. Ine sindikunena zimenezo kuti ndikhale wosiyana, ine ndikunena zimenezo kuti ndikhale woonamtima pamaso pa Mulungu, Yemwe Bukhu Lake ine ndikuyima nalo mmawa uno. Mukuona? Zonse zimakhala zolephera, zotsatira zofanana.

²¹⁶ Tsopano tiyeni ife tione chimene chinachitika pamene Mulungu (mu nthawi Yake ndi m'badwo) ndi aneneri Ake sakuwerengeredwa, amangodalira pa fiyoloje, ansembe, zipembezdo monga ife timachitira lero. Tsopano, mwatcheru. Izo zonse zimasokonekera. Ngati Mzimu woona wa Mulungu pamenepo, Iwo udzalondolera iwo mu Mawu; osati malo amodzi okha mu Mawu, Mawu onse kwa m'badwo wonsewo. Mukuona?

²¹⁷ Tsiku la Pentekoste, Mzimu unalondolera iwo mu Iwo, ku Yoweli 2:38. Mukuona? Tsiku la Luther, Unalondolera iwo mu Iwo; Wesley; mu chochitika ichi chotsiriza cha Chipentekoste; koma uwu ndi m'badwo wina, uku ndi kuyitanira kunja kwa Mkwatibwi. Osati zaka thuu sauzande zapitazo pa Pentekoste, kapena kubwereza, kapena kubwerera. Pentekoste . . .

²¹⁸ Mzimu Woyera unali mwa Luther, Mzimu Woyera unali mwa Wesley; ndi Mawu a Mulungu akudzozedwa. Ndipo Mzimu Woyera unabwerera kwa anthu a m'badwowo ndipo iwo anayamba kukhala ndi kubwezeretsedwa kwa mphatso. Iwo anapeza kuti, podzipereka okha kwa Mulungu, Mzimu Woyera unayankhula mmalirime kudzera mwa iwo. Iwo anayika manja awo pa odwala, ndipo iwo anachira. Iwo anavina mu Mzimu. Mukuona? Umenewo unali m'badwo wa Kukonzanso kuwubweretsanso mpingo mu dongosolo. Ndipo dongosolo lotsiriza la mpingo linali kukhazikitsa mphatso mu mpingo; monga Luther anakhazikitsa kulungamitsidwa, Wesley anakhazikitsa kuyeretsedwa, Pentekoste anakhazikitsa mphatso. Koma kodi iwo anachita chiyani? Kulakwitsa komweko, monga chirengedwe chafanizitsidwira ku phesi la tirigu, iwo anapanga chipembezdo, chimene chiri chotsutsana ndi Mulungu, zosemphana ndi Mulungu.

²¹⁹ Tsopano, ife tikupeza kuti pamene . . . Ndiye pamene osonkhanitsa mapesi awa abwera pamodzi, amapanga lingaliro lawolawo. Ndipo ziribe kanthu . . . Pamene a “nkhani yatsopano,” monga iwo amazitcha izo, anatuluka kuchoka ku Assemblies of God, kodi iwo anachita chiyani? Iwo sakanakhoza kuchilandira Ichu. Ziribe kanthu ndi Choonadi chochuluka bwanji, ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, iwo anali kale Bungwe Lalikulu. Munthu anali atazilanda kale izo, Mzimu unali utawachokera kale iwo. Kulondola! Ndiyeno izi zinatulukira . . . Ine ndayankhula ndi ena mwa atsogoleri anu abwino; iwo amati, “Chabwino, ife tikanachita chiyani tsopano?” Iwo akanadzichititsa manyazi okha. Pamene, iwo adziwa kuti ndi Choonadi; ngati iwo satero, iwo ndi akhungu

mwauzimu ndi mbuli ku Baibulo. Sindikunena izo monyozetsa, tsopano, ndikunena izo molemekeza. Chifukwa, mulibe malo mu Baibulo pamene aliyense anayamba wabatizidwapo kugwiritsa ntchito maudindo amenewo, “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Ndipo sanagwiritsidwe ntchito konse mpaka pambuyo pa bungwe la ecumenical, mpingo wa Roma Katolika. Katekisimu wawo yemwe amachitira umboni chinthu chomwecho. Ndi miyambo ya Chikatolika! Osati chiphunzitsa cha Baibulo, koma miyambo ya Chikatolika. Ndipo inu Amethodisti munatulutsa ma katekisimu anu ndi chirichonse basi monga iwo anali nazo, mukungokula mwapang’onopang’ono kuchokera ku icho. Koma tsopano pamene inu mufika ku Pentekoste, ndi kufalitsa ina ya miyambo imeneyo, inu munagwiritsitsabe kwa iyo.

²²⁰ Koma tsopano ndi kuyitanira kwa Mkwatibwi, tsopano ndi pamene Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zatsegulidwa, tsopano pamene zinthu zathunthu zimene okonzanso anazisiya ziyenera kutsegulidwa; ndipo ndi Malaki 4 yekha angachite zimenezo, chifukwa zimatengera vumbulutso molunjika kuchokera kwa Mulungu kwa munthu payekha kuti achite chomwecho. Ndiko kulondola! Izo sizingabwere kwa gulu, sizinachitike nkome. Munthu mmodzi! Ndicho chimene Mulungu analonjeza mu zoyimira za kudza kwa Mkwatibwi Wake, Elieza. Mukuona?

²²¹ Zindikirani pamene ansembe, atumiki, ndi ena otero, angapeze kudzoza kwawo komwe, ndi kudzozedwa moona. Davide anadzozedwa. Baibulo linanena chomwecho. Koma, inu mukuona, iye anadutsa mu gwero lolakwika, iye anapita ku mpita wolakwika. Iye anadutsitsa kudzoza kwake ku mbali yolakwika, kwa anthu ndi zomwe iwo ankaganiza, kwa akapitawo, zomwe iwo ankaganiza, mmalo mopita ku mpita woyera wa Mulungu kuti apeze chimene PAKUTI ATERO AMBUYE anali, “Kodi ino ndi nthawi yake? Kodi ino ndi nyengo yake? Kodi ichi ndi chifuniro cha Mulungu?”

²²² Ndiye ngati iye ali mneneri woona wa Mulungu, apita pamaso pa Mulungu choyamba, ndikuti, “Atate, ndi chiyani icho?” monga Natani anachitira pambuyo pake kwa Davide.

Davide anati, “Kodi ndi koyenera kuti ine ndidzikhala m’nyumba ya mikungudza, ndi likasa la Mulungu wanga pansu pa mahema kunjaku?”

²²³ Ndipo yang’anani pa Nataniyeli, anati, “Davide, chita zonse zomwe ziri mu mtima mwako, pakuti Mulungu ali ndi iwe. Ndiwe chotengera chodzozedwa cha Mulungu.”

²²⁴ Koma uyo pokhala mneneri, ndi kulakwitsa kwake, ndipo Mulungu ali ndi udindo kwa mneneri Wake. Usiku umenewo Iye anawonekera kwa iye, anati, “Pita ukamuuze mtumiki Wanga Davide, Ine ndikuyamikira kulimba mtima kwake, Ine ndimamukonda iye chifukwa cha ichi, chifukwa iye ndi

mwamuna wa pamtima Wanga Womwe, ndipo Ine ndikudziwa kuti ndi nthawi yoti likasa Langa likhale mwanjira imeneyo, liyikidwe pansu pa chinachake, koma Ine basi. . . Si nyengo yake yoti izo zichitike. Ine ndidzamalola mwana wake kuti adzachite zimenezo, koma ine sindidzamalola iye kuti achite zimenezo.”

²²⁵ Ndiye apa pakubwera Natani ndi, “PAKUTI ATERO AMBUYE, Davide, vumbulutso lalikulu limene inu munali nalo ndi lolakwika monga momwe linaliri pamene inu munabweretsa likasa.” (Uh-huh! Uh-huh! Mukuona?) “Musachite zimenezo. Musayesere izo! Koma Mulungu anati Iye adzamalola ‘mwana wanu kuti adzachite zimenezo.’” Pamene! Mukuona? Ndizimenezotu!

²²⁶ Davide anadzozedwa kuti anene zimenezo chifukwa ankakhoza kuziona patsogolo pake, monga mmene Abrahamu ankafunira Mzinda pa dziko lapansi. Inu mukudziwa, iye anali kuchiyembekezera icho chifukwa iye akanadzakhala kuno tsiku lina, Abrahamu ali, mu Mzinda umenewo. Ndipo iye anapita mozungulira kuwufunafuna iwo. Ndipo ali pa malo omwewo pamene iye ankayang’ana, iwo unali basi pamwamba pake ndiye, ndipo udzabwerera mu Zakachikwi ndipo iye adzakhala mu Mzinda umenewo. Koma pokhala mneneri, iye anakhazikitsidwa ndi kudzozedwa, iye ankadziwa kuti kunali Mzinda kwina kwake, ndipo iye ankawufunafuna iwo. Koma, inu mukuona, vumbulutso lonse la izo linabisidwa kwa iye. Sizinali za m’badwo wake. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . mpaka mmusi kukafika kwa Yohane, kumene iye anauwona iwo ukutsika kuchokera kwa Mulungu kuchokera Kumwamba. Umenewo unali Mzindawo.

²²⁷ Mwaona, chirichonse chiyenera kukhala mu nyengo yake. Inu mumadzala tirigu wanu mu dzinja ndipo. . . kapena mu masika ndi kumweta mu chilimwe chotsatira. Mukuona? Izo ziyenera kubwera kudzera mu phesi, kenako kubwera kudzera mu ngayaye, ndi mankhusu, ndi kupitirira mpaka mu. . . Ziyenera kukhala mu nyengo. Chirengedwe chonse chimayenda mopitirira. Mzimu wa Mulungu unapanga chirengedwe, ndipo zonse Mulungu ndi chirengedwe ziri mu kupitirira. Zinthu zonse zimene zinaikidwa mu kachisi zinali chitsanzo cha zimene iye anaziwona Kumwamba.

²²⁸ Inu mukaona mtengo ukuvutika kuyesetsa kuti ukhale moyo, zikutanthauza kuti pali mtengo womwe siumafa. Inu mukamuona munthu akuvutika chifukwa cha moyo, zimasonyeza kuti pali kachisi akudikirira kwina kwake yemwe samafa. “Ngati kachisi uyu wapadziko lapansi adzapasuka ife tiri naye kale wina akudikirira.” Atate wabwino wa Kumwamba anandilora ine kuti ndikayende kuseri kwa katani imeneyo tsiku lina ndi kukaziwona izo. Ndi angati anamva a. . .? . . . Mukuona? Kuyang’ana modutsa katani ya nthawi. Kumeneko izo zinali chimodzimidzi monga ine

ndikulalikirira kwa inu nonse, pamenepo iwo anayima. Miyoyo pansi pa guwa, ikulira, “Mpaka liti?” Osati nthano chabe, winawake amene anali ndi luntha: “Mpaka liti, Ambuye?” Mukuona? Pamene ife tikumverera izo tsopano, monga msinkhu wathu, monga M’bale Bill Dauch wakhala pano pa nainte-firii. Pali chinachake chimene chikulakalaka mnyamata ameneyo kachiwiri. Pali chinachake . . . Mukanatha kupereka chirichonse. Momwe ine ndikanakondera kutero. M’bale Jack, ndi ena tonse a ife. Kubwerera, M’bale Hierholzer, mkati muno, mu unyamata umenewo. Kodi ife tikufuna kuti tichite zimenezo chifukwa chiyani? Kuti tikhale aang’ono ndi kumathamanga mozungulira kenanso? Ayi, bwana! Chifukwa ife tikumverera kuti tikanakhala ndi nthawi yochuluka yomulemekeza Mulungu amene ife timamukonda.

²²⁹ Ndipo abale anga okondedwa, ine ndiri ndi Uthenga uwu mmawa uno, kuli Dziko kutsidya kwa mtsinje limene iwo amalitcha kuti lokoma kwanthawizonse. Kumeneko tidzamulemekeza Iye kudutsa m’mibadwo, ndi mibadwo yonse, ndi Umuyaya. Nchifukwa chiyani tikumverera choncho? Chifukwa chakuya chikuyitanira ku Chakuya. Ndipo bola ngati chakuya chikuyitana, pakuyenera kukhala Chakuya kuti chiyankhire ku kuyitana kumeneko kapena sipakanakhala kuyitana. Pasanakhale chirengedwe, pamayenera kukhala Mlengi choyamba kuti alenge chirengedwecho, kapena apo palibe . . . Izo zimasonyeza umboni womwewo umene ulipo.

²³⁰ Zindikirani ansembe awa, onse kunja kwa mzere. Zindikirani kudzozako, chabwino, palibe cholakwika ndi kudzozako. Chimodzimodzi ndi inu Achipentekoste, koma yang’anani mpita womwe inu mukuyendamo tsopano. Tsiku lasintha chiyambireni Pentekoste, chinachake chikuchitika. Mukanakhala munalibe mneneri mu dzikolo, mwinamwake Davide akanakhala akulondola. Uko kulondola. Koma apo panayima Natani, wotsimikiziridwa, wokhazikitsidwa, wochitiridwa umboni ndi Mulungu kukhala mneneri.

²³¹ Penyani! Likasa mu Baibulo nthawizonse ndi choyimira cha Mawu kwa ife, chifukwa anali Mawu a Mulungu mu likasa. Ndipo anali . . . Zindikirani likasa limene iwo analibweretsa, yang’anani momwe iwo anachitira izo. Ilo silinayikidwe pa malo ake apachiyambi okhazikitsidwa ndi Mulungu. Tsopano, Mulungu ananena kumbuyo kuno mu Chilamulo kuti izo ziyenera . . . momwe izo ziyenera kuchitidwira, momwe likasa ili liyenera kusunthidwira, ndi amene akuyenera kumalisuntha ilo. Koma Davide, pansi pa kudzoza kwake . . .

²³² M’bale wanga, musaphonye izi. Ndipo alongo anga, inu amene mukufuna kuti mukhale alaliki achikazi ndi zina zotero, musaphonye izi. Ziribe kanthu momwe kudzoza kwanu kwachulukira, inu muyenera kulowa mmalo operekedwa ndi Mulungu. Kudzoza kwa Davide kunali kwabwino, koma pochita

izo iye anatengeka ndipo anadutsa mzere wamalire. Kodi iye anachita chiyani? Anadutsa mzere wamalire. M'malo moliyika likasalo pa malo ake apachiyambi, iye analinyamula ilo pa ngolo yatsopano ndipo osati pamwamba pa mitima ya Alevi. Ilo linkayenera kunyamulidwa pa maphewa a Alevi, limene liri pamwamba pa mtima. Mawu siali mmalingaliro, Iwo ali mu mtima! "Osati pa ngolo yatsopano." Chimenecho chinali chiyani? Zina... Zinkayimira chinachake chatsopano, Davide anachichita pamenepo, zinkayankhula za chipembedzo chirichonse chimene chikanati chidzakhalepo. Mawu a Mulungu sayenera kukhala ndi... kunyamulidwa ndi akulu ampingo a mdziko kapena mabishopu, ndi ena otero, a zipembedzo. Ndi Ubatizo wa Mzimu Woyera mu mtima wa munthu, ndipo osati mu kachitidwe kena kachipembedzo. Mzimu Woyera ndi chuma cha chikondi cha Mulungu mu mtima mwa amuna ndi akazi kuti adziwumvera. Mukuona?

²³³ Panali pa mapewa a atumiki Ake, atumiki Ake anali Alevi. Ankaliyika ilo paphewa lawo lakumanzere ndi kulinyamula likasa limenero munga choncho, chifukwa ilo linali pamwamba pa mtima wawo. Iwo anali nako kulemedwa kwa Mawu pa mtima wawo. Ameni! Tsopano inu muli nako kulemedwa kwa chipembedzo chanu pa mtima wanu, kulemedwa kwa osonkhana anu: kaya inu mumanga *ichi*, kapena kuchita *icho*, kapena kuchita chinachakenso. Kulemedwa kwa chiwerengero chomwe mungachitengere ku chipembedzo chanu; mmalo mwa kulemedwa kwa Mawu a Ambuye, kuti anthu amenewo adzangoona Mawu a Mulungu okha osati china chirichonse. Koma inu mwawatengera Iwo pa ngolo yamakono tsopano. Mukuona? Akuwanyamula Iwo kuno ngakhale mu bungwe la ecumenical, paphewa. Ine sindikufuna kuti ndikhale wotsutsa, ndipo Mulungu andithandize ine tsopano. Ine ndikungokuuzani inu Choonadi.

²³⁴ Tsopano, mokopedwa ndi zikhulupiriro ndi mabungwe a ecumenical, Mawu, Mawu enieni a nyengo ya m'badwo umenewo ananyalanyazidwa, chifukwa iwo anali nazo zotengeka zochulukuka. Koma Davide, mfumu yodzozedwa... Iye anali mfumu, koma iye anali mfumu yodzozedwa. Inu mukuti, "Ndine mtumiki, wodzozedwa." Ndiye khalani mtumiki, musayesere kuti mukhale mneneri. Mukuona? Ngati ndinu mlaliki, khalani mlaliki.

²³⁵ Kumbukirani Uziya, m'masiku a Yesaya, mfumu yaying'ono... mneneri wamng'onoyo. Uziya anali mwamuna wopambana, mwamuna wodzozedwa, Mulungu anamudalitsa iye; anadzidalitsa yekha. Eya, ine ndinalalikirira pa zimenezo kwa inu pano nthawi ina. Ndipo tsiku lina iye anadzikuza kwambiri mpaka iye ankaganiza kuti iye akanakhoza basi kutenga udindo wa wansembe, ndipo anatenga moto ndipo analowa pamaso pa Ambuye. Ndipo a... Ansembe amenewo anamuuzi iye,

“Usachite zimenezo, Uziya!” Koma iye anadzikuza. Mneneriyo sakanakhoza kumuuzza iye kanthu. Ansembe ankadziwa lamulo lawo, iwo ankasunga lamulo lawo, iye anati, “Si lamulo lako, Uziya. Usachite zimenezo!”

²³⁶ Chabwino, iye anawakhalitsa iwo “Chete!” Ndipo iye anapita ndi—ndi moto, kuti akapereke, kutenga ntchito ya wansembe; iye anadzozedwa kukhala mfumu, osati wansembe. Ndipo ansembe aja anali kuyesetsa kumuuzza iye, “Ndiwe mfumu yopambana, ndiwe wodzozedwa, Mulungu watidalitsa ife mwa iwe. Koma ndiwe mfumu, osati wansembe.”

²³⁷ Ndipo inu abusa simuyenera konse kumuuzza mneneri choti achite, kapena inu alaliki kumuuzza m’busa. Mwaona, aliyense ali ndi udindo wake ngati iwo uli wozindikiritsidwa mwangwiro.

²³⁸ Kotero iye analowa ndi motowo, ndipo anakanthidwa ndi khate ndipo anafa.

²³⁹ Tsopano apa pali Davide, mfumu. Davide akuyesetsa kuti achite chinthu chomwecho apa. Iye wadzitengera izo pa iyemwini. “Chabwino, izo ziri bwino, ndiyenera kupita.” Anayang’ana mozungulira kwa anthu, “Ukuti bwanji, kapitawo? Iwe uli nawo teni sauzande.”

²⁴⁰ “Ulemerero kwa Mulungu, Davide, ine ndikumverera Mzimu.” Oh, iye anatero! Iye anawumverera Iwo. “Iwe ukuganiza bwanji, Davide? Kodi iwe ukuwumverera Iwo?”

²⁴¹ “Ulemerero kwa Mulungu, Zonse ziri pa ine! Tiyeni tifufuze ndi kuona ngati ziri zolondola, tiyeni tione. Kodi likasalo ndi la kwa ndani?”

²⁴² “Ndi lathu! Ndi la pakati pathu.”

²⁴³ “Kodi tifunsire kwa ndani? Ndithudi, likasa.” Chinthu chomwecho basi monga malo amenewo anali a kwa—kwa Israyeli m’ malo mwa Afilisti. Ndiko kulondola, ndi awo. “Ndipo pamene ine ndikumverera kudzoza, inenso.”

²⁴⁴ Akapitawo a mazana, osonkhana onse, “Ulemerero kwa Mulungu!” Iwo anawombera mmanja, ndipo iwo anafuula, ndi kuvina, ndi kulumphamba mmwamba ndi pansu.

²⁴⁵ Iwo anali ndi Mzimu, koma kodi inu mukuganiza kuti Atate ankaganiza chiyani? “Momwe ine ndamutumizira Natani, mneneri ameneyo kumusi uko! Iwo akudziwa choti achite, ndipo chimodzimodzinso Davide, koma tsopano iye anangotengeka yense ndipo anawoloka malire ake ndi kupita kuti akachite *zimenezi*.”

²⁴⁶ Chabwino, zindikirani, “kulinyamula Ilo pa mapewa” linali dongosolo la Mulungu lapachiyambi. Pali *zokakamiza* zisanu. Ine ndikufuna kuti inu muzilembe izi, ngati mutero. . . Ndikuwona mukulemba.

Ndipo ndi maminiti twente, maminiti twente chakuti itadutsa teni, kotero ndiyetsa kuti ndimalize ikamakwana leveni, ngati nkotheke. Ndifulumira mwamsanga basi momwe ine ndingathere.

Ziribe kanthu mmene munthu angakhalire woonamtima pomutumikira Mulungu, ziribe kanthu mowona mtima bwanji, kudzozedwa mochuluka bwanji, mochuluka bwanji mungakhalire Apresbateria, Abaptisti, Achipentekoste; ziribe kanthu kaya ndinu bishopu, dikoni, chirichonse chimene muli, m'busa, mlaliki, mneneri, chirichonse chimene chingakhale; pali zokakamiza zisanu zomwe ziyenera kuganziziridwa poyamba. Ziribe kanthu ndi kudzoza kochuluka bwanji, zinkaoneka zabwino bwanji, mmene anthu ankafuulira, chirichonse chimene Mzimu ukuchita, pali *chokakamiza*.

²⁴⁷ Tsopano, abale anga, pamene inu mukukonzekera pepala lanu, kodi inu mukumvetsa tsopano chifukwa chiyani? Tsopano kumbukirani, nonse mwakhala mukuganiza, ndipo mwakhala mukuphunzitsidwa pakati panu, osati... (mukuona, ine ndikuyankhula ku fuko lonse)... kuti ine sindinakhulupirire mu kuyankhula malirime. Ine ndimakhulupirira mu kuyankhula m'malirime, koma inu mukhoza kumayankhulabe m'malirime ndi kusakhala nawo Mzimu Woyera. Akorinto Woyamba 13, amati, "Ngakhale ndiyankhula ndi malirime a anthu ndi angelo, sindine kanthu apobe." Mukuona? Ndiko kudzoza kwa Mzimu Woyera, komwe kulibe kanthu kochita ndi solo mkati mwanu. Inu mukhoza kuyankhula m'malirime ndi kukana Mawu. Ine ndaziwona izo zikuchitidwa, ndipo inu mumazona zimenezo inunso. Mukuona? Mkazi akhoza kulalikira Uthenga ndipo... Mwaona? Akhoza kuchita zonse... Iwo amameta tsitsi lawo, ndipo komabe amafuula ndi kumayankhula m'malirime ndi china chirichonse. Uh-huh, ndiko kulondola ndendende. Inu muyenera kufola ndi Choonadi cha Mawu.

²⁴⁸ Zindikirani! Ziribe kanthu momwe munthu angakhalire woonamtima, ziribe kanthu ndi mopambana bwanji momwe iye wagwiritsidwira ntchito ndi Mulungu, ziribe kanthu chomwe ali, iye akuyenera kukhala ichi: akuyenera kukhala... Chinthu chimene iye akuchinena chiyenera kukhala pa nthawi yake mwa Baibulo. Winawake akuti, "Chabwino, Mose kumbuyo uko." Ine ndikudziwa zimene Mose anachita, koma izo si zimene Mulungu akuchita lero. "Chabwino, kumbuyo uko, zaka sarte zapitazo, Luther anatero..." Izo zikhoza kukhala zabwino, koma izo si zomwe Iye akuchita lero. "Chabwino, zaka forte zapitazo, Pentekoste anagwa." Koma izo si zomwe Iye akuchita lero. Mukuona? Zikuyenera kukhala pa nthawi yake.

²⁴⁹ Izo ziyenera kukhala molingana ndi Lemba. Zikuyenera kukhala mu nyengo, chachiwiri. Chachitatu, ndipo ziyenera kukhala molingana ndi momwe Mawu a Mulungu ananenera kuti zidzakhalira.

²⁵⁰ Ndipo inu mukuti, “Ulemerero kwa Mulungu! Mzimu Woyera unagwera pa ine, aleluya, monga momwe Iwo unachitira pa Tsiku la Pentekoste.” Koma zimenezo zingakhale zosiyana lero. Iwo unagwera pa Davide, nayenso, sichoncho iwo? Ndithudi, Iwo unatero. Unagwera pa Uziya, koma zinali zolakwika! Mwaona, inu muyenera kuti mupite mozama kuposa pamenepo tsopano. Mukuona? Inu muyenera kupita mozama kuposa pamenepo. Tsopano, musamverere kupwetekedwa, basi—ingokhalani molemekeza.

²⁵¹ Ndipo zindikirani, ndipo komanso ziyenera kubwera kwa munthu wosankhidwa ndi Mulungu. Osati kusankha kwa chipembedzo, osati mwa kusankha kwa anthu, koma molingana ndi kusankha kwa Mulungu. Ndipo ngati uli Uthenga wochokera kwa Mulungu, wa vumbulutso lalikulu lochokera kwa Mulungu, iwo uyenera kubwera kwa mneneri Wake. Tsopano, ngati inu mukufuna Lemba la zimenezo, ndi Amosi 3:7. Mukuona? Tsopano, izo ziyenera.

²⁵² Pali zinthu zisanu zomwe ziyenera kukhala: Ziyenera kukhala mu nyengo. Ziyenera kukhala pa nthawi imene Mulungu anati zikanadzakhala. Izo ziyenera kulembedwa m’Mawu a Mulungu. Izo ziyenera kukhala mu nyengo ya nthawi ya Mulungu, mwaona. Ndipo izo ziyenera kukhala mwa kusankha kwa Mulungu.

²⁵³ Ndipo Mulungu samasowa aliyense wa ife kuti azitanthauzira Mawu Ake, Mulungu ndi Wodzitanthauzira Yekha. Iye samasowa maseminale athu. Iye samasowa nzeru zathu, ndi zamkhutu. Mukuona? Eva anakhala nazo izo, uhuh, ndipo anaphonya Kutanthauzirako ndi nzeru zake.

²⁵⁴ Mukuti, “Oh, mnyamata, munthu ameneyo ndi mwamuna wanzeru.” Chabwino, izo sizimatanthauza kanthu. Ndithudi. Ahabu anali mwamuna wanzeru. Belteshazzar anali mwamuna wanzeru. Satana anali wothyathyalika kwambiri komanso wankhanza, wochenjera, palibe aliyense wa inu amene akanakhoza kumupirira iye, palibe nkomwe.

²⁵⁵ Ine sindimadalira pa...chirichonse...osati pa nzeru, ndimangodalira pa Mulungu. Mukuona? Kodi Mulungu ndi wotani? Iye ndi Mawu. Ndiyeno kodi Mulungu amatanthauzira bwanji Mawu Ake Omwe? Mvetserani mwatcheru tsopano, musaphonye zinthu izi. Kodi Mulungu amatanthauzira bwanji Mawu Ake Omwe? Powapangitsa Iwo kuti achitike, osati *amodzi* okha apa, koma *onse* a iwo kwa nyengo imeneyo.

²⁵⁶ Osati, “Nowa pita kunja ndipo ukalalikire, iwe wadzozedwa,” koma, “Manga chombo, ika zitseko mmenemo, chikonze icho mwanjira *iyi*, ndi mwanjira *iyoyi*.” Nanga bwanji ngati angayike chitseko pamwamba m’malu mwa pansu? Nanga bwanji ngati angayike zenera pansu, chitseko pamwamba? Mwaona? Izo ziyenera kulangizidwa molingana ndi nthawi yake,

chifukwa ndizo ndendende zimene Mulungu ati azigwiritsire ntchito izo. Ziyenera kukhala mwanjira imeneyo, ndipo ziyenera kubwera mwa kudzoza.

²⁵⁷ Ine ndinamumva munthu akunena nthawi ina, anati, “Ndikukhulupirira munthu ameneyo amapempherera odwala, ine ndikukhulupirira izo nzabwino. Koma zokhala mneneri,” anati, “Ine ndikukhulupirira iye ndi mneneri wa Mulungu; koma ngati mphunzitsi, bwanji, iye ndi wa ‘Yesu yekha.’” Zomwe a . . . Ndi munthu wamtundu wanji amene inu mungamutche? Munthuyo sakudziwa zomwe iye akunena.

²⁵⁸ Mawu omwe oti *mneneri* amatanthauza kuti “iye ndi wowulula Mawu a Mulungu,” kutanthauzirako kumangobwera kwa ameneyo. Ndipo ndicho chifukwa lero ife tiri mu kusowa koteru kwa munthu wamkulu uyu amene akuyenera kuti atumizidwe kwa ife m’mawonekedwe a mneneri Eliya, chifukwa lidzakhala vumbulutso la Mulungu lodziwika kwa ife mwa kutsimikizira, kusonyeza kuti ndi tsiku ndi ora ndi nyengo zimene Mulungu anazilonjeza kudzakhalamo. Ndipo, kumbukirani, iye adzayankhulidwa momutsutsa; nthawizonse zakhala choncho, nthawizonse zidzakhala choncho. Kukanidwa, basi monga momwe mankhusu angachokere . . . Poyamba iye adzalandiridwa, chifukwa mankhusu amangogwira tirigu mpaka atakhoza kutulukira ku dzuwa. Chipentekoste chidzangophimba chabe Uthenga, kuwupatsa Iwo khomo lotseguka kufikira Iwo utamwazika, ndiyeno mankhusu adzachokapo, ndipo tirigu adzagona mu Kukhalapo kwa Mwana, mwaona, kuti ache.

²⁵⁹ Sipadzakhala chipembedzo chirichonse, ingokumbukirani. M’bale Jack pano ndi wa za mbiriyakale, ambiri a inu pano muli. Sipanayambe pakhala chitsitsimutso koma pafupifupi zaka zitatu chikatha chitsitsimutsocho iwo amayamba chipembedzo pa icho. Ndi kulondola uko? Ndipo kusuntha kotsiriza kozizwitsa kwakukulu uku kwa Mulungu m’masiku otsiriza ano, kwafika zaka twente; ndipo kuli mailosi miliyoni kutali ndi chipembedzo, kukupita motalikira nthawi zonse; mankhusu akuchokapo, palibe mgwirizano, palibe kanthu ndi Iye. Mukuona? Nthawizonse iwo amachoka kwa Iye. Sipangakhale chinanso, ndi tirigu tsopano. Koma ndife obiriwira kwambiri. Uh-huh. Uko nkulondola. Ayenera kugona mu Kukhalapo kwa Mwana kuti akhale wokhwima, ndizo zonse za izo. Kubiriwira kochuluka; ife tiribe kuwonamtima, kupatulika, chinthu chimene ife tikuyenera kukhala nacho pakati pathu, kudziwa kuti Mzimu wa Mulungu wamoyo, ukuyenda mu Mawu Ake ndi kutisonyeza ife zinthuzo, apobe.

²⁶⁰ Ife tiri ndi otsanzira abodza akuwuka. Kodi amenewo ndi oti achite chiyani? Anyenge. Baibulo linati iwo akanadzatero. “Monga Yambre ndi Yane analimbana ndi Mose, momwemonso awa adzatero m’masiku otsiriza.” Mukuona? Iwo amachita

chinthu chomwecho, amabwera motsatira nkumatsanzira Izo, ndendende basi. Mukuona? Samalani! Penyani Chiphunzitso cha Baibulo. Penyani uthenga umene ukutsatira zizindikiro zimenezo! Sukulu yakale yomwe ija ya uthenga? Iwalani zimenezo!

²⁶¹ Mulungu anatumiza zozizwa ndi zizindikiro kuti adzakope tcheru cha anthu Ake. Pamene Yesu anabwera akungochiritsa odwala ndi zina zotero, chomwechonso aneneri anachita. Iwo anaganiza, “Oh, ulemerero, Iye akubwera, Iye adzakhala Mfarisi. Iye adzakhala Msaduki.”

²⁶² Koma Iye anati, “Inu m’badwo wa njoka ndi amamba.” Anati, “Ndinu a atate wanu mdierekezi, ntchito zake inu mukuzichita.” Anati, “Pokhapokha inu mudye thupi la Mwana wa munthu, ndi kumwa Magazi Ake, mulibe Moyo mwa inu.” Iye sanazifotokozere Izo. Iye sankasowa kuti azifotokozere Izo. Aleluya. Izo zinali za nyengo ina. Uh-huh. Iye anangonena zomwe Iye ankayenera kuti anene, “Ine nthawizonse ndimachita icho chimene chiri chokondweretsa kwa Atate, ndipo ndicho kusunga Mawu Ake. Ngati ine sinditero, moyo Wanga ndi ntchito Zanga sizikufanana ndi Mawu Ake amene ndikuyenera kuwachita, ndiye musandikhulupirire Ine, Ine sindine Iye; koma ngati zitero, ndiye khulupirani ntchitozo ngati simungathe kundikhulupirira Ine,” Iye anatero.

²⁶³ Zindikirani tsopano *zokakamiza* zimene zikuyenera kuchitidwa.

²⁶⁴ Tsopano, onani, Mulungu anali asanachiwulule chinthucho kwa iwo mwa njira Yake yoperekedwa, Iye anali atachiwulula icho mwa kudzoza, koma izo zinali mu mpita wolakwika. Mwaona, kudzoza kumayenda bwino, koma ngati kuli mu mpita wolakwika, iko kumaperekedwa molakwika. Monga inu mutenge chipolopolo ndi kuchiwombera icho molunjika ku chandamale, icho chimapanga njira yake ku chandamale, koma mphepo ikhoza kuchiwulutsira icho kumbali. Tsopano, mu galimoto yanu, mumapita chotsika ndi msewu sikisite, mailosi sevente pa ora ndipo mphepo imakuwombani inu, inu mukhoza kuwongola magudumu anu mmbuyo, kuwabwezeretsa iwo mu msewu kachiwiri. Koma inu simungachiwongolere chipolopolo; palibe kalikonse mmenemo kuti kawongole magudumu ake, icho chimaphonya chandamale. Mukuona, icho chiyenera kuyenda mu mpita wake wapachiyambi.

²⁶⁵ Momwemonso Mawu a Mulungu ayenera kuyenda mu mpita Wake wapachiyambi. Palibe kuwomba pang’ono kwa mphepo komwe kungawawuluze Iwo; palibe kachipembedzo kakang’ono, kapena chirichonse, chiti chiwawuluze Iwo; palibe chizunzo chaching’ono chiti chiwawuluze Iwo: Iwo alondoleredwa ku malo! Iwo amenya pamenepo, nawonso. Ndiyeno Mulungu, pamene Iwo amenya pa malo amenewo,

Mulungu adzawatsimikizira Iwo, “Molunjika!” Uh-huh, ndendende zomwe Iye ananena kuti Iye adzachita. Apa izo ziri mu Malemba, izi, “PAKUTI ATERO AMBUYE, ‘Izo zidzafika pochitika!’” Apa izo ziri. Mukuona? Ndizimenezotu.

²⁶⁶ Tsopano, Mulungu anali asanaziwulule izo mwa njira Yake yoperekedwa. Kotero iwo anapita kuti akazichite izo kunja kwa Mawu Ake, ndipo kunja kwa nyengo, chimodzimodzi basi monga iwo achitira tsopano. Pamene anthu, ziribe kanthu mowonamtima bwanji, anayesa kuti amuchitire Iye ntchito kunja kwa njira Yake yoperekedwa, iwo nthawizonse amazisokoneza izo. Monga Balamu, Balamu ankaganiza kuti iye anali kumuchitira Mulungu ntchito.

²⁶⁷ Kodi inu mukuganiza kuti Mulungu amanama? Kodi Mulungu amasintha konse maganizo Ake? Chabwino, anthu lero amachita ngati Iye anatero. Pamene Iye ananena kuti akazi asamamete tsitsi lawo, iwo amati, “Ife tikhoza kumalimeta ilo, Dr. *Wakuti ndi wakuti* anati ife tikhoza. M’bale *Wakuti ndi wakuti* anati ndiwe wamalingaliro operewera kwambiri.” Uh-huh, uh-huh. Mukuona?

²⁶⁸ “Chabwino, kodi *izi* zikhoza kuchitika? *Izi* zimachitika?”

²⁶⁹ “Eya, uh-huh, *Wakuti ndi wakuti* ananena chomwecho.”

²⁷⁰ Mulungu samasintha malingaliro Ake.

²⁷¹ Kodi inu mumakhulupirira kuti Balaamu anali mneneri? Baibulo linati iye anali. Kodi inu mukukhulupirira kuti iye anali mneneri? Tsopano, kumbukirani, Balaki anabwera kwa iye ndipo anati, “Pita ndipo ukawatemberere anthu awa, pakuti iwo onse ali pa nkhope ya dziko lapansi. Iwo siali nkomwe chipembedzo, siali fuko, iwo basi ndi gulu lomwazikana; ndipo ife ndife olemekezeka a mdzikolo. Tsopano iwe upite kumeneko ndipo ukawatemberere anthu amenewo, ndipo ine ndidzakulipira iwe chifukwa cha zimenezo.”

²⁷² Ndipo Balaamu anachita ndendende zomwe mneneri ayenera kuchita, iye anati, “Ine sindipita. Inu ingodikirani apa, usiku wonse, mundilole ine ndiwone chimene Mulungu anganene kuti ndichite.”

²⁷³ Kotero iye analowa, anati, “Ambuye, pali anthu ena kunja kuno ndi ine amene abwera, akufuna kuti ine ndipite uko ndi ukawatemberera anthu ena kumeneko.” Anati, “Kodi Inu mukufuna kuti ndichite chiyani pa izi?”

²⁷⁴ Mulungu anati, “Usapite, pakuti iwo ndi anthu Anga!”

²⁷⁵ Balamu anatuluka, anati, “Bwererani kunyumba kwanu. Ine sindingapite nanu, Mulungu wandiuza ine kuti ndisachite izo.” Tsopano, pali Mawu apachiyambi a Mulungu: “Usapite!”

²⁷⁶ Chabwino, ndiye iwo anabwerera, anati, “Inu mukudziwa, bishopu wanu sanemvere.”

²⁷⁷ “Chabwino,” mfumu inati, “ndikuuzeni zomwe ife tichite. Iye akusowa ndalama pang’ono, ine ndikukhulupirira izo zikhoza kumukopa iye. Kapena mwinamwake ine ndimupanga iye kukhala mkulu wampingo wa chigawo, mwinamwake ine ndimupezere iye chinachake chachikulu choti azichita. Ine ndikhoza kumupanga iye bishopu, inu simungakhoze kudziwa chimene ine ndingachite. Pano, ine ndikuwuzani zomwe ine ndingachite. Anthu inu mulibe maphunziro okwanira kuti mumukope iye mulimonse; ma *zake* anu ndi *ma ayi*, ndi *tote* ndi *funa* ndi *tenga*, siali olondola. Iye sakanamvetsera kwa inu, ife titumiza gulu lophunzira kwenikweni kumeneko, olemekezeka kwambiri.”

²⁷⁸ Iwo anapita kumeneko, anati, “Dokotala Balamu, *Dokotala* Balamu, moni kwa inu. Ndakubweretserani moni wochokera kwa mfumu.”

²⁷⁹ “Mmawa wabwino, abale.” Mukuona?

²⁸⁰ “Tsopano, Dokotala Balamu...” Ndipo, oh, mawu, momwe iwo anatsanulidwirapo kwenikweni. Ndipo anati, “Tsopano, amfumu anena kuti adzakukwezani inu, ndipo iwo adzakupatsaninso ulemu wawukulu. Ndipo, inu mukudziwa, iwo anakupatsani inu ndalama zochulukira *chotere* kuti mutenge udindo umenewu, koma amfumu akuti azichulukitsa izo katatu, kanayi kuchulukitsa katatu, ngati inu mungangobwera kuti mudzatenge izo.” Ndiye, Balamu anamva kuyabwa manja, ngakhale. Iye anapeza malingaliro opusa ndipo iye anatakasa malingaliro ake.

²⁸¹ Tsopano, kumbukirani, iye anamuyitanira Mulungu pa izo, wodzozedwa, koma iye anamutakasa Mulungu pomwepo kuchokera ku dongosolo lapachiyambi. Ndipo ndicho chimodzimidzi chimene Pentekoste yachita! Kuti mukhale otchuka, inu a Umodzi, inu a Utatu, chifukwa cha kutchuka munapanga chipembedzo kuti mukhale osiyana, inu munapanga bungwe ndipo ndinu akufa! Inu simudzawukanso. Koma, inu mukuona, inu mukanayenera kukhala ndi a Mulungu apachi-...Iye anakutulutsani inu mu Gulu limenero kuti akupangeni inu anthu, koma inu munapanga bungwe ndipo munabwereranso m’masanzi omwewo amene (ndikhululukireni ine) munatulukamo, zinthu zomwezo zimene inu munatulukamo, “Monga galu amapita ku masanzi ake ndi nkumba ku matope ake.” Pepani kuti ine ndinanena zimenezo, mundikhululukire ine, si zolondola pa nsanja pano. Mwaona? Ine ndinangonena zimenezo mu thupi. Zindikirani tsopano a...ndi chimene ine ndikutanthauza, kusanza. Ine ndikanayenera kunena izo monga choncho. Mawuwo anali onse olondola, koma anangogwiritsidwa ntchito molakwika. Mukuona? Iwo anagwiritsidwa ntchito molondola, koma anangomveka molakwika, inu mukudziwa. Masanzi, “Monga galu amabwerera ku masanzi ake.”

282 Ngati a Assemblies of God, General Council, anapanga bungwe Chipentekoste poyamba ndipo anawatengera iwo mmenemo kuti iwo asakhoze kuvomereza mavumbulutso, kodi inu simukudziwa, a Umodzi, inu munachita chinthu chomwecho? Inu mungakhoze bwanji kulandira Uthenga wa “mbewu ya serpenti, chitetezo Chamuyaya,” ndi zinthu zina izi zomwe zabwerapo? Ndinu omangirizika kwambiri ku bungwe mpaka inu simukulola nkomwe Iwo kuti ulowe pakhomo panu, uh-huh, uh-huh, chinthu chomwecho chimene Balamu anachita. Koma Mulungu sanasinthe malingaliro Ake.

283 Choncho Balamu anapita ndipo anati, “Ambuye, tsopano taonani, ine ndiri nawo mwayi kwenikweni tsopano kuti ndikhale winawake. Inu mukudziwa ndakhala ndisali kanthu, koma ndinali ndi mwayi wokhala winawake. Inu mukuti chiyani za izo tsopano, Ambuye?” Tsopano, iye sanene konse zimenezo! Iye ankadziwa ndendende zomwe Mulungu anati achite!

284 Chomwechonso aliyense wa inu amene anabatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” pa nkhani zina izi za Baibulo zomwe zikuyenera kukhala mu tsiku lino, inu mumadziwa choti muchite pa Izo, ndi kuzilandira Izo! Pamene inu mumuwona Mulungu akutsimikizira poyera “Ndi Choonadi,” ameneyo ndi Mulungu akutanthauzira Mawu Ake Omwe. Koma kodi inu mungachite izo? Ayi, bungwe lanu silingakuloleni inu kuti muchite zimenezo!

285 Ambiri a atomiki uko mu Tucson amene akumvetsera mmawa uno. M’bale Gilmore, ine ndiribe kanthu kotsutsana nanu; M’bale Brock, First Assembly, ndi mpingo wa Friendly. Amuna inu, ine ndinali kumeneko nthawi yonseyo, inu simukanandilola ine ngakhale kuti ndilowe. Ine. . .Ndithudi, inu simungathe, inu simungathe ndi kukhala chimene inu muli. Inu simungakhoze kuvomereza vumbulutso, chifukwa ndinu achipembedzo. Ndipo mvetserani, monga momwe Uza anaphedwa chifukwa anali pansu pa kudzoza kwabodza kumeneko, momwemonso Akhristu owona ambiri akutaya chowachitikira chawo kumbuyo uko mu zipembedzo zakale zakufa zimenezo, chifukwa iwo akuyika dzanja lawo pa Likasa pamene sanadzozedwe kuti achite chomwecho. Tsopano inu mukhoza kuzikhulupirira Izo, kapena kusazikhulupirira Izo, izo ziri kwa inu. Mulungu ndi Woweruza wanu. Mulungu sanabweze konse Mawu Ake. Zimene Iye ananena nthawi yoyamba, Iye akuzinena nthawi iliyonse.

286 Iye anamuza Balamu, “Usapite!”

287 Ndiyeno Balamu anabwerera, anati, “Koma Ambuye, ine ndingapite?”

288 Tsopano taonani! Mulungu anati, “Pita!” Tsopano, Iye anamupatsa chilolezo kuti apite. Pali chifuniro chongololera cha

Mulungu, ndipo osati chifuniro chapachiyambi cha Mulungu. Inu mukuona vuto lomwe iye analowamo?

²⁸⁹ Ndipo munthu aliyense yemwe amanga chirichonse, bungwe lirilonse, kapena chirichonse kunjira kwa Mawu a Mulungu, ndi mchanga wogwedezeka ndipo chidzagwa! Ichochidzafa motsimikiza monga chirichonse, chifukwa Mawu a Mulungu ndi Thupi lomwe likukula la Mkwatibwi. Inu simungakhale nalo Ilo lonse ngati phazi, lonse mkono, lonse ntchafu. Zinthu izi zimabwera munyengo yake.

²⁹⁰ Ndipo Pentekoste, inu munalipanga ilo lonse chinthu chimodzi, chotero inu simungakhoze kuvomereza vumbulutso latsopano. N'chifukwa chake inu mumakhala pomwe inu muli ndi kufa. Ilo limasunthira patsogolo. (Mochuluka kwambiri; sindikufuna kuti ndikutopetseni inu.) Koma Mulungu samasintha malingaliro Ake, chiganizo Chake choyamba ndi cholondola ndendende. Kotero Mulungu samasintha malingaliro Ake, Iye amangokulolani inu kupitirira mu chifuniro chanu chongololera. "Mulungu ndi Mulungu wabwino," monga Oral Roberts amanenera. Iyenso ndi Mulungu woopsa!

²⁹¹ Onani, monga inu mumanenera, "Ulemerero kwa Mulungu, ine ndikufuna kuyankhula ndi malirime!" Iye amakulolani inu kuti muchite zimenezo, koma chimenecho si chizindikiro choti muli nawo Mzimu Woyera.

²⁹² Mukukumbukira zomwe Tomasi ananena, wokayikira wakaleyo? "Pokhapokha nditakhala ndi umboni wina, ndiyenera kupisa zala zanga m'misomali Yake, manja Ake, ndi mu nthiti Mwake, ine—ine—ine—ine sindikhulupirira nkomwe Zimenezo." Tsopano, ndi inu apo, chinthu chomwecho.

²⁹³ Yesu anati, "Ndi ili, Tomasi, lowetsa manja ako mmenemu ndiye ngati ndizo zomwe iwe ukufuna kuti udziwe." Mwaona? Mwaona? Tsopano, ngati inu mukufuna njira ya Tomasi, pitirirani. Koma kodi Iye ananena chiyani? "Ndi yopambana bwanji mphotho yawo amene sanawone komabe akukhulupirira."

²⁹⁴ Zindikirani, zindikirani, pa kuchita izi, iye anapangitsa imfa ya munthu woonamtima, kuyika dzanja lake pa likasa pamene iye samayenera kuchita izo. Munthu wamkulu, woonamtima, amaganiza kuti kudzoza ndi chirichonse chinali cholondola basi, koma likasa linali likupita mu njira yake yolakwika. "Ng'ombe," Baibulo linati, "zinapunthwa," osati Alevi. Ng'ombe zinapunthwa, ndipo ngoloyo inapendekeka; ndipo munthu woonamtima, ndi mtima wake wodzala ndi chikondi, anayika dzanja lake pa likasa kuti alibwezeretse ilo, ndipo anakanthidwa nkufa chifukwa panalibe munthu akanakhoza kulikhudza likasa limenero koma Mlevi. Mukuona momwe Mulungu amasungira Mawu Ake, amasunga mpita Wake, amasunga dongosolo Lake? Uziya anakanthidwa ndi khate. Apa pali Davide, onse

pamodzi anapangitsa imfa ya munthu, ndi ngozi yayikulu; pokhala odzozedwa ndi Mzimu, onse a iwo, koma kuchoka mu mpita wa Mulungu. Ndi kulondola uko? Iye anafa. Oh, izo zinamuwopsyeza Davide pafupi kufa, izo zinatcha—dzina la malowo, monga M'bale Jack anawerenga izo. Mukuona? Iye anamuyika chizindikiro pamenepe.

²⁹⁵ Ndi kangati kamene zipembedzo zachita chinthu chomwecho kwa okhulupirira owonamtima. Mpingo wa Katolika, Methodist, Baptisti, mpingo wa Khristu, ngakhale Achipentekoste, apangitsa imfa zambiri zauzimu ndi chinthu chomwecho. Pamene Iwo unabwera, ndi zinthu izi, iwo anapeza. . . ndipo iwo sangathe kupitirira, chifukwa ndicho chimene chipembedzo chawo chimakhulupirira.

²⁹⁶ Yang'anani lero, misonkhano yokopa yayikulu, chinthu chomwecho. Siimachita kalikonse koma kuwapanga iwo “mwana waku gehena wofutukuka pawiri, oyipa kuposa momwe iwo analiri poyamba.” Zimawapangitsa iwo kulimba, kwenikweni, kubwera ku Choonadi. Kukhala nacho chimodzi cha zitsitsimutso zazikulu izi, ndipo onse a iwo amalowa mkati, nkumapitirira kwa kanthawi pang'ono, ndi kubwerera kunja ndipo iwo amayamba tchimo lonse ili kachiwiri. Kumva za chitsitsimutso china, nkuti, “Ah, ine ndinali ndi zina za zinthu zimenezo, ine ndinayesetsa. Palibe kanthu kwa izo.” Mukuona? Iwo sakuwudziwa mpitawo. Sakuwona.

²⁹⁷ Ine ndinamumva mlaliki wathu wamkulu Billy Graham, atakhala mmawa wina pa kadzutsa monga chonchi, ndipo anati, “Ine. . .” Apa, iye akuyika Baibulo, mu Louisville, Kentucky, anati, “*Apo* pali chitsanzo cha Mulungu.” Ndipo izo nzoona, mwamunayo ananena zoon. Iye anati, “Inu pitani. . . Paulo analowa mu mzinda ndipo anali ndi wotembenuka mtima mmodzi, nkudzabwerera chitatha chaka kuchokera pamenepe ndipo anali ndi sarte kuchokera kwa wotembenuka mtima ameneyo.” Anati, “Koma ine ndimapita mu mzinda, ndipo ndimakhala nawo otembenuka mtima sarte sauzande, ndi kudzabwerera mmiyezi sikisi ndipo sindimawapeza okwanira sarte.” Iye anati, “Kodi mukudziwa chomwe chavuta?” Anati, “Inu alaliki aulesi,” anati, “inu mumakhala mozungulira ndi phazi lanu pa desiki ndi—ndi kumawayimbira anthu awa foni m'malo mowayendera ukatha mgonero ndi kumayankhula kwa iwo.”

²⁹⁸ Oh, mtima wanga umatentha. Ine ndinaganiza, “O munthu wamkulu wa Mulungu, ine ndikudana nazo kuti ndisagwirizane nanu apa, koma kodi ndani anali alaliki aulesi pa wotembenuka mmodzi wa Paulo? Zomwe iye anachita, anamutengera iye mu Mawu, anamutengera iye mu Uthenga, anamutengera iye kumene anamupeza Mulungu; mtima wake unayaka moto, analiyika dzikolo pamoto! Ndipo chinthu chokhacho chimene inu mumachita ndi kuwayika iwo mu mpingo wa Baptisti

kapena wa Methodisti, kapena chinachake, nzosadabwitsa palibe chinthu choti chiyake.” Uh-huh. Inde, bwana!

²⁹⁹ Ndiye taonani zomwe Mawu alonjeza lero. Tiyeni tipeze ngati chiri Methodisti, Baptisti, Achipentekoste, kapena chiyani, kwa lero. Tsopano inu mukhoza kupita kuti mukawerenge Malemba anu. Tengani Malemba awa omwe ine ndakhala ndikuwabwereza kwa inu. Komanso Chivumbulutso...

³⁰⁰ Ndikanakhala ndi nthawi, ine ndikanawerenga zimenezo, koma ine basi ndiribe. Ine ndiri nawo pafupifupi maminiti thwelofu kapena fortini. Ndiyenera kuti nditseke pa nthawi yake, pa leveni, ngati ine ndingalondole.

³⁰¹ Zindikirani Malaki 4, Chivumbulutso 10, Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Kodi Baibulo silinanene... Tsopano penyani! Panali Mngelo, Mthenga wochokera Kumwamba, ndi mthenga wapadziko lapansi. Ndipo mthenga aliyense anali wa m’badwo wa mpingo. Iye anati, “Mmasiku...” kuyankhula tsopano, “panadza Mngelo, Mthenga” (mawu oti *mngelo*, mawu a Chingerezi amanthauza “mthenga”). “. . . anatsika kuchokera Kumwamba, ndipo Iye anayika phazi Lake pa mtunda ndi panyanja, ndipo analumbira pa Iye wokhala ndi moyo kwanthawizonse kuti nthawi sidzakhalaponso.” Ndi kulondola uko? Utawaleza utazungulira mutu Wake, ndi zinthu zonse izi zikungochitika. Mngelo ameneyo anali Khristu! Ndithudi! Koma kodi Iye ananena chiyani? “Koma m’masiku a mngelo wachisanu ndi chiwiri, m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri.”

³⁰² Nthawizonse ndi kumapeto kwenikweni kwa m’badwo wa mpingo kumene iwo amachipanga chinthucho mochuluka... zachipembedzo kusokonezeka kwambiri mpaka Mulungu amatumiza mthenga, ndipo umenewo ndi Uthenga kwa m’badwo wa mpingo umenewo. Ndiye iwo amatenga uthenga wake, chifukwa iye anangokhala moyo kanthawi pang’ono, ndipo Mulungu... ndiye iwo amatenga uthenga wake mmalo mowunyamula iwo ndi zina zonse a Iwo, iwo amapanga chi—chipembedzo. Ndiyeno iwo anabwera kuti adzapange chipembedzo china; mthenga wina, kutenga winanso.

³⁰³ Inu nonse munazona mu bukhu langa, izo zonse zidzajambulidwa mu *Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo*, imene Iye anandiiza ine; imene ndayima nayo monga mboni kwa Mulungu kuti ndidzaweruzidwe pa Tsiku la Chiweruzo chifukwa cha Iyo. Izo zinachokera kwa Mulungu, osati kuchokera mmalingaliro anga. Zindikirani, apa. Ine ndinaganiza—ine ndinaganiza mosiyana ndi izo, ngati ndikanati ndikhale ndi lingaliro langa langa. Monga M’bale Jack anandiuzira ine za Mngelo kumeneko, momwe kuti “Khristu ameneyo anali thupi laulemerero.” Koma izo sizinali, zinkasonyeza kuti Uthenga kukhala wolondola, Umulungu Wapamwamba, Iye

anali Mulungu. Mukuona? Chinthu chomwecho basi chimene ine ndinakhala ndikulalikira kuchokera mu Mawu. Mawu nthawizonse amachitira umboni za Mawu.

³⁰⁴ Tsopano, mwamsanga tsopano, pamene ife tikukonzekera kuti titseke mu mphindi zochepa.

³⁰⁵ Tsopano, Iye anati, “M’masiku a Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, mngelo wapadziko lapansi, m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, ndiye zinsinsi zonse izi zomwe zatayika mmbuyo kudutsa m’mibadwo isanu ndi umodzi iyi ya mpingo ziyenera kuwululidwa panthawi imeneyo.” Chabwino, ndizo ndendende zomwe Angelo amenewo ananena. Apa pali Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, kapena kutsegulidwa kwa zinsinsi izi. Ndipo inu mumayesera kuti muzitengere Izo pamaso pa zipembedzo zimenezo. Zosiyana ndi zomwe iwo. . . M’bale, iwo amadzitsekera ngati nkho, koma iwo nthawizonse akhala akuchita izo. Koma ndi nyengo!

³⁰⁶ Ndi angati akudziwa kuti uwu ndi m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] M’badwo wa Laodikaya, wofunda umene Mulungu amawulavula kuchokera mkamwa Mwake. Ndipo iwo amamulavula Mulungu kutuluka m’kamwa mwawo; kulibe m’badwo wina mu Baibulo kumene Yesu anapezeka kunjira akuyesetsa kugogoda, kuti abwerere mkati. Iwo anamutulutsa Iye kunjira, popanda mgwirizano. Kodi Yesu ndi ndani? Mawu! Mawu anatulutsidwa kunjira. Mankhusu anaponyera tirigu kunjira! Iye anati, “Ine ndayima pakhomo ndipo ndikugogoda, ndipo munthu aliyense m’maunyolo awo kunjira uko adzamva Liwu Langa.” O Mulungu, tichitireni chifundo!

³⁰⁷ Zinali pa nthawiyo, pamene munthu ameneyo anafa, kuti Davide ndi kudzoza anawona chimene iye anali atalakwitsa. O Davide, iwe m’busa, kodi iwe sungakhoze kuwona tizikhulupiro tako takufato ndi zipembedzo zomwe iwe wagwiritsitsako? Kodi simukuwona zomwe chikuchita? Chikumupha Uza. Wakufa mwauzimu, ndipo inu mumadabwa nchifukwa chiyani kulibe chitsitsimutso; kuwalola akazi anu kumeta tsitsi lawo, kupenta nkhoze zawo, kuvala akabudula; kumawatumiza anyamata anu kutali ku sukulu za ma *ricky*, ndi zina zotero monga choncho, kumene theka la iwo amabwera kunyumba okwatirana amuna okhaokha, ndi chirichonse.

³⁰⁸ Zindikirani cholinga cha Davide: iye anali kubweretsa likasa ku nyumba kwake *komwe*. Limenero silinali likulu, amenewo sanali malowo, ilo linali la mu Yerusalemu. Koma Davide ankaliweretsa ilo ku nyumba yake yomwe, iye ankafuna kuti chitsitsimutsocho chikhale pa chipembedzo chake chomwe. “Oh, ngati ndinu wa Assembly, chabwino. Ngati ndinu wa Oneness, chabwino. Ngati ndinu wa Chipentekoste, chabwino.”

309 Monga wina anati, anati, “M’bale Branham, kodi inu mungamupangitse bwanji aliyense kuti azimvetsera kwa inu?” Anati, “Ine ndikukhoza kumuwona Billy Graham, iye ali nacho chipembedzo chirichonse mu dzikoli limodzi naye. Ine ndikukhoza kumuwona Oral Roberts, wa Chipentekoste aliyense amakhala pafupi ndi iye. Koma,” anati, “inu mumatsutsana ndi chinthu chonsecho.” Uh-huh. Anati, “Kodi mu dziko inu mumapeza bwanji aliyense?”

310 Ine ndinati, “Ndi Mulungu!”

311 “Ine Yehova ndinawudzala iwo asanayikidwe maziko a dziko lapansi. Ndidzawuthirira iwo usana ndi usiku pokhapokha ngati ena mwa iwo atawuchotsa iwo mu dzanja Langa,” Yesaya. “Ine ndidzawuthirira, Ine ndinawudzala iwo. Ine ndinayika maina awo pa Bukhu asanayikidwe maziko a dziko lapansi, mwa kukonzedweratu. Ndidzawuthirira iwo, mudzingopitirira kumayenda. Ine ndiwaza madzi, inu muzingowupopera Iwo.” Kumondola. Mukuona? “Ndidzathirira iwo usana ndi usiku pokhapokha ngati umodzi wa iyo utachotsedwa mu dzanja Langa.” Ndzimenezotu.

312 Ankafuna ilo libwere ku mzinda wa Davide, mmalo mwa Yerusalemu. Panalibe malo okonzedwera ilo pa nthawi imeneyo, ndipo chimodzimodzinsu lero. Zinsinsi zazikulu izi zomwe zafutukulidwa ndi Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, mulibe malo mu chipembedzo chirichonse... akanayenera kusiya kukhala chipembedzo kuti awatenge Iwo. Njira yonse kuchokera kwa Luther kupitirira mpaka ku Pentecostal Oneness, palibe malo angakhoze kuwalandira Iwo. Ngakhalenso munthu sangakhoze kuwalandira Iwo ndi kumakhala mu chipembedzo chake. Iye adzayenera kutsatira tirigu kapena kupita ndi mankhusu, chimodzi chomwe iye akufuna kutero.

313 Khristu ndiye Likasa lathu, Mawu. Iwo akufuna chipembedzo chawo. Iye sangakhoze, zindikirani, sanganyamulidwe pa ngolo zatsopano za chipembedzo, Uthenga wake sungapite pa ngolo ya chipembedzo chatsopano pamene Iwo ukuyenera kuti unyamulidwe ndi kubwera pa mtima wa mneneri. Iwo sungatero. Iye analonjeza izo, Izo zikanakhala motero, ndipo umo ndi momwe Izo ziyenera kukhalira.

314 Chotero chipembedzo sichidzawulandira konse Iwo, ngakhalenso iwo sangakhoze kuwulandira Iwo. Ndipo iwo angochititsidwa khungu kwa Iwo monganso Ayuda analiri pamene iwo anamupachika Yesu pa mtanda, pamene Yesu anati, “Atate, akhululukireni iwo, sakudziwa nkomwe chimene iwo akuchita.” Musawanyazitse iwo, koma tangoganizani: pakuti bwanji ngati inu munali mu chikhalidwe chomwecho ndi maso anu akhungu kotero kuti inu simungathe kudzuka ndi kuwona chimene chikuchitika?

³¹⁵ Ngakhalenso iwo sakanakhoza kuwona kuti Ameneyo anali Mulungu wawo yemwe. Pamene Iye anali atapachikidwa pamenepo pa mtanda, ndipo iwo akuyimba Salimo la 22 mu kachisi, pa mtanda wa mayadi thuu handiredi, “Mulungu Wanga, Mulungu Wanga, kodi Inu mwandisiyirani Ine? Iwo alasa mapazi Anga ndi manja Anga.” Mukuona? “Mafupa Anga onse, akundiyang’ana Ine. Mwandisiyirani Ine?” Ndipo pamenepo, Mulungu yemweyo amene anali atayimba za iye, akhungu mokwanira mwakuti anamukhomera Iye pa mtanda, ndipo sanadziwe izo.

³¹⁶ Tsopano, kodi Baibulo silimanena kuti mpingo wa Laodikaya, umene umaganiza kuti ndi wawukulu kwambiri mwa mamembala ake achipembedzo, iye akanadzakhala “wamaliseche, womvetsa chisoni, wosauka, wakhungu, ndipo osadziwa izo”? Kodi *akhungu* amatanthauza chiyani? *Akhungu* amatanthauza kwa mpingo wa Laodikaya uwu monga zinachitira pakutha kwa mpingo wa Chiyuda, akhungu kwa Khristu yemweyo amene anamuyika kunja, akugogoda, akuyesera kuti alowe mkati; “wamaliseche, womvetsa chisoni, wosauka, watsoka, wakhungu, ndipo osadziwa izo.” O Mulungu, tichitireni chifundo!

³¹⁷ Bwanji tirigu sakukhala mu Kukhalapo kwa Mwana ameneyo kumeneko, ndi kuwona ora limene ife tikukhalamo? Inde, Khristu ndi Likasa lathu, koma njira Yake yapachiyambi yochitira izo. Ndiye ndi Uyu apa... Iwo anali nawo Mzimu Wake chabwino, ife tikudziwa zimenezo. Iwo amayembekezera pa Ambuye, kuwona dongosolo Lake pa Mawu Ake apachiyambi mu nyengo Yake kuti atsimikiziridwe, ndi zomwe ife tiyenera kuchita pakali pano. Ndipo Iye—Iye amawulula chikhulupiriro chawo mwa Mawu Ake, kumuwona Iye akutsimikizira dongosolo lililonse limene Iye analonjeza, osati madongosolo a munthu a chipembedzo, osati kuwapanga mamembala chifukwa cha likasa lathu lomwe.

³¹⁸ Iwo ali nalo likasa la Methodisti, likasa la Baptisti, likasa la Presbateria, aliyense akulowa mu likasa ili ku chisautso chachikulu chikubwera; “Ulemerero kwa Mulungu! Ine ndinabatizidwa mu likasa la Methodisti, Chipresbateria, likasa la Chipentekoste.” Pali Likasa limodzi lokha, ndiye Yesu Khristu, ndipo Iye ndi Mawu!

³¹⁹ Zindikirani, Mulungu anamuza mneneri, anati, “Idya mpukutuwo,” mu Chipangano Chakale. Mneneri wa Chipangano Chatsopano, Iye anati, “Idya kabukhu kakang’onoko.” Chifukwa chiyani? Kutu mneneri ndi Mawu akhale mmodzi! Mukuona? Ndilo Likasa, Mawu a Mulungu.

³²⁰ Mulungu analonjeza, Mawu Ake, momwe Iwo akanati adzakwaniritsidwire ndi momwe Iwo akanati adzafike pochitika pamene Iye anasankha Mkwatibwi Wake, mmene

izo zikanadzachitikira. Izo zikuchitika pamaso panu pomwe, mu Dzina la Ambuye, ndipo izo ndi mwa Mawu apachiyambi! Uthenga wa nthawi yakumadzulo uli pano.

³²¹ Ndi angati amamukumbukira Haywood pamene iye analemba:

Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo,
Njira ya Ulemerero ndithudi mudzayipeza.

³²² Inde, lonjezo lakumadzulo la Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, la Chivumbulutso 10, Malaki 4, Luka 30 ndi 10. Werengani Deuteronomo 4, 4:1 ndi 4, kenako ndime ya 25 ndi 26, ndipo muwone zomwe Iye ananena za tsiku lotsiriza ili. Uyu anali Mose akunena kwa Israeli “sungani Mawu aliwonse, inu musawonjezere chinthu chimodzi!” Mose, mneneri ameneyo anali atakhala kumeneko ndipo anawawona Mawu a Mulungu amenewo. Ndipo Iwo analembedwa kwa iye ndi kutsimikiziridwa ndi dzanja la Mulungu Lomwe likuwalemba Iwo. Iye anati, “Inu musunge Mawu aliwonse, musawonjezere chinthu chimodzi kwa Iwo kapena kuchotsapo chinthu chimodzi kwa Iwo.” Inu mukhoza kuwerenga izo mu ndime ya 25 ndi 26 ya Deuteronomo 4.

³²³ Zindikirani! Inu musawonjezere kwa Iwo, musachotsere kwa Iwo; chifukwa ngati inu mutero, Mulungu adzachotsa gawo lanu kuchokera mu Bukhu la Moyo. Ndipo izo zimasonyeza kuti inu simunali mbewu Yake.

³²⁴ Kumbukirani! Chirichonse chimene Mulungu watilonjeza ife, chirichonse chimene Mulungu wayankhula kwa ife, chirichonse chimene chinanenedwa kwa inu mu Dzina la Ambuye, icho chachitika! Mulungu sanapange konse lonjezo limodzi kukhala lopanda kanthu, koma Iye wasunga lonjezo lirilonse limene Iye ananena, watiuza ife, lakhala Choonadi. Kwa zaka twente izi, Shreveport, Ine ndalalikira kwa inu kudzera mu mphamvu ya Mulungu, ndi chilolezo cha abusa anu, ndipo ine ndikutengerani inu kuti mulembe lero. Ngakhale kwa akazi amene anadutsa pobereka; amuna, ana, kusautsika, machiritso, uneneri, zinthu zimene zikanadzachitika, palibe chimodzi cha izo chinalepherapo! Tsopano, khalani kutali ndi zipembedzo zimenezo, izo zikukutsogolerani inu ku imfa.

³²⁵ Samueli anayimirira tsiku lina, ndipo iwo anati, “Ife tikufuna mfumu, ife tikufuna kukhala ngati dziko lonse lapansi.”

³²⁶ Iwo...Samueli anati, “Musaitenge mfumu imeneyo. Iye adzatenga ana anu aamuna, ndi aakazi, ndipo iye adzachita izi ndi kuchita izo.”

³²⁷ Iye anati, “Inde, ine ndikudziwa kuti mukulondola.”

³²⁸ Koma Samueli anati, “Mvetserani kwa ine. Kodi ine ndinatengapo ndalama zanu? Kodi ine ndinakupemphanipo

chakudya? Kodi ine ndinakuwuzanipo kuti mumayenera kundipatsa ine malipiro ochulukirapo kuti ndikupangireni msonkhano?” Tsopano dziweruzeni nokha, ngakhale tsopano! Mukuona? Iye anati, “Kodi ine ndinayamba ndakuwuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye kupatula chimene chinafika pochitika?” Palibe chinthu chimodzi.

³²⁹ “Oh, inde, Samueli, iwe sunatipemphe konse ife ndalama, iwe sunafune zinthu zazikulu. Samueli, izo nzoona, ndipo chirichonse chimene iwe unatiuza ife mu Dzina la Ambuye chinachitika. Koma, Samueli, ife tikufuna chipembedzo chathu mulimonse!”

³³⁰ “Ndiye pitani mukachitenge icho. Ziri kwa inu.” Uko nkulondola.

³³¹ Inu mukhoza kuganiza kuti mukumuchitira Mulungu ntchito, ndipo ngati inu mukutuluka mu njira ya Mulungu yochitira izo, inu mupitiliza kuzisokoneza izo, mopitirira ndi mopitirira. O Mpingo wa Mulungu wamoyo! Chonde khululukirani njira yanga ya chi Irish komanso nthabwala zanga, koma mu kuwonamtima ndi kupatulika kwa mtima wanga, inu a Assemblies of God, inu a Oneness, a Presbateria, a Methodist, chirichonse chimene inu muli, thawani kuti mupulumutse moyo wanu. Kumbukirani, chokani kumeneko.

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka,
(Kukonzekera otsalira amenewo.)

Zizindikiro zomwe aneneri ananeneratu;
Masiku achipembedzo akuwengereka, ndi
zopsyinja zikuchuluka,
“Bwererani, O omwazika, kwanu.”

Tsiku la chiwombolo layandikira,
Mitima ya anthu ikulephera ndi mantha;
Dzazidwani ndi Mzimu Wake, konzani nyali
zanu ziwale,

Yang’anani mmwamba! chiwombolo chanu
chayandikira.

³³² Kodi mukukhulupirira zimenezo? Ife tiri pa nthawi yotsiriza, ife tiri pano. Cholembedwa chiri pa khoma, Kudza Kwachiwiri kwayandikira, Mkwatibwi akusankhidwa, akuthiriridwa, akutulutsidwa.

³³³ Tsopano, izo sizikutanthauza kutulutsidwa mu mpingo, izo zikutanthauza kutulutsidwa ku zachipembedzo. Inu muyenera kumapita ku tchalitchi, koma musajowine bungwe lililonse. Yesu anapita ndi mabungwe onse, koma Iye sanajowine konse limodzi la iwo. Ndipo sanatenge mbali ndi umodzi wa iwo, ayi ndithu, koma Iye anali pakati pawo. Apo ndi pamene Kuwala kumayenera kumwazikana. Ndipo inu mukhale pomwepo pamene inu muli, mukumwaza Kuwalako. Mwaona? Ndi chimene Mulungu akukugwiritsirani ntchito. Anthu a

mitima yanjala, aloleni iwo adziwe kuti Yesu Khristu ndi weniweni, mofanana basi monga Iye analiri dzulo, Iye ali lero; ndipo adzakhala kwanthawizonse.

³³⁴ Ndi zotheka, mwamuna kapena mkazi ndi kuwonamtima konse, kuyesetsa mmene angathere kuti amuchitire Mulungu ntchito, ndipo anazitakasa izo mnjira yolakwika. Ndi kudzoza koono kwa Mzimu Woyera pa iwo, koma anazitakasa izo mosiyana ndi dongosolo la Mulungu la m'badwowo, ndi kusokoneza chinthu chonsecho. Tsopano, ngati inu mukukhulupirira kuti ndicho Choonadi, nenani, "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Ife tangowerenga Izo. Kusokoneza chinthu chonsecho posabwera njira yoperekedwa ndi Mulungu yochitira izo.

Tiyeni ife tipemphere.

³³⁵ O mpingo, kuno ndi kuwoloka fuko lonseli, mvetserani kwa wantchito wanu wodzichepetsa mmawa uno. Kodi mutero? Yang'anani kumene inu munali zaka zingapo zapitazo pamene ichi chinkayamba poyamba; tsopano yang'anani zomwe otsanzira akhazikikapo pa izo, ndipo mamiliyoni aakulu ndi mabiliyoni a madola awulukira m'mabungwe. Mukuona? Akadali kutali ndi Mawu a Mulungu. Zimango ndi mabungwe si njira imene Mulungu amatakasira Mzimu Wake. Iye amawutakasa Iwo mpaka mu Mawu Ake, kuwapangitsa Iwo kukhala amoyo. Ndipo ngati inu munadzozedwa kuchokera ku chiyambi cha dziko lapansi ku Mawu amenewo, Mawu aliwone adzabwera pompo pamwamba pa Mawu. Monga kakhungu ka munthu sikadzakhala ndi kakhungu kamodzi kamunthu, ndipo kakhungu kotsatira ka galu, ndipo kotsatira kakhungu ka mphaka; ito tidzakhala timakhungu ta munthu. Koma payenera kukhala kakhungu koyambira. Ndi kulondola uko? Nenani, "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Chabwino, ngati kali kakhungu ka Mawu koyambira, timakhungu tina ta Mawu timadzozedwa kuti tikhale thupi lathunthu.

³³⁶ Musakhale ana, mu chikondi chabe, koma khalani amuna mu Mzimu ndi mu chiweruzo. Weruzani ngati ine ndakuuzani Choonadi kapena ayi. Weruzani ngati Iwo ali Mawu a Mulungu kapena ayi. Weruzani ngati ndi ora limene tikulikamba kapena ayi. Weruzani ngati zinthu izi zinalonjezedwa. Tsopano, kodi izo zatsimikiziridwa? Ndi zinthu zimene palibe munthu padziko lapansi amene angakhoze kuchita izo. Koma Izo zakhala zawamba kwambiri kwa ife mpaka ife tikuzilola Izo kutidutsa ife. Dikirani, mpingo, dikirani.

³³⁷ Ngati alipo mmodzi muno mmawa uno amene sakumudziwa Yesu Khristu, sakuyima wolungamitsidwa mmawa uno, machimo anu onse apita ngati kuti inu simunachimwepo, ndipo inu mukufuna kuti mukhale mwanjira imeneyo...chifukwa kumbukirani, tsiku lina, mwinamwake lero, mwinamwake

mu maminiti asanu otsatirawa, koma tsiku lina mtima umenewo udzayima. Ndipo wamkati mwa wamkatiyo adzatenga kuwuluka kwake kuti akayime mu Kukhalapo kwa Mulungu kuti aweruzidwe molingana ndi zomwe inu mukuchita ndi Uthenga uwu mmawa uno, molingana ndi Uthenga *uwu* umene inu mukuwuwona. Ayi. . . Si ine, ndangokhala choyankhulira chabe. Monga mayikolofoni awa, iwo sanganene kanthu pokhapokha ine ndikuyankhula mmenemo. Ndipo ngakhalenso ine sindinganene chirichonse pokhapokha ngati Mulungu akanayankhula kudzera mwa icho, koma inu mumaona Mulungu akuchitsimikizira icho kukhala Choonadi. Inu mukufuna kuti mukhale Mkhristu weniweni.

³³⁸ Tsopano, ife tiribe malo oyitanira kuguwa, koma pa gome pomwe inu mwakhala. Malowa ndi odzaza ndi opanikizana, asefukira. Ine sindingakuyitanireni inu ku guwa, palibe guwa pano loti ndikuyitanireniko inu. Koma guwa liri mu mtima mwanu. Kodi inu simungalole kukhudzika kwakung'ono kumeneko kuti “Yesu Khristu ndi weniweni” kusunthire pafupi lero ndi kuyitanira thupi Lake lonse kwa inu, kumusunga Iye mu mtima mwanu? Ngati Iye siali mmenemo, kodi inu mungakweze dzanja lanu, mwa chizindikiro kwa Iye, kuti, “Ambuye, ndidzazeni ine, ndidzazeni ine ndi Mawu Anu ndi Kukhalapo Kwanu, kuti ine ndikhoze kukhala moyo mwa Inu”?

³³⁹ Pamene mutu uliwonse uli woweramitsidwa, diso lirilonse liri lotsekedwa, kudutsa fuko lonse, kwezani manja anu apa mwa omvera owoneka ndi kunjira ukonso; ndipo ine ndikupemphererani inu. Ndizo zonse zomwe ine ndingathe kuchita, ine sindingathe kuwudzaza iwo. Mulungu akudalitseni. Ine sindingathe kuwudzaza iwo. Mulungu akudalitseni inu; ndi inu. Mulungu akhoza kuwudzaza iwo. Mulungu akudalitseni inu. Manja akukwera mmwamba apa mwa omvera owoneka, kulikonse. “Dzazani iwo. Ndidzazeni ine, O Ambuye. Ndidzazeni ine.” Ndipo tsopano, ine ndikatha. . . Zikomo inu, mlongo. Zikomo inu, m'bale. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikatha. . . Mulungu akudalitseni inu, mlongo wokonedwa. Inu. Ndikatha. . . Ine ndikuganiza tsopano ndagwira ochuluka owonamtima, akuyesetsa kuti akhale, ine ndikufuna kuti ndikweze manja anga ndi inu.

³⁴⁰ O Ambuye, musandilole ine kuti ndiyime njii. Mopitirira, Ambuye, mulole ine ndisayime pa chinthu chimodzi, ndiloleni ine ndizingopitirira, Ambuye, mpaka nditatsiriza chirichonse chimene Inu munandikonzera ine kuti ndichite. Mosasamala za mtengo, mosasamala mtengo wake, mosasamala za kutsutsidwa, mtandawo ndi wolimba bwanji, Ine ndidzakumbukira mtanda umene Inu munawusenza.

Kotero mtanda wopatulika uwu Ine
ndidzawusenza
Kufikira imfa idzandimasula ine,

Ndiye nkumadzapita Kwathu, kukavala
korona,
Pali korona kwa ine.

Kodi Yesu anyamule mtanda yekha,
Ndipo dziko lonse lizipita mwaufulu?
Ayi, pali mtanda kwa aliyense wa ana Ake,
Pali mtanda kwa ine.

³⁴¹ Wokonedwa Mulungu, Mawu ayankhulidwa. Iwo sangakhoze kubwerera opanda kanthu, Iwo adzapeza malo Ake penapake. Ngati mbewuyo inadzalidwa kale, Adzayithirira iyo mpaka itakula. Ndipo palibe angayichotsemo iyo mu dzanja Lanu, “Onse amene Atate anandipatsa Ine adzadza kwa Ine, palibe munthu angakhoze kuwachotsa iwo mu dzanja Langa. Atate Anga anawapereka iwo kwa Ine asanayikidwe maziko a dziko lapansi”; pamene madongosolo onse anajambulidwa, monga choncho, Yesu anapatsidwa Mpingo Wake, Mkwatibwi Wake.

³⁴² Chikwati chabodza cha dziko lapansi, kwa zipembedzo izi. Inu munabwera ndi kudzafa mu dziko lapansi, Inu munamuwombola Iye, Inu munamulungamitsa Iye, Iye sanachite konse izo kuyamba nkuyamba. Iye anakodwa mmenemo, wakhungu. Ndipo monga nyimbo imanenera:

Ndinali wotayika kale ndipo tsopano
ndapezeka,
Ine kamodzi ndinali mu Laodikaya,
wakhungu, koma tsopano ine ndikuwona.

Ndipo ndi chisomo chomwe chinaphunzitsa
mtima wanga kuchita mantha,
Chinali chisomo chinachotsa mantha anga;
Ndi mopambana bwanji chisomo icho
chinawonekera
Ora limene ndinayamba kukhulupirira!

Ndipo madzi a Mulungu anagwera pa moyo wanga. Ine ndinkawawuka.

³⁴³ Mulungu, pa guwa laling’ono ili la mtima uliwonse womwe uli pano ndi kuzungulira fukoli, mulole madzi otuluka pansu pa guwa la Mulungu atumphukire mmawa uno pa Mpingo Wanu; ndi kuwuthirira Iwo, Ambuye, pakuti nyengo yatsala pang’ono kutha. Upatseni Iwo Moyo, Madzi a Moyo, kuti Iwo ukhoze kugona mu Kukhalapo kwa Mwana kuti ukhwime kwa nkhekwe Yanu yayikulu.

³⁴⁴ Atate, ine ndikuwapempherera Iwo. Koma phesi liyenera kuwuma, kotero ine sindingalipempherere ilo; liyenera kufa, kotero ilo ndi lakufa. Koma ine ndikupempherera Tirigu, Ambuye, amene akuwumbika mu Thupi la Khristu. Perekani, Ambuye, kuti madzi abwino a Mulungu asunge masaya Ake ndi misonzi yachimwemwe ndi kumvetsetsa mpaka chokololeracho

chibwere kuti chidzawutengere Iwo kunyumba. Mu Dzina la Yesu, ine ndikuzipereka izo zonse kwa Inu, Ambuye; zotsatira ndi Zanu. Amen.

[Mlongo apereka uthenga. Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Amen.

³⁴⁵ Koteru Atate Mulungu, ife tikukuthokozani Inu. Ndipo, Atate, ife tikupempherera mlongo wathu wamng'ono, mdzakazi apa, chifukwa cha mphamvu zake. Ine ndikuganiza za nthawi imene ine—ine ndinafika pamaso pake, momwe Mzimu unadzera pa iye ndi kupereka uthenga womwewo umene Mngelo wa Ambuye anapereka pa Mtsinje tsiku lija: “Monga Yohane M’batizi anatumidwa kudzatsogolera kudza koyamba kwa Ambuye Yesu, iwe watumidwa kudzatsogolera kwachiwiri.”

³⁴⁶ Poziwona izo zikuwumbika tsopano mu gawo la tirigu, Mulungu, ife tikukuthokozani Inu pa chirichonse chimene Inu mwachita. Mitima yathu ndi yodzazidwa mosaneneka. Ine ndikumverera kudzazidwa kwambiri, Ambuye, ine basi sindikudziwa momwe ndinganenere china chirichonse. Koma zikomo Inu Atate, kachiwiri, pa zonse zimene Inu mwatichitira ife. Kudzera mu Dzina la Yesu Khristu.

Ndinkonda Iye, . . .

Tiyeni tingoyimbira kwa Iye, tsopano. Kumbukirani, Iye ali pano.

Chifukwa Iye anayamba kundikonda,
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

³⁴⁷ Kodi izo zikukupangitsani inu kumverera wamng'ono kwenikweni, wamng'ono kwenikweni? Yense wodzikhuthula, wokonzekera Mzimu basi, mwaona.

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,
Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

Usakhumbire chuma cha mdziko chachabe,
Chomwe chimavunda mwamsanga,
Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,
(Palibe chipembedzo, tsopano.)

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

Gwira pa dzanja losasintha la Mulungu!

Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,
Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

³⁴⁸ Ndi angati akuyesetsa kuti achite zimenezo? Kwezani dzanja lanu. Tsopano fikirani kuwoloka pa tebulo apo, ikani manja anu mdzanja la wina ndi mzake, monga *chonchi*, pamodzi. Inu mukhoza kukhala pansu, izo ziri bwino, kapena chirichonse

chimene inu mukufuna kuti muchite. Mvetserani mwatcheru. Tiyeni tiyiyimbe iyo limodzi tsopano. Izi zikuyimira unyolo wathu wosaduka wa chikondi cha Mulungu. Tikugwirana manja wina ndi mzake chifukwa ife timakhulupirira mwa Mulungu. Ife timagwirana wina ndi mzake chifukwa ndife abale ndi alongo, Mzimu wogunda womwewo, Mawu Amuyaya a Mulungu akukhala m'mitima yathu akuwonetseredwa.

Pamene ulendo wathu udzatha,
Ngati kwa Mulungu takhala owona,
Kokongola ndi kowala kunyumba kwathu mu
Ulemerero,
Moyo wathu wokwatulidwa udzakuwona!

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,
Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
(Mzimu wa Ambuye!)

Gwira kwa Mulungu . . .

Ingoyikani malingaliro anu pa Iye, mwaona. Uwu ndi mtundu wa misonkhano yomwe ife tiyenera kukhalamo mtsogolomu.

. . . dzanja losasintha!

Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,

Mawu ndi chinthu chokhacho chomwe chiri Chamuyaya.

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

Usakhumbire zachabe za dziko lino . . .

(Kutchuka, maphunziro.)

Zimene zimavunda mofulumira kwambiri,
(Tayang'anani pa izo lero, zomwe
zachitidwa.)

Ufunitsitse kupeza chuma Chakumwamba,
Izo sizidzatha konse!

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!


³⁴⁹ [Mlongo ayankhula mu lirime lina, mlongo wina akupereka kutanthauzira—Mkonzi.] Momwe ife tikukuthokozerani Inu, Ambuye. Pamene ife tikukhala mu mphindi yolemekezeka iyi, pafupifupi ngati maliro, pakuti tayang'anizana ndi kuyikidwa mmanda kwa lakufa, dziko lakufa; wakufa, mpingo wakufa.

O Mulungu, sonkhanitsani tirigu Wanu mwamsanga, Atate. Idzani msanga, Ambuye Yesu.

³⁵⁰ Dalitsani anthu Anu, Atate, bweretsani kuwonamtima ndi kuya ku mitima ya anthu. Mulole ife tichoke ku mavinidwe

oweyeseka osalimba awo, tikhazikike pansu mu chuma chakuya cha uchi wa Mulungu. Perekani izi, Ambuye. Sungani mitima yathu ikhazikike ndi chikondi ndi kuwonamtima.

³⁵¹ Dalitsani anthu Anu kulikonse, Atate. Pamene ife tikuchoka malo ano mulole ife tipite mu Dzina la Ambuye Yesu kuti tikayankhule icho chimene chiri chowonamtima, icho chimene chiri Choonadi, icho chimene chiri cholondola, mulole ife tipewe icho chimene chiri cholakwika, Ambuye. Pamene munthu ayamba kutinamiza ife, mulole ife titembenezire msana wathu kwa iye mwamsanga, titembenezire msana wathu kuchoka ku zoyipa zonse, nthabwala zonyansa ndi zinthu za mdziko, ndi kungotembenezira msana wathu ndi kuchokapo. Tithandizeni ife, wokondedwa Mulungu. Tiwumbeni ife, tipangeni ife, tiphwanyeni ife, ndipo mutipange ife kukhala zifanizo za ana aamuna ndi aakazi a Mulungu kuti ife tikakhoze kuchita ndi ukoma wa Mzimu Woyera. Ife tikudzipereka tokha kwa Inu, ndi manja athu mwa wina ndi mzake, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Tiyeni tiyime. M'bale Nolan. 

65-1127B Kuyesera Kuti Umuchitire Mulungu Ntchito
Popanda Icho Kukhala Chifuniro Cha Mulungu
Washington Youree Hotel
Shreveport, Louisiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org